


CHILUMIKIZO CHOSAWONEKA CHA MKWATIBWI WA KHRISTU

 Ine ndachotsa ulendo wa kokasaka, kuti ndikhale ndi utumiki kwa Ambuye. Kotero ziri...Ndife okondwa kuti tiri pano. Ine ndikukhulupirira, nthawi yotsiriza pano, ine ndinakuuzani inu: nthawi iliyonse yomwe ife timabwera, pamakhala winawake akuswapo. Ndipo ngati ife titi tidzabwerere chaka chamawa, Ambuye akachedwa, padzakhala pali winawake akusowa.

² Wina anali wapafupi kwambiri, mbiri kwa ine mu mtima, mzimu. Ameneyo anali M'bale Lyle. Ine nthawizonse ndimakhala nako kulandiridwa, pobwera muno, ndikaima kumbuyo uko ndi kumamvetsera, mowerengera mwa M'bale Jack, ku kuyimba kwachikale kwa anai. Iwo akuimba ku Ulemerero, usikuuno. Chabwino, liripo limodzi la maliwu awo lomwe liri kale Kumeneko, akuwayembekezera ena atatuwo. Ine ndikulingalira ine sindidzalimva ilo kenanso kuno pa dziko lapansi. Koma ndithudi ine ndikuyembekezera kudzalimva ilo kachiwiri, M'bale, Mlongo Moore kuno, mu Dziko ilo komwe iwo ati...ilo silidzazilaritsidwa konse.

³ M'bale Palmer anali wantchito wopambana wa Khristu. Ine ndikukhoza kukumbukira M'bale Jack akundiuzwa ine za—moyo wake wodzipereka kwa Mulungu. Iwo anali ampalamatabwa, palimodzi. Ndipo anati iye ankakhoza kukhala akudya cha—chakudya chake chamasana, ali ndi sangweji yake mdzanja lake, akudya sangweji ndi kumawerenga Baibulo lake. Mwaona? Iye anachita zinthu zina zamphamvu kwambiri, M'bale Palmer anazichita. Iye ndi mpalamatabwa wabwino, bambo wabwino kwa ana ake, banja lokondeka. Iye anawalera onse kuti azitumikira Ambuye. Monga momwe ine ndikudziwira, iwo onse ali opulumutsidwa ndi odzazidwa nao Mzimu Woyera. Ndipo ndicho chothandizira chachikulu kwa bambo aliyense mu masiku ano, anyamata ndi atsikana. Koma, onani, zonse zomwe iye anazichita siziwerengedwera mochuluka kwambiri mpaka potumikira Mulungu, monga iye ankamutumikira Mulungu. Ndipo usikuuno, zomwe iye anachita pano pa dziko lapansi, ntchito zake zabwino, iye wapita ku mphotho yake, kuti akakhale nawo. Mulungu ipumitseni solo ya m'bale wathu.

⁴ Ine ndikudziwa, utali wonse pomwe uyu ali kachisi pano, ndipo i—ine ndikudziwa iye adza...liwu lake lidzakhala likadali pano. Inu mukhoza kumalimva ilo. Mlongo Anna Jeanne n—ndi mlongo wake, poyimba limba ndi piano, momwe iwo

sankachita kudikirira nkomwe. M'bale Palmer ankangoima apa ndipo iye ankangoigwira nyimboyo, nkumapitirira nayo. Iwo ankaigwira iyo. Ndipo ine sindinali. . . Ine ndikuyembekezera kudzamumva iye akutsogolera nyimbo.

⁵ Kwa ana ake; kwa mkazi wake; ndi kwa M'bale Jack, mzake wapachifuwa, iwo akhala ali abwenzi kwa zaka zonse izi; ndi M'bale Brown, Mlongo Brown, kachisi yense inu: Mulungu akudalitseni inu. Ine ndikumusowa iye, nanenso. Mulungu apumitse solo yake yolimbikayo, mpaka ife tidzakomane naye mu mtendere.

Tiyeni ife tiweramitse mutu wathu.

⁶ Atate Akumwamba achisomo, timangoyankhula za wantchito wamkulu uyu, ine ndamusowa iye, usikuuno, iye kundigwedeza manja anga, ndi kumwetulira kwakung'ono kwa makani kuja komwe iye nthawizonse amakhala nako pamene iye ankati, "Ambuye akudalitseni inu, M'bale Branham," pamene ife tinkayenda polowa pakhomo. Ine ndikudziwa kuti iye wabwera ku Nyumba Kwanu, usikuuno. Kotero ine ndikupemphera, Mulungu wokonededwa, kuti Inu mulole zipatso, ntchito zake zomutsatira iye, zikhale zazikulu, zipitirire ndi ana ake, mkazi wake. Ife tikupemphera kuti Inu mumudalitse iye, Ambuye. Inu munati Inu mudzakhala mwamunawo wa "akazi amasiye omwe anali amasiye indedi." Ine ndikumupempherera Mlongo wathu Palmer ndi kwa ana onse. Ine ndikudziwa momwe ndingamverere nawo chisoni onsewo, atataya mzawo ndiponso nditataya adadi anga.

⁷ Kotero, Atate, pamene ife tikadali pano, usikuuno, ife tikupemphera kuti Inu mukonzeketsere mitima yathu, nayonso, kwa ora limenelo. Ife sitikudziwa. Ilo likhoza kubwera modzidzimutsa monga lake lachitira. Ife sitikudziwa liti pomwe ilo liti lidzabwere, koma ife tikudziwa kuti ilo liyenera kubwera. Chotero ife tikupemphera, Mulungu, kuti Inu muufufuze mtima uliwonse umene uli muno, usikuuno. Mulungu, musati muusiye wanga kunja. Ufufuzeni wanga, nawonso, ndipo ndiyeseni ine. Ambuye, ngati pati pakhale choipa chirichonse mwa ife, chichotsenimo icho. Ife tikufuna kuti tizikutumikirani Inu. Ndicho cholinga chathu chathunthu, ndi kuti tizikutumikirani Inu.

⁸ Tsanulirani Mzimu Wanu pa ife, usikuuno, ndi sabata lonse ili. Mudalitse kachisi uyu wa dzina la Life Tabernacle. Mulole iye alandire madalitso athunthu a dzina limenelo ndipo akhale wodzaza ndi Moyo wa Mulungu, sabata ino, kuti apulumutse moyo wotaika uliwonse, kuti amdzaze wokhulupirira aliyense ndi Mzimu Woyera, ndi kukonzanso ziyembekezo zomwe ziri mwa ife, Ambuye, kachiwiri. Ife tikupemphera kuti Inu muchizenso odwala onse ndi osautsika omwe akubwera pakati pathu. Mulole Mzimu Wanu Woyera waukulu ukhale pano,

Ambuye, ndipo muzingochiza. Ndipo mudzoze aliyense kuti akhulupirire. Perekani zinthu izi, Atate.

⁹ Mulungu, mutandithandiza ine tsopano. Ngati izi zindigwera, kugwera pa nthawi yanga kuti ndibweretse Uthenga. Ine ndikupemphera, Mulungu, kuti Inu mungolola gawo la munthu liime ku mbali imodzi. Mulole Mzimu Woyera ubweremo ndipo usunthire pa ife, Ambuye. Mulole Mzimu Woyera utenge msonkhanowu, Ambuye. Ife tikudziwa kuti ndife osakwanira kwambiri. Ife sitingakhoze kuzichita izo, palibe wa ife. Ife sitikudzinenera kuti ndife okhoza kuzichita izo. Koma, Ambuye, ife tikudziwa kuti Inu ndinu Mmodziyo. Koteri ife tikuyang'ana kwa Inu, Ambuye. Sunthani, Mzimu wa Mulungu, ndipo gwerani mwatsopano pa ife. Ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

¹⁰ Tsopano ine ndikufuna kuti ndipereke moni uko pa wayayu, kwa mipingo tsopano yomwe yalumikizidwa kudutsa mu dzikoli. Ife tiri pa kulumikiza kwa telefoni, komwe kuli kulumikiza kwabwino kwakung'ono komwe ife takhoza kukupeza, kupyolera mwa M'bale wathu Peary Green wa ku Beaumont, Texas. Ndipo mipingo, kwathunthu, ali kutsatira Uthengawu, ulendo wonse kudutsa mu United States, alumikizidwa, usikuuno. Ife tikutumiza moni, chokwera ndi chotsika Gombe la Kumadzulo, njira yonse kuchokera ku Vancouver mpaka ku Tijuana, Mexico, kudutsa ku San Jose, Los Angeles. Magulu onse cha uko, ife tikukupatsani inu moni kuchokera ku Shreveport. Ndiponso, njira yonse mpaka ku Prescott, Arizona, ku gulu uko komwe lomwe likuyembekezera pa Ambuye, ife tikutumiza moni kwa inu, ndi ku Tucson, ndiponso ku Sierra Vista. Njira yonse mpaka ku New York, kukwera ndi kutsika, kudutsa mu fukoli, Ambuye akudalitseni inu, aliyense. Tikukhumba inu mukadakhala muli pano, usikuuno, dziko lakale lokongola ili la Louisiana, komwe kumawoneka ngati kwathu kwachiwiri, kwa ine. I . . .

¹¹ Inu mukudziwa, anthu inu uko mu New York, inu nonse mumakhala ngati mukuseka kwa inu pang'ono, momwe inu mumayankhulira. Ine ndiri kwathu komwe usikuuno. Eya. Aliyense pansi apa, inu mukudziwa, iwo anati, “Moni, meeko, M'bale Branham. Inu mbwere ni Mlongo Branham ni wana wose ndipo mbwere kuno mudzatipenye ife.” O, mai! Izo zimandipangitsa ine kumverera bwino. Icho ndicho Chichewa chenicheni kwa ine. Sikuti ndikukunyojetsani inu anthu uko kummawa ndi kumpoto, ndi malo osiyana. Koma, inu mukudziwa, ine ndikuganiza ine ndinangobadwa Mchewa wachikale ndipo ine ndiyenera ndizikhala mwanjira yomweyo. I—ine ndimakhala ngati ndimazikonda izo, mwiniwanga. Ndicho Chichewa chenicheni.

¹² Ine ndinali ku kadzutsa wa Amuna Amalonda, kuno si kale litali, ndipo iwo anati, “Ife tsopano tati tiime ndi kuimba nyimbo

ya fuko.” Ndipo ine ndinaimirira apo, nkuti, “Poti kwathu kwakale ku Kentucky, nkutali ndithu.” Chabwino, kwa ine, iyo inali nyimbo ya fuko, nzonse zomwe ine ndinkazidziwa pa izo. Kotero, ife tikukutumizirani inu moni. Tsopano kwa . . .

¹³ Ine ndikukhulupirira iwo ayesera kuti awulutse za kadzutsayo, naponso, kadzutsa wa Amuna Amalonda, Loweruka mmawa. M’bale Green adzakuuze inu, pamene iye ali pa maikolofoni kunja uko tsopano. Kotero iye akuuzani inu nthawi yomwe kadzutsayo ati ayambire, ndi nthawi yake, usiku uliwonse, kuti muzitcherako. Ife tikukuthokozani inu mwachifundo kwambiri. Muzitipempherera ife.

¹⁴ Tsopano, kwa gulu lakomkunoli pano, ndi kachisi wa M’bale Jack, ine ndati ndingokupemphani chifundo chanu, usikuuno. Pokhala kuti ine ndimati ndipereke Uthenga wanga wa kupereka mathokozo kwa—fukoli, usikuuno, kwa mipingo yathu wamba yomwe ikutsatira Uthengawu. Umu, i—ine ndikhoza kutalikitsa pang’ono. Ndiyeno, kachiwiri, ine ndikhoza kulalikirapo Chiphunzitso china. Kotero, ngati ziri choncho, ndipo inu simuli kugwirizana Nacho . . .

¹⁵ Basi monga ine nthawizonse ndimanenera za kudya chitumbuwa cha nthuza, ine ndikaluma njere. Ine sindimataya chitumbuwacho. Ine ndimangotaya njereyo, nkumangopitiriza kudya chitumbuwacho.

¹⁶ Kotero ngati ine ndipezeka kuti ndikutchula chinachake usikuuno, i . . . Chabwino, ndi chifukwa chimodzi chomwe ine ndinatengera kuitanidwa uku, usikuuno, kuti ndidzakhala kuno, kuti ndidzabweretse Uthenga wanga wa kupereka mathokozo kwa magulu a mu dziko lonseli, zinali chifukwa M’bale Jack nthawizonse amatsegula chitseko chake momasuka nkuti, “Lalikirani zomwe ziri pa mtima wanu.” Kotero ine ndikumverera ngati kwathu kwenikweni.

¹⁷ Kotero izi zikhoza kukhala kuti mkati muno, mu gulu wamba la kunoli ndi M’bale Jack, pakhoza kukhala pali atumiki ndi anthu ena omwe akhoza kusagwirizana ndi Chiphunzitsocho. Kawirikawiri ine ndimakhala ndi ulemu wosatchula chiphunzitso pa guwa la munthu, yemwe wandiitana ine kuti ndibwere kudzamuyankhulira iye. Kotero, pambuyo pa usikuuno, ine ndikulingalira ine ndidzakhala ndikungopempherera odwala ndi kumachita utumiki wachizolowezi. Koma ine ndinaganiza kuti ine ndikanakudziwitsani inu zisanafike pochitika, kuti ngati chinachake chimene ine ndingachiyankhule chingakhoze kukhala chiri chosagwirizanika, bwanji, mungozilolera izo ku umbuli wanga, ine ndikulingalira, ndi kusadziwa bwinoko. Ndipo mundipempherera ine.

¹⁸ Kotero tsopano tiyeni ife titembenuze mu Mawu, ku mutu pano. Ine ndikukhumba kuti ndilozere ku malo ambiri usikuuno,

chifukwa ine ndiri nawo Malemba angapo ndi zolembe pang'ono ndazilemba apa pa cholembapo.

¹⁹ Ine ndikukumbukira nthawi yoyamba yomwe ine ndinakwera pa nsanja ku Life Tabernacle, zaka makumi awiri zapitazo. I—ine sindinkasowa kuti ndizichita kulemba Malemba anga ndi zolozeraako. Ine ndinali zaka twente zokha wachichepereko apo. Koma tsopano ine ndadutsa kale twente-faifi, kotero i . . . nthawi yachiwiri. Kotero ine ndiri . . . sindingakhoze kumakumbukira izo monga ine ndinkachitiramo. Ine ndimachita kulemba Malemba anga apa, ndipo nthawizina kulemba mwachidule chinachake chimzake chomwe ine ndikufuna kuti ndilozereko.

²⁰ Ndipo tsopano Ambuye atidalitse pamene ife tiziwerenga kuchokera mu Mawu a Mulungu, ndipo Bukhu la Aroma, mutu wa 7. Tsopano, ine ndikufuna kuti ndikhale ngati ndiphunzitse izi monga phunziro la Sande sukulu.

²¹ Ine ndikuwaona anthu omwe aima. Ndipo ku kachisi, kawirikawiri, ku Jeffersonville, ife tikufuna kuti tikupatseni moni inu nonse, usikuuno, ukonso, tikudziwa kuti inu mwalumikizidwa uko ku kachisi. Ndipo zikuwoneka ngati tiri ku kachisi, usikuuno, ngati inu mukanakhala muli kuno, anthu azungulira makoma, ndipo asefukira. Tsopano, ine ndikulingalira inu muli mwa njira imeneyo, inunso, anthu onse omwe abwera uko mu gawo ilo la dziko, omwe adzera Uthengawu.

²² Tsopano ife tigwiritsa ntchito uwu ngati phunziro la Sande sukulu. Ndipo izo sizikulunjikidwa kwa chirichonse, munthu wina aliyense, kapena chirichonse; kwa Mpingo basi, Thupi la Khristu lomwe ife tikuyesera kuti tilitsogolere ku maganizo okuya ndi zolinga zapamwamba, kukhulupirira kuti Kudza kwa Ambuye Yesu kuli pafupi. Ife tikukhulupirira zimenezo. Mochuluka kwambiri, ndi zaka twente pafupiko kuposa momwe zinaliri nthawi yoyamba yomwe ine ndinabwera ku Shreveport. O, zochuluka kwambiri zachitika kuchokera nthawi ija! Tsopano ife tikuyang'anira Kudza kwa Ambuye, mu kam'badwo kathuka. Ine sindiri kuyang'anira chitsitsimutso mu kam'badwo kathuka. Ine ndikuyang'anira Kudza kwa Ambuye, mu kam'badwo kathuka.

²³ Tsopano mu Aroma 7. Ndikudalira kuti inu muli ndi Mabaibulo anu otsegulidwa, kulikonse tsopano, ku dziko lonseli. Ife tikufuna kuti tiwerenge mwacheru tsopano. U—Uthenga uwu wochokera apawu, iwo ukuwoneka ngati uli pa chikwati ndi chilekano, koma iwo suli kwenikweni. Kwa ine, iwo ndi uneneri kwa Mpingo mu tsiku lotsirizali. Tiyeni ife tiwerenge.

Kodi inu simukudziwa, abale, (pakuti ine ndikuyankhula kwa iwo omwe amadziwa lamulo,)

momwe kuti lamulolo limachita ulamuliro pa munthu utali wonse pamene iye alimoyo?

Pakuti mkazi yemwe ali ndi mwamuna ali womangidwa mwa lamulo kwa mwamuna wake utali wonse pamene iye alimoyo; koma ngati mwamunakeyo akhala atafa, iye ali womasulidwa ku lamulo la mwamuna wakeyo.

Koterono ndiye ngati, pamene mwamuna wakeyo alimoyo, iye akwatiwa ndi mwamuna wina, iye adzatchedwa wachigololo: koma ngati mwamuna wake akhala atafa, iye ali womasulidwa ku lamulo limenelo; kotero kuti iye salinso wachigololo, ngakhale iye atati akwatiwe kwa mwamuna wina.

Chotero, abale anga, inunso mwakhala okufa ku lamulo mwa thupi la Khristu; kuti inu mukakhale muli olumikizidwa kapena mukhale mutakwatiwa kwa wina, ngakhale kwa iye amene anaukitsidwa kwa okufa, kuti ife tizibalira zipatso kwa Mulungu.

Pakuti pamene ife tinali mu thupi, . . .zilakolako za tchimo, zomwe zinali mwa chilamulo, zinali kugwira ntchito mu ziwalo zathu kuti zizibalira zipatso za ku imfa.

Koma tsopano ife tiri omasulidwa ku chilamulo, kuti pokhala okufa umo momwe ife tinagwidwa; kuti ife tizitumikira mwa utsopano wa mzimu, ndipo osati mwa ukale wa lemba.

24 Ndipo tsopano tiyeni ife tipemphere.

25 Wokonedwa Mulungu, ife tangowerenga zomwe ife tikuzikhulupirira kuti ndi Mawu opatulika a Mulungu. Ndipo ndi chimene ife tikuchikhulupirira, kuti palibe kolembedwa kamodzi kapena neno limodzi liti lidzachoke mwa njira iliyonse kwa Awa mpaka zonse zitakwaniritsidwa. Ndipo ife tikukhulupirira kuti Ambuye wathu anatiuza ife, mu Chivumbulutso mutu wa 22, kuti, “Aliyense yemwe adzachotsa Mawu amodzi kwa Awa kapena kuwonjezera amodzi kwa Iwo, mofanana, gawo lake, lidzachotsedwa kuchokera ku Bukhu la Moyo.”

26 Ndipo ife tikuziwona izo, mwa kuperekedwa molakwika kwa Mawu awa, monga Satana anawaperekera Iwo molakwika kwa Eva, namupangitsa iye kuti akaikire Mawu amodzi, zinauponyera mtundu wonse wa anthu mu chisokonezeko chokugwa. Mawu amodzi okha!

27 Ndiye ife tikuwona pakati pa Bukhu, anadza Ambuye wathu ndi Mpulumutsi, ndipo Iye anatipatsa ife chobwerezedwa ichi chokhudza Iwo. “Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha,

koma ndi Mawu onse omwe atuluka kuchokera mkamwa ya Mulungu.”

²⁸ Ndiye chenjezo losamalitsa mu Bukhu lotsiriza, la Chivumbulutso cha Yesu Khristu, “Aliyense yemwe ati adzawonjezere mawu kapena kuchotsapo Mawu, gawo lake lidzachotsedwa ku Bukhu la Moyo.”

²⁹ O Mulungu, podziwa, powona momwe ife tiriri osalimba, podziwa kuti ife tikuyenda pa ulusi wosalimba wa moyo, wa moyo wachivundi uno, posadziwa nthawi yomwe ife titi tiitanidwe kuti tikayankhe Mmwamba umo. Mutilole ife, O Ambuye, tiyike kumbali chirichonse cha mu mtima mwathu, chirichonse cha mmalingaliro mwathu, ndi kuyang’ana molunjika ku Mawu Anu, usikuuno, ndi kuti Inu mubwere ndi kudzawatanthauzira Iwo ndi mayankhulidwe amoyo. Perekani izi.

³⁰ Mulole Mzimu Wanu ugwere pa ife ndipo uwadzozere Mawuwa ku mtima wathu, kuti tikhoze kupita kuchokera kuno, usiku uno, anthu abwinoko kuposa momwe ife tiriri pano, kuti ife tikhoze kukhala nako kuyang’anitsitsa kwa pafupi pa Yesu Khristu. Perekani izi, Ambuye, kuti ife tikhoze kumalimvetisa tsiku lomwe ife tiri nkukhalamoli, ndi kukonzeketsera kwa Mulungu kwa anthu Ake mu ora lino; nthawi iyi, yaikulu, yovuta, ya mdima yomwe ife tiri kukhalamo tsopano. Mulungu, adzozeni iwo, osati kokha woyankhula, koma omvetsera. Ndipo, palimodzi, mupange mitima yathu kuti injenjemere nao Mawu Anu. “Pakuti kuwopa Mulungu ndicho chiyambi cha nzeru.” Perekani zinthu izi, Atate, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

³¹ Ine ndikufuna kuti nditche ndemanga pang’ono izi zomwe ine ndikuti ndizipange pano, ndi Malemba ena omwe ine ndikanafuna kuti ndiwatsatire mwacheru mmbuyomo, ngati Ambuye alola, ku—Uthenga wa kupereka mathokozo, kwa wosawoneka, wa: *Chilumikizo Chosawoneka Cha Mkwatibwi Wa Khristu. Chilumikizo Chosawoneka Cha Mkwatibwi Wa Khristu*. Iwo sukumveka ngati Uthenga wa kupereka mathokozo. Ngakhale, Lemba lililonse, ndife othokoza chifukwa cha onse a Iwo.

³² Ine ndiri wothokoza kwambiri kwa Mulungu, kuti ndiri moyo mu nthawi ino, ya zochitika zotsekera mbiriyakale ya dziko iyi. Ine sindikudziwa. Ngati ine ndikanati ndikhale ndi chonena asanaikidwe maziko a dziko, ndipo Mulungu akanaliika dongosolo lonse kwa ine, ndipo akanati kwa ine, “I—ine ndikufuna kuti iwe uzilalikira. Ndipo tsopano ndi m’badwo uti womwe iwe ukukhumba, kuti upite ku dziko lapansi kuti uzikalalikira?” Ine ndikanasankha m’badwo uno, chifukwa ine ndikuganiza uno ndi m’badwo wagolide.

³³ Ine ndithudi ndikanakonda kukhala ndiri kuno pa nthawi ya kudzachezera Kwake ku dziko lapansi. Koma, apabe, ine ndikuganiza ino pakali pano ndiyo nthawi yaikulupo, chifukwa ndi nthawi yomwe Iye akubwera kuti adzatenge anthu omwe Iye anawaombola, kuyandikira chiukitsiro pamene owomboledwa onse ati adzatulukire. Ndi mwayi wauemerero bwanji womwe ife tiri nawo, kuti tikuyankhula kwa anthu amene akufa, nthawi yaikulu! Ife tatengeka nayo.

³⁴ Ndipo ife tikudziwa kuti mbiriyakale ikutsekeredwa. Mbiriyakale ya dziko posachedwapa itha, ndiye ife tidzakalowa mu tsiku latsopano, kupita mu Zakachikwi zopambana. Kutu, munga wokhulupirira mmodzi, ine ndikukhulupirira mu . . . mu Zakachikwi, kulamulira kwamu Zakachikwi ndi Khristu, zaka chikwi pa dziko lapansi; kubwerera mwathupi kwa Ambuye Yesu, kuti adzatenge anthu mwathupi, aulemerero, mwa Magazi Ake oyeretsa.

³⁵ Paulo pano akupereka kulongosola, mu Lemba lathu, pa za lamulo ndi chisomo, ndipo akulongosola izo munga chikwati ndi chilekano. Gawo ili silimalalikiidwa kawirikawiri kwambiri, chifukwa ilo, mochuluka kapena mwapang’ono, limafanizidwa ndi, munga, chikwati ndi chilekano. Koma ilo limafanizidwanso ndi gawo lalikulupo la chikwati ndi chilekano, la momwe iye akuyesera kuti aike mu dongosolo apa kuti ife, mo—munga Mpingo, sitingakhosenso kukhala okwatiwa kwa dziko ndi kwa Khristu, pa nthawi yomweyo, n—ndi kukhala ovomerezeka ndi mwamalamulo nazo, kuposa momwe izo zingakhoze kukhalira kwa mkazi kuti azikhala ndi mwamuna pamene iye ali ndi mwamunake wamoyo. Ndipo ine ndiri nalo lingaliro langa langa pa izo, ndipo ine ndikukhulupirira kuti zomwe Baibulo limanena ndizo Choonadi.

³⁶ Tsopano, koma ine ndikukhulupirira, naponso, ndi mwa kukhulupirira kwanga, kuti ilo likufunyulula chimodzi cha zinsinsi zazikulu za uneneri. Ndipo ine ndikuyembekeza kuti Ambuye atithandiza ife, usikuuno, pamene ife tikupereka izi kwa anthu athu oyembekeza ku dziko lonseli.

³⁷ Izi zinanenedwa, nthawi ina. Ine ndinali kuwerenga, pamene ine ndinali kulemba zolemba za izi, i—ine sindingakhoze kulikumbukira kwenikweni bukhu lomwe izo zirimo. Koma i—ine ndikutsimikiza uku ndi kulondola, kuti, limodzi la mabuku omwe ine ndinawawerenga linali la Bambo Moody, Dwight Moody, ku Chicago. Ife tiri ndi mpingo waukulu ukumvetsera ku Chicago, nakonso, usikuuno. Kutu, Bambo Moody, atatha kuwerenga Aroma 7, anathamangira ku msewu, ndipo munthu woyamba yemwe iye anakomana naye, iye anati kwa iye, “Kodi iwe ukumudziwa chisomo?”

Ndipo bamboyo anayankha, “Chisomo ndani?”

Bambo Moody anati, “Chisomo cha Mulungu.”

38 Kotero, izo zinamukondoweza iye kwambiri pamene iye anawona zomwe, momwe chisomo chinali chitatilekanitsa ife kwa lamulo, ndi momwe, gawo lomwe chisomo chinasewera. Chabwino, tsopano, chirichonse chomwe ine ndikufuna kuti ndichite, ndi pamene. . . Ine nthawizonse ndimawauza anthu, pamene ine ndidzaloza mzere, kumbali inayo, ine ndikanafuna kuti ndidzaima ndi kuimba.

Chisomo chodabwitsa! Kukoma kwake
pochimva,
Chomwe chinapulumsa wopandapake
monga ine!
Chisomo, chisomo chofunika!
Zambiri za chisomo kuti ndizidziwe!

39 “Pakuti ndi mwa chisomo kuti ife tinapulumsidwa; osati ndi zomwe ife tingakhoze kuzichita.” Zomwe ife tingakhoze, chirichonse chomwe ife tichichita, icho sichimawerengedwera kwa ife. Chisomo ndi chimene chimatipulumutsa ife. “Mwa chisomo inu munapulumsidwa, kudzera mchikhulupiriro.”

40 Mulole ine ndiwonjezere kwa Mkazi uyu, Chisomo. Mundilole ine ndimukhazikitse Iye mu Baibulo, umonso, iye amatchedwa Dona wosankhidwa, Abiti Chisomo uyu yemwe ine ndikuti ndikambe za iye. Mukudziwa, Baibulo limanena, linati, “Kwa Dona wosankhidwa.” Kutu, ngati inu mungazindikire, “kusankhidwa” kumachokera ku mawu “Dona wosankhidwa.” Dona Mmodzi, pakati pa madona ena onse, anasankhidwa.

41 Monga, namwali anali woti adzalibale thupi la Mulungu, pa dziko lapansi. Iye anali mkazi wosankhidwa. Mulungu anamusankha Maria.

42 Ndipo, aponso, Mulungu wamusankha Dona wosankhidwa, yemwe ali Mkwatibwi Wake. Iye ndi wosankhidwa. Ine ndikuyembekeza ndife ziwalo za iye, usikuuno, ku dziko lonseli, ku fuko lonseli, kani.

43 Kulongosolaku pano, kukusonyeza ubale wa Mkwatibwi kwa Khristu, Dona wosankhidwa: ndi momwe Iye anali woti abweretsedwe kwa Iye; komwe Iye akanakhala atachokerako; ndi momwe Iye akanati adzabweretsedwere kwa Iye. Mpingo apa, mu kulongosola komwe ife tiri nako poonekeraku, ukulongosoledwa ndi mkazi. Chomwe, mkazi nthawizonse ali choimira cha Mpingo, chifukwa Mpingo umatengedwa ngati Mkwatibwi. Mkwatibwi, Iye ndi Mkwatibwi wa Ambuye Yesu, Mwana wa Mulungu.

44 Nthawizonse, ngati inu mungapenye, penyani zikhaliidwe ndi kachitidwe ka akazi, ndipo inu muwona pomwe mpingo uli.

45 Tsopano, izi, ndemanga zina izi zikhoza kuwoneka zachilendo kwa ena inu, koma ndi zowonjezera kwa Uthenga umene ine ndiri nawo wochokera kwa Ambuye, umene ine ndikuyesera kuti ndiwufikitse kwa anthu. A. . . Inu muzipenya

chirichonse mwa chibadwa, momwe izo zikuchitikira, chirengedwe, ndipo muchipenye icho. Icho chimayenda moonana ndi zauzimu, nachonso.

⁴⁶ Tsopano, ngati inu mukanati muone kachitidwe ka akazi mu dziko lero, penyani kachitidwe ka mpingo wachidziko lero. Ingopenyani. Ndithudi, tsopano, palinso kachitidwe ka Mkwatibwi wauzimu, Mpingo. Mwaona? Muupenye Uwo, aponso. [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] Chifukwa, wachilengedwewo, wongotchedwa kuti ali Mkwatibwi.

⁴⁷ Tsopano, chonde ndiloleni ine ndinene kachiwiri kwa osonkhana apano. Musati mumverere moipa tsopano. I—ine ndikuyankhula kwa onse ku dziko lonseli, kwa, yemwe ine ndikuganiza, ndi Dona wosankhidwa. Koteru ngati zichitika kuti muli atumiki muno, omwe sakugwirizana nazo, chabwino, ingogwirani mtendere wanu kwa kanthawi pang'ono. Mwaona? Zindikirani. Ingomvetserani.

⁴⁸ Zindikirani khalidwe ili. Pamene inu muwaona akazi akungoyenda mwachisawawa, akungochita zirizonse zomwe iwo akufuna kuti azichita, upenyeni, mpingowo ukuchita chinthu chomwecho. Zindikirani.

⁴⁹ Koma penyani pamene, Mkwatibwi wauzimu, pamene Iye ayamba kukhala ndi chitsitsimutso, pamene Iye akuyamba kubwerera ndi kudzifoletsa Yekha ndi Mawu a Mulungu. Mpenyani apo kachiwiri, inu mukuona, momwe kuti Malemba, pa nthawi imeneyo, Pakhala pali Uthenga ukusesera kunja kuti umugwire Mkwatibwi ameneyo, umugwire Mkazi uyo, Wosankhidwayo.

⁵⁰ Pakuti, monga dziko, Satana, wonyengayo yemwe anamunyenga mkwatibwi woyamba, pa kumuchimwira Mulungu, pa kusawakhulupirira Mawu Ake.

⁵¹ Ndipo tsopano, lero, pamene ife tikuwuona mpingo wachilengedwe, mu uthenga waluntha, ukupita motalikira talikira ndi Mawu, mu uthenga wachisangalatso; ife tikupeza kuti akazi a mdziko, pa misewu, mamembala a yoteroyo, akudzinyamulira okha mu chikhalidwe chomwecho. Inu simungakhoze kuwauza iwo. Iwo ataya kumverera konse kwa khalidwe wamba, anthuwo atero. Mwaona? Ndipo umo ndi momwe mpingo wachitira. Ndipo inu mukhoza kuziwona izo zikupita molunjika ku ecumenical council, motsimikiza basi monga chirichonse mu dziko, ndi mpaka kukalowa mu Roma molimbikira momwe iwo ungakhoze kupitira, mwaona, chifukwa izo zinaloseredwa. Ndipo ndi uyo apo. Ilo ndilo khalidwe lake.

⁵² Komano penyani kachiwiri kwa Mpingo wauzimu, momwe gulu ilo la anthu, loitanidwa lituluke, Osankhidwa, kudutsa mu chitsitsimutso chirichonse. Mwa Marteni Lutera, izo zinachitika mwanjira yofanana mu kukonzanso. Chinachitika chinthu

chofanana mu nthawi ya John Wesile. Chinachitika chinthu chofanana pamene Chipentekoste chinkayamba koyamba. Iwo anawagwetsera akazi amenewo kubwerera kumene mu mzere ndi Mawu, ndiyeno iwo akulowerera kutali. Apo iye akupita akubwerera kumene uko mu chisokonezeko. Komano nthawi yomwe anthu ali okonzekera kuti adzifoletse, pamakhala Uthenga umene umabwerapo, ndipo iwo amadzifoletsa limodzi Nawo.

⁵³ Lutera anali mtumiki wa tsiku lina, wa kulungamitsidwa, ndipo Mpingo unadzifoletsa kumene ndi icho, ena a iwo. Ena onsewo anapitirira nazobe. Wesile anabwera ndi kuyeretsewa, Mpingo unadzifoletsa limodzi ndi izo. Chipentekoste chinabwera ndi kubwezeretsa kwa mphatso, Mpingo unadzifoletsa limodzi ndi izo, Osankhidwa a tsiku limenelo; ndiyeno wazirara nutha; anabwera kumene mu zachipembedzo ndipo anapita kunja komwe limodzi ndi ena onsewo, onse awo chotsika nazo kutsatira mzerewo.

⁵⁴ Tsopano, koma inu mukuzindikira, pamene anthu ayamba kuyesera kudzifoletsa ndi Mawu, apo pamadza Uthenga watsopano wochokera ku Mawu a Mulungu, molunjika kumene kwa anthuwo. Ndipo iwo amaugwira Uthenga umenewo ndipo amadzifoletsa apo, nthawi iliyonse. Izo ziri basi mwa Mulungu. . . Ife tiri nazo izo.

⁵⁵ Ife tiri nawo mabanja. Banja lirilonse mkati muno likuzidziwa izo. Nthawizina chirichonse chikhoza kumakuyendera bwino iwe, kwa zaka. Ndiye, zonse iwe mwakamodzi, iwe umagundana ndi chilala pamene, ife timanena izo nthawi zambiri Kummwera kuno, “Pamene iyo ivumba, iyo imakhuthuka,” ndipo chirichonse chimayenda molakwika. Inu mukudutsa mu nthawi yausiku. Ndiye pali kutulukira kwa tsiku, kenako nthawi ya usiku. Chirichonse chimayenda mogwirizana.

⁵⁶ Mneneri, Paulo, apa akunena kuti mkazi sangakhoze kukwatiwanso mpaka mwamuna wake woyamba atafa. Iye sangakhoze kukwatiwanso utali wonse pamene mwamuna wake woyamba ali moyo; iye, si mwanjira iliyonse, konse. Iye ayenera kuti azikhala mbeta utali wonse pamene mwamuna wake woyamba alimoyo. Ndipo ngati iye angachite tchimo loterolo, “iye azitchedwa wachigololo.” Ine ndikuyankhula za chilengedwe tsopano, kuti ndifanizitse izo ndi zauzimu. Ngati mkazi uyu angati achite tchimo loterolo, ndiye iye amaikidwa chizindikiro, “wachigololo,” ngati iye ali ndi amuna awiri amoyo pa nthawi yomweyo. Chotero, iye wapinyolitsa, pa kuchita izi, mafulu ake kwa Mulungu ndi Kumwamba, pa kuchita choncho. Iye ndithudi watero. Iye ndi wotayidwa kunja kwa chuma cha Mulungu, malingana ndi Malemba omwe ine ndangowawerenga awa.

⁵⁷ Chomwecho uli mpingo, pamene iwo uyesera kusakaniza kachikhulupiriro ndi chipembedzo ndi Mawu a Mulungu. Iye sangakhoze kukwatiwa ndi chipembedzo, ndi kukhala Mkwatibwi wa Khristu, pa nthawi yomweyo. Iye ayenera kuti afe kwa mmodzi kapena mzakeyo. Lamulo likunena chomwecho, apa. Muli malamulo ambiri mu Mawu a Mulungu. Ndipo ilo ndi Lamulo Lake, Paulo akuyankhula chinthu chomwecho pano. Iye sangakhoze kukhala atakwatiwa kwa Mpingo wa kachikhulupiriro kazachidziko, ndi kukhala Mkwatibwi wa Khristu, chifukwa (iye) winayo ndi wosiyana ndi mzakeyo. Tsopano, kumbukirani.

Mukuti, “Chabwino, ife timakhulupirira *izi*, koma ife sitimakhulupirira *Izo*.”

⁵⁸ Ngati inu mwakwatiwa kwa Khristu, Khristu ndi Mawu a Mulungu. Mu Yohane Woyera, mutu wa 1, anati, “Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu. Ndipo omwewo anapangidwa thupi ndipo anadzakhala pakati pathu.” Khristu anali Mawu amoyo. Iye nthawizonse anali Mawu. Iye akadali Mawu. Iye nthawizonse adzakhala ali Mawu. Iye anali kuwonetsera kokhako kwa zikhumbo za Mulungu, pakuti Iye anali Mwana wa Mulungu.

⁵⁹ Ndipo mwana aliyense ali chikhumbo cha abambo ake, ndipo monga inu munali mu majini a abambo anu, mu thupi la abambo anu pamene iwo anali mnyamata wamng’ono. Inu munali mwa iwo. Komabe, iwo sakanakhoza kuti akhale nacho chijanano ndi inu, chifukwa iwo sanali kukudziwani inu. Komano, kupyolera mu nthaka yobalirapo ya amayi, inu munabweretsedwa mu dziko lapansi ndipo munadzakhala mu chifanizo cha abambo anu, ndiye iwo akhoza kuchita chijanano ndi inu.

⁶⁰ Ndipo chomwechonso inu munali, ana aamuna ndi aakazi a Mulungu, pasanakhale ngakhale mwezi, nyenyezi, kapena molekyulu. Inu munali ana aamuna ndi aakazi a Mulungu, pakuti inu muli mawonetseredwe a thupi chabe a zikhumbo zomwe zinali mwa Mulungu pachiyambipo. Pakuti pali mtundu umodzi wokha wa Moyo Wamuyaya, ndipo uwo unali inu, asanati. Inu simukudziwa kanthu za izo. Ngakhalenso inu simunkadziwa pamene inu munali mwa atate anu apadziko, koma inu mwawonetsedwera, inunso, mu chifanizo chake. Mu chifanizo cha Mulungu inu mwapangidwa, ndipo inu munawonetsedwera kwa ulemerero ndi chijanano cha Mulungu.

⁶¹ Ndipo, kotero, motsimikiza monga jini yanu inkayenera kuti ikhale ili mwa abambo anu, kubadwa kwanu kwachilengedwe kusanachitike, nyongolosi yanu yauzimu inkayenera kukhala ili mwa Mulungu, chifukwa ndinu kufotokozera kwa zikhumbo za maganizo Ake, asanaikidwe maziko a dziko. Kulondola. Palibe

njira yochizungulirira icho. Ndiko kulondola. Tsopano, tsopano ife tikuzindikira, ndiye, Moyo uwo pokhala uli mwa inu, Moyo wa Mulungu pokhala uli mwa inu, kuyambira ku maziko a dziko.

⁶² Tsopano, tsopano, inu simungakhoze kusakaniza kachikhulupiriro ka chipembedzo ndi Mawu, chifukwa izo ndi zosiyana kwambiri, china kwa chimzake.

⁶³ Ndizo ndendende zomwe Satana anayesera kuti achite ndi lingaliro lake laluntha kwa Eva. Iye anati iye anavomereza kuti Mulungu ananena izo, koma iye anati, “Ndithudi, inu simudzafa ayi.” Mwaona? Ndipo iwo anazikhulupirira izo.

⁶⁴ Ndipo ndi zomwe tizikhulupiriro tachita, usikuuno. Chipembedzo chawalekanitsa anthu ku Mawu a Mulungu. Kodi Yesu sanati, pamene Iye anabwera, “Inu, kupyolera mu mwambo wanu, mwawapanga Malamulo a Mulungu kukhala opanda mphamvu kwa anthu”? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndipo kupyolera mu kachikhulupiriro kathu, ife tathetsa chiyanjano cha Mzimu Woyera kuti uziwadzoza Mawu a Mulungu omwe akonzedwera mu kam’badwo kano. Ife tawalekanitsa anthu, ndi chipembedzo, moti iwo sangakhoze kukhala nawo mwayi woti awaone Iwo.

⁶⁵ Tsopano, Mulungu, Iye, kam’badwo kalikonse, Iye amawonjezerapo gawo latsopano la Bukhu lake. Izo zonse zimayendera limodzi.

⁶⁶ Monga thupi langa linamangidwira. Ine ndimauidwa kuti zinayambira mu nsana, koma silinali lonse nsana. Ilo linapita kuchokera apo kupita ku nthiti, ndipo kuchokera ku mapapu, ndi ku manja, ndi mikono, ndi mapazi, ndi zina zotero, ndipo izo zinabwerabe mpaka kudzakhala munthu yemwe ine ndiri.

⁶⁷ Ndipo chomwechonso Mulungu anawonetseredwa pachiyambi. Ndipo potsiriza Iye anawonekera ngati Yehova, Mulungu Atate. Ndiye Iye anadzawonekera ngati Mulungu Mwana, mwa Yesu Khristu. Tsopano Iye waonekera ngati Mulungu Mzimu Woyera. Mulungu yemweyo, nthawi zonsezo, mawonetseredwe atatu a yemweyo—Mulungu yemweyo.

⁶⁸ Tsopano, ife tikupeza mkati umu, kuti, kam’badwo kalikonse, Mulungu anali ataikamo Mawu Ake kuchokera pachiyambi.

⁶⁹ Monga momwe kusintha kunadzera. Monga momwe chinthu choyamba chimene Mulungu anachilenga, mwinamwake chinali . . . Tiyeni titi Iye analenga moyo wa zomera, choyamba. Kenako Iye analenga moyo wa zinyama, motsatira. Ndiye Iye analenga moyo wa umunthu, kenako. Kukhala ngati kusintha, kukwera mmwamba.

⁷⁰ Chotero izo zinkayenera kukhala ziri mwa Mulungu ndi Mpingo Wake. Kulungamitsidwa pansu pa Lutera. Kuye- . . . Ndiko kumukokera Mkwatibwi Wake kunja apo, tsopano. Iye

akulenga Mkwatibwi Wake. Kulungamitsidwa pansu pa Lutera; kuyeretsedwa pansu pa Wesile; ndi zina zotero, inu mukuona. Iye, kusintha kwa Mzimu kuli kuperekedwa mochulukira mochulukira, chifukwa Thupi likuwumbidwa, likubwera ku Mutu, womwe uli Khristu, Thupi la Khristu.

⁷¹ Tsopano, Iye, monga mkazi, ngati Iye wakwatiwa ndi Khristu Mawu, Iye sangakhoze kukwatiwa ndi mpingo wachipembedzo pa nthawi yomweyo, pakuti Iye ali womangidwa ndi icho. Iye adza... sangakhoze kumakhala ndi amuna awiri onsewo pa nthawi yomweyo. Iwo ndi osiyana, wina kwa mzake. Mmodziyo ndi wotumidwa ndi Mulungu, winayo ndi wopangidwa ndi anthu, kotero iwo ndi osiyana. Anati, “Mulole mawu a munthu aliyense akhale bodza; Anga akhale Choonadi.” Mulungu ananena izo.

⁷² Osiyana mochuluka basi wina ndi mzakeyo, momwe lamulo linaliri kwa chisomo, monga Paulo akuyankhulira apa. Mmodzi ayenera kuti afe, kuti akhale ndi winayo. “Ndipo ngati iye ayesera kuti awasakanize iwo, iye azitchedwa wachigololo.” O! Taganizani za izo. New York, Arizona, ku fuko lonseli, taganizani za izi. Mulungu anati, “Ngati iye ayesera kuti akwatiwe ndi awiri pa nthawi yomweyo, iye azitchedwa wachigololo.” Ndi wachigololo uti angakhoze kukalowa Kumwamba? Kodi Mulungu angakwatire wachigololo? Ndithudi ayi. Iye anatipempha ife kuti tisamachite izo. “Iye adzatchedwa wachigololo.”

⁷³ Ndiye, ana ake, ngati iye ali wachigololo, ana ake ndi apathengo. Apathengo! Apathengo kwa chiani? Osati kwa mpingo, koma ku Mawu. Iye ndi wapathengo. Chithunzi chake cha Chivumbulutso 3 uyu pano, cha tsiku lotsiriza, m’badwo wa mpingo wa Laodikaya! Gulu lapathengo lakelo! Kusokonezeka kwa chipembedzo kwakeko! Ofunda, kumapitiriza ndi kumadzitcha okha Akhristu, ndi kumawakana Mawu a Mulungu, “Okhala nawo mawonekedwe aumulungu, koma kumaikana mphamvu yakeyo,” monga mneneri anati iwo akanadzakhala ali.

⁷⁴ Chikwati ndi chikhazikitso chakale kwambiri mu dziko. Chikwati chinachitidwa koyamba, ndipo chinadzakhazikitsidwa, mmunda wa Edeni.

⁷⁵ Mkazi ali wodalaridwa ndi makhalidwe enaake omwe iye samayenera kuti aziwaipitsa. Mkazi ndi wodalaridwa kwa izo. Palibe cholengedwa pa dziko lapansi chonga mkazi. Palibe galu wamkazi, palibe chachikazi cha mtundu uliwonse, chodalaridwa ndi khalidwe lomwe mkazi ali.

⁷⁶ Mkazi sanali nkomwe mu—pachiyambi pa chilengedwe, chifukwa Mulungu ankadziwa kuti iye akanadzagwa. Zazikazi zina zonse sizingakhoze kuchita chigololo. Iye ndi mmodzi yekhayo yemwe angakhoze kuchita chigololo. Ngati iye

akanati apangidwe monga chapachiyambi, icho chikanakhala chonyozetsa ku nzeru yaikulu ya Mulungu. Mukuona? Iye anapangidwa mochokera kwa mwamuna.

⁷⁷ Koma chifukwa iye anaponyedwera ku mbali imeneyo, iye nayenso wapatsidwa ulamuliro wopatulika kuchokera kwa Mulungu, wa chiwombolo. Iye ali ndi makhalidwe omwe iye samayenera kuti aziwawononga.

⁷⁸ Ngati iye awawononga iwo, iye waipitsidwa kwa nthawi ya moyo. Ziribe kanthu kuchuluka kwa momwe wakhululukidwira, iye sangakhoze kulungamitsidwa. Ine ndizikhudza izo mwa pang'ono pokha. Ndiri nalo Lemba pa izo, mu maminiti pang'ono. Iye akhoza kukhululukidwa chifukwa cha kudziyipitsa kwakeko, koma iye sangakhoze kulungamitsidwa mu moyo uno. Izo ziri nthawizonse ndi iye. Zindikirani tsopano. Iye wapatsidwa izi. Iye akhoza kukhululukidwa, koma osati kulungamitsidwa.

⁷⁹ Thupi lake linapatsidwa kwa iye, chidaliro chopatulika chochokera kwa Mulungu. Palibe galu wamkazi, palibe mbalame, palibe nyama ina iliyonse, palibe cholengedwa china chonga iye. Ayi. Ndi Iye yekhayo. Ndi izo, iye ali. . . Chifukwa chomwe izo ziri zopatulika kwambiri, iye ndi woti azibweretsa moyo ku dziko lapansi. Thupi lake ndi nthaka yobalirapo moyo, chotero ndi chifukwa iye anapatsidwa zidaliro zopatulika izi.

⁸⁰ Tsopano apa ndi pamene inu mukhoza kusagwirizana, ambiri, inu afioroje. Ndi chimene chinadetsa mtundu wonse wa anthu, ndi chigololo chija pachiyambipo. Nthaka yake yobalirapoyo inayipitsidwa. Iye anabala mapasa aja, Kaini ndi Abele. Kuchita kumodzi, ana awiri. Fufuzani Malemba. U-nhu.

⁸¹ Zindikirani tsopano. Ife tikupeza kuti thupi lake ndi nthaka yobalirapo, ndipo kotero ndi chidaliro chopatulika, kuti asamachiipitse icho. Tsopano, ine ndikuyankhula tsopano, ndi kubweretsa izi ku kulongosola, kuti ndikusonyezeni inu pamene Mpingo waima. Ine sindiri kuyankhula za inu akazi. Chirichonse chomwe inu muli, izo ziri pakati pa inu ndi Mulungu, kapena inu amuna. Koma ine ndikuyankhula za Mpingo ndi Khristu.

⁸² Tsopano, ichi iye anapatsidwa, kuti azibalitsira moyo umene Mulungu Mwiniwake yekha angakhoze kuwupereka. Mwamuna wake akhoza kukhala yemwe ali ndi nyongolosiyo, koma Mulungu amayenera kuti apereke moyowo. Ndiko kulondola. Iwo uyenera kubwera. Moyo wonse umayenera kuchokera kwa Mulungu. Moyo uliwonse uyenera kuchokera kwa Mulungu. Ukakhala wopotozedwa, ndipo nchomwe chimaupangitsa iwo kukhala wauchimo, koma moyo umayenera kuchokera kwa Mulungu. Iye ndi woyambitsa moyo. Tsopano iye ali ndi zop- . . . chimodzi . . .

⁸³ Ine ndikufuna kuti nditchule zinthu zitatu pano zomwe iye sayenera kuti azichoka kwa izo. Tsopano, ine ndikuyankhula,

muusunge Mpingo mu malingaliro pamene ine ndikuyankhula izi kwa mkazi wachilengedwe, monga Paulo ali apa, mu mutu wa 7 wa Aroma.

⁸⁴ Iye ali ndi chidaliriko chopatulika cha ukoma womwe unaperekedwa kwa iye ndi Ambuye wake, ukoma winawake. Palibe chinanso chiri nao iwo koma mkazi. Kulondola. Iko kunaperekedwa kwa iye ndi Mulungu. Iye samayenera kuti awuyipitse ukoma umenewo.

⁸⁵ Ngati iye achita ngakhale chinachake cholakwika, iye ayenera kuti azikalapa izo kwa mwamuna wake iye asanamutenge iye, ndi kuzikonza izo. Mofanana ndi mpingo womwe unakwatiwa ndi lamulo, uyenera kuti ubwere nawonso pamaso pa Khristu, chisanachitike chikwati chachiwiri. Iye ayenera kuti avomereze izo. Ngati iye satero, ndipo ngati iye akhala ali ndi mwamuna wake kwa zaka khumi ndiyenera nkudzavomereza izo, mwamunayo ali nawo ufulu woti amusiye iye ndi kukakwatira mkazi wina. Ndilo Lemba. Chiwerewere ndi makhalidwe opanda chiyero.

⁸⁶ “Yosefe, usayi uwope, kudzitengera kwa iwe Maria mkazi wako, pakuti icho chimene chikuyembekezedwa mwa iye ndi cha Mzimu Woyera.” Iye ankalingalira zoti amusiye iye mwamseri, mwaona, iye atamutomera kale iye. Pamene iwe umutomera iye, momwe Mulungu zinamukhudzira, iwe wakwatiwa naye iye.

⁸⁷ Zindikirani tsopano. Iye ali nazo zidaliriko zopatulika za ukoma zomwe zaperekedwa kwa iye, zadaliridwira kwa iye ndi Ambuye. Mulungu anamupatsa iye ukoma umenewo. Monga momwe izo zinali mmunda wa Edeni, iye akanakhoza kunena kuti “inde” kapena “ayi.” Iye ali nazo zidaliriko zopatulika za ukazi zomwe zinaperekedwa kwa iye, kuti iye samayenera kuti aziziswa. Ukazi umene ine ndikuwukamba apa ndi kachitidwe kake, khalidwe lake pomwe pali amuna. Osamulola mwamuna aliyense. . .

⁸⁸ Ukayang’ana pa zoonetsera izi ndi kuwaona akatswiri a pa kanema awa akupsyoppsyonana, ndi kumasisitana, ndi kumagwetsana, ndi paliponse, pa akazi awa. Mkazi yemwe amachita izo, ndi wa khalidwe loipa. Iye akhoza kukhala wangwirowi, mwinamwake. Koma, onani, mu mtima mwake. . . Pamene, zofunitsa izo, zofunitsa kugonana, ziri mu milomo. Mwamuna akamupsyoppsyona mkazi, iye ali kwenikweni, mwamtundu wina, wachita chigololo. Zofunitsa kugonana ziri mu milomo ya mkazi ndi mu milomo ya mwamuna. Iye akhoza kumupsyoppsyona iye pa dzanja, izo sizingasakanize zofunitsa kugonana zawo. Koma zofunitsa kugonana ziri mu milomo. Ndipo poona zachabechabe zonse izi mu—Hollywood lero, za kugwetsana konse uku ndi kugonana apo ndi akazi, ndi zina zotero, ndipo asungwana aang’ono akuyang’ana pa izo zonse.

Palibe zodabwitsa makhalidwe athu avunda ndi kuwola, ndi mwanyansi, mwaona, chifukwa izo zikumaikidwa patsogolo pa ana. Ndiko kulondola. Izo ziyenera kumakhala mwanjira imeneyo kwa tsiku lotsirizali.

⁸⁹ Tsopano usungeni mpingo mu malingaliro. Iye akupsyopsonana ndi kumagwetsana, ndi kumasakanizana apo mu china chirichonse kupatula Mawu, kumamulola Mdierekezi, ndi maphunziro ndi kafukufuku wasayansi, ndi zina zotero.

⁹⁰ Pamene, mwasayansi, maphunziro, chirichonse, ziri mwamtheradi mosiyana ndi Mulungu. Kachitidwe konse ka chitukuko komwe ife tiri nako tsopano kali mwamtheradi kotsutsakhristu. Kachitidwe ka maphunziro ndi kotsutsakhristu. Chitukuko ndi chotsutsakhristu. Ndi zotsutsana ndi Mulungu. Inu mukuti, “Ukutsutsa chitukuko?” Mulungu adzakhala nacho chitukuko, limodzi la masiku awa, chomwe sichidzakhala nayo imfa iliyonse yochita nayo kwa icho. Chitukuko chamakono ichi chinabwera ndi Satana. Ine nditsimikizira izo kwa inu, ngati Ambuye alola, usikuuno, kuchokera mu Baibulo. Zinthu zonse izi ndi za Satana. Chitukuko chathu chatsopanocho sichidzakhala nazo zirizonse za izi mu icho.

Iye ali nawo ukazi wopatulika uwu.

⁹¹ Palibe zodabwitsa kuti amuna akumachita pa akazi momwe iwo akuchitiramu, nchifukwa chakuti akazi akumachita kwa amuna momwe iwo akuchitiramu. Iye akudzipatsa makhalidwe kunja uko atavala zazifupi, ndi zomanga-thupi, ndi zovala zachimuna ndi zinthu, uko pa msewu, akudzipotola uko. Ziribe kanthu zomwe iye anena, iye akhoza kukhala wangwiro kwa mwamuna wake momwe iye angakhoze kukhalira, koma, pamaso pa Mulungu, “Iye ndi wachigololo.” “Aliyense yemwe ayang’ana pa mkazi ndi kumukhumbira iye wachita chigololo ndi iye kale mu mtima mwake.” Ndipo iye anadzipereka yekha kuti akhale choncho.

Ndipo ndizo ndendende zomwe mpingo wachita nalo dziko.

⁹² Zindikirani. Zomwe zaperekedwa kwa iye: ukoma wopatulika, ukazi wopatulika, ndipo kenako umayi wopatulika, azimulemekeza mwamuna wake.

⁹³ Tangoyang’anani lero. Mu mizinda ina, mizinda yambiri, iwo amakhala ngakhala ndi maphwando aakulu zomwe amazitcha chiyanjano, mamembala a mpingo, nawonso. Amaika zipewa zawo pansu, ndipo iwo onse amaledzera ndipo amayika makiyi awo mmenemo. Mkazi aliyense amapita ndi kukatola makiyi pa chipewacho, a mwamuna yemwe iye ati akhale naye mapeto a sabata onsewo. Mitundu yonse ya maphwando oterowo! Chomwe, ine ndiri nazo zambiri zoti ndizinene pano, ngati Ambuye alola, ine ndiribe nthawi yoti ndilowe mu izi. Nyansi zoterozo!

⁹⁴ Ndipo mpingo uli woipa mofanana, kulondola, kumachita chigololo ndi chirichonse, ndipo iye analibe ntchito yoti azipita umo. Iye anayenera kuti azikhala ndi Mawu.

⁹⁵ Manyumba ndi abwino. Zipatala ndi zabwino. Zinthu zina zonse izi ndi zabwino. Mapurogramu a maphunziro, izo ndi zabwino. Iye tiyenera kumakhala moyo kuno, tiyenera tiziwerenga, kulemba. Ndi chimodzi cha chumacho.

⁹⁶ Monga, ife sitinkayenera kuti tizivala zovala zirizonse, pachiyambi. Ine ndilalikira pa izo, mtsogolomo sabata ino, Ambuye akalola. Koma ife tiyenera kuti tizivala zovala chifukwa Mulungu anatipatsa ife zovala. Koma, pachiyambi, ife sitinkazisowa izo. Ife tinali ophimbidwa.

⁹⁷ Tsopano iye waphimbidwa kwa tchimo lake. Iye sakudziwa nkomwe kuti iye akuchimwa, mwaona, momwe iye analiri apo. Mwa. . . Tsopano iye waphimbidwa ndi Mdierekezi; apo iye anali ataphimbidwa ndi Mulungu. Kusiyana kwa izo.

⁹⁸ Tsopano ife tikupeza kuti iye wapatsidwa chidaliriko chopatulika ichi chomwe iye samayenera kuti azichiswa: la ukazi, kachitidwe, azikhala ndi khalidwe lake, azilera ana ake, azikhala wolemekezeka kwa mwamuna wake.

⁹⁹ Masiku ano, iwo akupereka chidwi chochuluka pang'ono kwa izo kuposa chirichonse mu dziko. Inu mukanati mudzakhale mu ofesi yanga nthawi ina ndi kuwaona amuna akubweretsa akazi awo, pamene iwo akuyesa kukhala mwabwino ndi Mulungu ndi kuvomereza za amuna onse omwe iwo amakhala nawo, ndi chirichonsecho, kuyambira pomwe iwo anakwatirana. O, inu mukuti, “Ndiko. . .” Ayi. Awo ndi Achipentekoste. U-nhu. Enawo sangabwere. Kotero ziri. . .

¹⁰⁰ Ine ndikuyankhula za momwe izo zingakhoze kuchokerapo, pamene inu mufika posakanizikana ndi dziko, mpingo, ndi mafashoni onse ndi zinthu zomwe ife tiri nazo. Ife sitiri mochulukiranso monga chipentekoste chapachiyambi chinali kuposa momwe usana uliri kwa usiku. Ife talowerera kutali kwinakwake, mu chisokonezeko cha mdima china kwinakwake, ndipo tatayika.

¹⁰¹ Chidaliriko chopatulika chakecho! Udindo wake kwa mkaziyo! Tsopano taonani chifukwa chomwe iye ali choimira cha Mpingo, womwe uli nawo udindo womwewo. Monga mkazi ali nawo udindo wopatulika kwa umayi wake, kwa ukoma wake, kwa mwamuna wake, Mpingo uli ndi udindo wopatulika kwa pemphero ndi kwa Mawu, ndi kwa Khristu, mofanana basi monga mkazi aliri nawo.

¹⁰² Ndipo pamene mkazi alowerera kwina ndi mwamuna wina; pamene mpingo uchoka pamalo ndi mapurogramu a zikhazikitso awa, ndi mapurogramo a zomanga ndi masukulu, ndi zina zotero. Ine ndiribe kanthu kotsutsira izo. Izo zonse nzabwino. Izo zimathandizira cholinga chawo. Koma izo si ziri. . .

103 Yesu sananene konse, “Pitani, mukapange masukulu.” Iye anati, “Kalalikireni Mawu.”

104 Ndi pamene iwo sanawasamalire Iwo. Osati kupanga zikhazikitso, zipatala, ndi zina zotero. Zimenezo ndi zabwino, koma iyo si ntchito ya Mpingo. Ntchito yawo ndi kulalikira Uthenga, koma ife tachita china chirichonse kupatula izo. Ndipo ife talowerera umu, basi monga Satana anachitira, ndipo tazisakaniza izo ndi Uthenga wina, china chakenso, ndi china chakenso, mpaka izo ziri ndi chisokonezeko chosakhala kanthu. Chivundi, ngakhale lathu lonse, dziko lonse! Yang’anani kachitidwe ka dziko.

105 Powerenga *Reader’s Digest*, kuno osati kale litali, komwe asungwana aang’ono akudutsa kusintha kwawo kwa thupi, ndi amuna, kusintha kwa moyo, pakati pa usinkhu wa zaka twente ndi twente-faifi. Iwo akudutsa mu usinkhu wao wapakati. Chivundi, (bwanji?) chifukwa cha kafukufuku wasayansi wa zakudya ndi zinthu zomwe zafala, kuchokera ku zinthu zachilengedwe zomwe ife timayenera kumaika mu thupi lathu. Ife sitiri kanthu koma gulu la zivundi zakufa.

106 Tsopano, ndi chimene mpingo uli, nawonso. Iwo uli mu chikhalidwe chofanana.

107 Iye ali choimira. Iye ali nawo maukoma ofunika ofanana mwa Mzimu, zitapatsidwa kwa Iye, kuti ziziusunga Mzimu ndi Mawu, ndipo asamachite konse chigololo ndi chirichonse cha mdziko kapena chirichonse. Azikhala namwali kwa Mawu, monga mkazi ali woti azikhala waukoma kwa mwamuna wake. Icho ndi chidaliriko chopatulika, kuti azilemekeza Mawu a Ambuye Wake pamwamba pa kachikhulupiriro kopangidwa ndi anthu kalikonse, nzeru, chipembedzo chomwe chiripo. Mpingo unapatsidwa chidaliriko chimenecho.

108 Ngati iwo ati, “Chabwino, mpingo wanga...” Ine sindikusamala zomwe mpingo wanu umakhulupirira. Ngati izo ziri zosiyana ndi Mawu a Mulungu, khalani kutali ndi iwo.

109 Baibulo linati, “Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, kwanthawizonse.” Marko 16 anati, “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.” Ngati mpingo ulalikira zosiyana ndi Izo, inu musati. Inu mufe kwa chinthu chimenecho. Khalani obadwa kachiwiri, mu Mawu a Mulungu. “Pitani inu ku dziko lonse ndi kukalalikira Uthenga kwa cholengedwa chirichonse.” Ndiwo utali wake womwe Iwo ukanati uzipitira. “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira, mu dziko lonse, ndi cholengedwa chirichonse chomwe chiti chidzakhulupirire.” Mukuona momwe ife tafikira kutali kwa Iwo? Zedi. Koma Iye ali ndi choyankhira kwa Iwo.

110 Koma tsopano taonani chomwe, Hollywood, yachotsa zinthu zaukoma kwa akazi athu.

111 Ine ndakhala pano ndikuyang'ana pa mkazi wachikulire wokondedwa, Mlongo Schrader, ambiri a akazi pano, ndi kumbuyoko, ndi Mlongo Moore cha kuno, akazi achikulire omwe akukumbukira zaka zingapo zapitazo. Ngati amayi awo, kapena ngakhale iwo, akanamayenda pa misewu, momwe akazi ena awa akuyendera lero, mamembala a mpingo, iwo akanawatsekera akazi awo kuti ndi openga. "Iye waiwala kuvala siketi yake." Chabwino, ngati inali misala apo, ndi misala pano.

112 Chabwino, taonani, dziko lonse likutsimikizira kuti iyo ndi misala. Tayang'anani pa okupha ndi zinthu zomwe zikuchitika tsopano mu dziko. Mwaona? Misala!

113 Chinthu chonse chikubwera podzakwaniritsa Chivumbulutsu. Ife mwina tifika ku izo, sabata ino. Kumene, zinthu zowopsya izo, izo si zachibadwa. Ndi zinthu zamizimu, izo nzowapangitsa anthu kufuulira kwa miyala ndi mapiri, ndi china chirichonse, kuti zigwere pa iwo.

114 Misala yamphumphu, kwathunthu yomwe dziko lino liti lilowemo, pomwe pano, ilo liri pafupi pamenepo tsopano. Bwanji, inu mukuona moponda mapazi mwake. Ndi izo apo. I—iyo ikuyenda apo pomwe mu msewu, mpaka mu mipando ya mtchalitchi yomwe, misala yathunthu, kumachita zinthu zomwe munthu wokhalapo sakanati aziganiza kuti azizichita pokhala wotukuka.

115 Taonani zomwe Hollywood yachita kwa mkazi. Taonani momwe izo ziriri. Izo zaba maukoma opatulika a mkazi. Mopitirira pitirira, ife tikhoza kumapita. Mwaona?

116 Zonse izi iye wazitaya. Kodi iye wazichita motani izo? Chifukwa panali chida chothyathyalika chotchedwa mpingo, monga chinali uko mmunda wa Edeni. Munthu wothyathyalika, Mdierekezi, anayenda nalowa mu tchalitchi monga momwe iye anachitira mmunda wa Edeni, ndipo anamunyenga iye kuti alowe mu izo. Iye wanyengedwa. Mkaziyo akuganiza; iye sakutanthauza kuti akhale wolakwitsa.

117 Eva sanali kutanthauza kuti achite cholakwika. Izo sizinali mwadala. Koma iye. . . Baibulo linati, mu Timoteo Wachiwiri, Timoteo Woyamba 3, "Iye ananyengedwa." Ndipo *kunyengedwa* si pamene iwe uchita izo mwakufuna. Ndi pamene iwe wanyengedweramo kuti uchite izo.

118 Ndingo ndizo ndendende basi zomwe zachitika lero. Iye wanyengedwa, ndi televizioni, ndi magazini, ndi anthu awa, izi, zinthu zonse zabwino izi zomwe iwo akupitira nazo kunja, uko mu msewu. Atsikana amakono, iwo amayang'ana pa magazini ndipo iwo amayang'ana pa zithunzi. Iwo amayang'ana pa msewu. Iwo amawona zovala mmasitolo. Momwe Satana, chida chachikulu icho c—cha gehena, chabwera apo pakati pa anthu ndi kuwanyengera iwo mu zinthu izi! Ndipo mkazi amaganiza kuti iye ali bwino bwino. Ndipo iye ndi wakufa ndipo sakudziwa

izo. Iye ali kutali ndi Mulungu. Taonani momwe iye anataira zonse izi, ndi momwe izo zinaliri zochenjera?

¹¹⁹ Lero, ine ndikufuna inu kuti muzindikire. Yesu anayankhula za izo. Naponso, ngati inu mukufuna kuti muziwerenge izo, Yesu anatchula kuti chinthu ichi chikanadzabwera pomachitika. Kodi inu mukuzidziwa izo? Mu maora Ake otsiriza, kusanachitike kumene kupachikidwa Kwake. Tiyeni tingoziwerenga izo, Luka Woyera, m—mutu wa 23, ndipo kwa mphindi yokha, monga phunziro la Sande sukulu. Tiyambire ndi ndime ya 27, ine ndikukhulupirira ndasonyeza apa. Yesu akupita ku Kalvare. Mvetserani pamene ine ndikuwerenga izi. Chabwino. Luka Woyera 23:27, ine ndikukhulupirira, ndi pamene ife tiri nazo izo. Cholemba changa chiri nazo izo mwanjira imeneyo. Eya. Ndi izi apa.

Ndipo apo linamutsatira iye khamu lalikulu la anthu, ndi... akazi, omwe nawonso anamulirira ndikumumvera chisoni iye.

Koma Yesu potembenkira kwa iwo anati, Ana aakazi a Yerusalemu, musati mundilirire ine, koma dzilirireni nokha, ndi ana anu.

Pakuti, taonani, tsiku—masiku akudza,... omwe iwo adzati, Wodala ali osabala, ndi mimba yomwe siinayambe yabalapo, ndi maere omwe sanayambe ayamwitsapo.

¹²⁰ Taganizani, lero, nchamanyazi kuti iye akhale ndi mwana. Mwaona?

Ndiye iwo adzayamba kunena kwa mapiri, Gwerani pa ife; ndi map-... ndi mapiri, Tiphimbeni ife.

Pakuti ngati iwo akuchita zinthu izi kwa wauwisi—mtengo wauwisi, iwo adzachita chiani kwa wouma?

¹²¹ Akuyankhula za tsiku lomwe akazi sakanatinso azidzafuna ana. Iwo akumafuna garu kapena mphaka, kapena chinachake chonga izo, koma iye sakuwafuna ana panonso. Bwanji? “Iye ndi Mayi Hubbard wachikulire ngati iye akhala ndi ana.” Mwaona? Iye samawafuna. Ndi—izo ndi ndemanga zaku Hollywood. Iyo siikumafuna kuti mkazi wake azikhala Mayi Hubbard wachikulire. Kotero iye atero, akhala ndi opareshoni ina itachitidwa kwa mwamunayo kapena mkaziyo, mmodzi, yomwe iti iziwalepheretsa iwo kuti azikhala ndi ana. Iwo sakuwafuna ana ayi.

¹²² Yesu anayankhula za izo. Ndipo kodi Iye anati chiani? “Panthawi imeneyo iwo adzayamba kulirira kwa miyala ndi mapiri kuti zigwere pa iwo.”

¹²³ Iye azidzaphunzira za kulera, kuti iye azikhoza kumapita ku maphwando. Iye asati azivutitsidwa ndi mwana akumuyamwa iye. “Izo zimuchotsera iye mawonekedwe. Pamene iye ali ndi

pakati, izo zikhala ziri, izo zimuchotsera iye mawonekedwe. Iye samawoneka momwe iye ankawonekera.” Ndipo mwamuna wake, waumbuli mokwanira kuti amamulola iye kuti azipita mwanjira imeneyo. Mkaziyo samupatsa iye mwana.

¹²⁴ Yesu anayankhula za izo. Ndipo Iye ananena, kuti, “Pamene iwo ali kuchita izi, pa nthawi imeneyo iwo adzakhala akulirira kwa matanthwe kuti agwere pa iwo.” Ndiko Kudza kwa Ambuye.

¹²⁵ Iwo amalipira ndalama zochuluka kwambiri pofuna amphaka, agaru, kuti aziwalera. Ndiko kulondola. Iye ayenera kuti azilera chinachake, chifukwa ndi chikhaliidwe choperekedwa ndi Mulungu kwa iye.

¹²⁶ Ine ndikuzindikira. Ine ndimasaka nyama zazikulu. Chimbalangondo chachikulu mu kugwa kwa chaka, pamene icho chimakhala chitabala chimbalangondo champhongo, icho chimakhala ndi ana ndiye omwe abadwa. Iwo amakhala ana a usinkhu-wabwino ndithu, mwinamwake olemera mapaundi handiredi kapena kupitirira. Iye amawapangitsa iwo kugona ndi kudzizimbaitsa, chifukwa iye akuti abalepo ana ena. Iwo amabadwa mu Febrewale. Chimbalangondo sichimadziwa kanthu za iwo.

¹²⁷ Iwo amabadwira mu timatumba tating’ono. Momwe Mulungu amawapangitsira iwo kuti azitsegula timatumba tating’ono ito, mwaokha, aang’ono...monga timatumba tating’ono ta zikopa zopyapyala. Iwo amapeza mpata wao woyendayenda. Manthu wawo amakhala ali mtulo zedi. Iye amakhala asanadye kalikonse kuchokera mu Oktobala, ndipo uyu ndi Febrewale. Iwo amabwera apo ndi kudzamuyamwa iye mpaka pakati pa Meyi.

¹²⁸ Ndiye pamene iye awaona ana ake, iwo ali ana ausinkhu wabwino ndithu, olemera mwinamwake mapaundi fifitini, teni kapena fifitini kalikonse. Iwo atamuyamwa iye. Momwe iye amapezera mkaka, ilo ndi lingaliro la Mulungu. Iye amakhala moyo, payekha, ndi kumatulutsa mkaka kwa anawo.

¹²⁹ Ndiyeno ngati kubala kwake sikuchitika, ndipo iye akakhala alibe ana konse, iye amawasaka iwo kwa chaka, ana a chaka chatha, ndi kumawalera iwo utali wa nthawi yonse ya chirimwe, chifukwa ndi kudziwa kopatsidwa ndi Mulungu. Iye amayenera kuti azilera chinachake.

¹³⁰ Ndipo ngati mkazi sakhala ndi mwana kwa mwamuna wake, iye amatenga garu kapena mphaka, kapena chinachake. Iye amayenera kuti azilera chinachake. Ndi chilengedwe. Koma kuti amubalire mwana mwamuna wake, ndi kumamulera iye ku utumiki wa Mulungu, izo ziri kwathunthu kunja kwa mzere wake. Iye ayenera. O, iye adza...O, iye angamachititsidwe manyazi kwambiri, ngati iye atatero, ndi gulu lake lokonda tchimo la mtundu wa akazi a 1965.

¹³¹ Chithunzi choona cha mpingo wamakono lero! Sikuti mpingo wamakono ukufunanso zirizonse za izi pano, kukuwa, kufuula, kuyankhula mmalirime, ana aang'ono a Machitidwe 2:38 pomwe iye ali. Eya. Eya. Mwaona? Eya. Iye sakufuna zirizonse za izo, kuisima ndi kulira, ndi kumakuwa, "Ameni! Aleluya!" Bwanji, mwana woteroyo mwamsanga angamutulutsitse iye mu chipembedzo chake. Iwo akanakhala nazo zina zonga izo mu umodzi wa mipingoyi, bwanji, iwo akanamuponyera iye kunja mwamsanga ndithu.

"Chifukwa chiani inu mukuloleza zinthu zotere monga izi kumapitirira?"

¹³² Kotero, inu mukuona, iye ali ndi pakati pa chinachake, chifukwa iye akumabala mamembala nthawizonse. Koma iye sakufuna kumakuwa kulikonse kwa iwo, kufuula, kumachita chibwibwi, Machitidwe 2:38, zolengedwa zomvetisa chisoni omwe iye akuganiza kuti iwo ali. Izo zikanati ndithudi zimuchititse manyazi iye. Izo zikanati zimuwonongere iye bungwe lake la maphunziro, a makhaliidwe, a mpingo wa mwasayansi lomwe iye alimo kuno. Iwo angamuponyere iye kunja, pa bungwe lotsatira. Iye sangakhoze kukhala nawo iwo. Kotero iye sakufuna kuti akhale ndi pakati nao Mawu, chifukwa ndiwo mtundu wokha womwe Mawu angakhoze kuwabala.

¹³³ Wobadwa ndi Mzimu wa Mulungu, iwo uli ndi Mzimu wa Mulungu mkati mwake. Palibe kujowina mpingo kwaluntha ndi kupita ndi kachikhulupiriro, odula tsitsi, nkhope zolochedwa; kulibe chinthu chotero monga icho mu zonse za Iwo. Inu simumazipeza izo mu Mawu a Mulungu. Inu mumamupeza mwana wa kachitidwe kachikale, woyeretsedwa, wodzazidwa Mzimu Woyera, wobadwa ndi Mzimu wa Mulungu, akukuwa, akuphokosera, akufuula, akutamanda Mulungu.

¹³⁴ Izo zonse ziri patali pa kufikira kwake. Iye samafuna Zimenezo. O, ayi, bwana! Ayi, ndithudi. Kodi iye amachita chiani ndiye? Kotero iye akubweretsa apo gulu, la a nkhope zolochedwa, lovala zazifupi, la Yezebeli, lapathengo la "amphaka," iwo amawatcha choncho, ine ndikuganiza izo ziri. Mwaona? Ine ndikuganiza iwo amawatcha iwo amphaka. Mwaona? "Tamuonani mphaka uyo akupita apoyo," iwo amatero, kapena chinachake chonga izo, inu mukudziwa.

¹³⁵ Iye anabadwa, kapena anakwatiwa, analumikizidwa ndi mwamuna wake woyamba, Adamu woyamba, ndi mkazi wachigololo uja Eva, mkazi woyamba wa Adamu. Inu mukuti, "Wachigololo?" Iye ndithudi anali. Koma, o, iye amadzinenera kuti Adamu uyu, Adamu woyamba uyu, anafa. "O, zedi, iye anafa nthawi yaitali kale. Ine ndabadwanso, kachiwiri," iye amatero, "ndipo ine ndithudi ndakwatiwa kwa Adamu Wachiwiri, Khristu, Mawu."

¹³⁶ Motani? Zindikirani zomwe iye akuzikonda. Mpenyeni womkonda wakeyo, inu mukufuna kuti muwone yemwe iye ali mu chikondi naye. Mawu amanena *Izi*, koma iye amati, “Mpingo wanga ukunena *izi*.” Ndiye iye ali mu chikondi ndi ndani? Mwamuna wake ndi ndani? Zipatso zake zomwe zikutsimikizira chomwe iye ali. Ndendende kulondola, zikusonyeza chomwe iye ali. Zindikirani. Iye anabadwira, poyamba, kwa Adamu, chifukwa ndiko kubadwa kwake kwachilengedwe. Mwaona? Ndipo iye sanazisiye konse izo. Iye ndi wokonda za mdziko. Iye amadzinenera kuti anabadwira nthawi yachiwiri, kwa Khristu. Koma womkonda wake, zindikirani, ndi Adamu, apabe, chifukwa iye amalikonda dziko.

¹³⁷ Ndipo china—chinthu china, zindikirani mtundu wa ana omwe iye akuwabala. Izo zikutiuza yemwe bambo wawo ali, ngati ali Adamu woyamba kapena Adamu wachiwiri. Ngati Mpingo ubala mwana wa Adamu Wachiwiri, iye amachita mwakachitidwe ka Adamu Wachiwiri, monga iwo anachitira pa Tsiku la Pentekoste. Amenewo ndiwo ana enieni owona a Adamu Wachiwiri. Mukuona? Kulondola. Chikhalidwe chawo chiri monga chake ndi cha mkazakeyo. Inde, bwana. Ana ake aakazi, ankhope-zolochedwa, atsitsi lodulidwa, ovala zovala zachimuna, matharauza. Baibulo limati kuti iye “asamachite izo.” Iye amalidula tsitsi lake. “Ndi zamanyazi kwa iye.”

Inu mukuti, “Tonthola, pa zimenezo.”

¹³⁸ Ndi chimene Mawu akunena. Ine ndikulozera kokha ku chirengedwe. Ndicho chimene iye amachita.

¹³⁹ Ana ake, ana ake obadwa kuchokera mwa iye, amadalira pa maphunziro, kuphunzira, sukulu ina ya Baibulo, yotchedwa choncho, koleji ina yaikulu yomwe ikuyenera kuti yakhalapo nthawi yaitali yapitapo, ikuwagogomola iwo, mu china chokhala ngati kachitidwe koutamira. Ofunafuna chipembedzo, achipembedzo monga-Kaini, apathengo basi ku Mawu monga Kaini analiri; kulondola, odwala basi, apathengo monga Kaini analiri, ndithudi, ofunafuna zachipembedzo. Inu mukuona chomwe icho chiri?

¹⁴⁰ Mulungu sanapange konse bungwe chipembedzo. Iye nthawizonse wakhala akutsutsana nazo. Mawu Ake amatsutsana ndi izo.

¹⁴¹ Koma iwo akugwiritsitsabe kwa izo, kotero inu mukuona zomwe iwo akubala apo. Izo zikusonyeza yemwe bambo ndi mayi wawo ali. Ndendende. Ndendende. Apathengo basi monga Kaini analiri. Ndiwo mtundu wa mwana yemwe iye anamubala kuchokera kwa Eva. Iwo anachoka ku Mawu, ndiye mukuwona zomwe iye anzibweretsa. Ndizo ndendende basi zomwe mpingo wabweretsa, chinthu chomwecho.

¹⁴² Ndikhoza kutsimikizira izo kwa inu, mwa Mawu, kuti ndi pamene maphunziro ndi chitukuko chinadzera, kupyolera mwa

Kaini. Ndizo ndendende kulondola. Pakuti iwo akudzinenera . . . Koma i—iwo akudzinenera kuti ali ana a Mulungu, koma iwo ndi mtundu wachipembedzo, masikolala a sukulu a mwachipembedzo, china chirichonse. Ndizo ndendende kulondola. Ochenjera, anzeru! Mai! Chomwechonso anali serpenti, bambo wao. Kulondola. Ochenjera basi ndi alaliki amwasayansi momwe Kaini analiri. Mukuona? Ziri ndendende chinthu chomwecho.

Inu mukuti, “M’bale Branham, kodi izo nzoona?”

¹⁴³ Tembenezirani ku Genesis 4:16 ndi kukapeza apo. Pitani mmbuyo umu pa Genesis 4:16, miniti yokha, inu mupezapo momwe izo zinachitikira.

Ndipo Kaini anapita . . . kuchoka pamaso pa AMBUYE, ndipo anakakhala mu dziko la Nodi, kummawa kwa Edeni.

Ndipo Kaini anamudziwa mkazi wake; ndipo iye anaïma, ndipo anabala Enoki: ndipo iye anamanga mzinda, ndipo anawutcha dzina la mzindawo, motengera . . . mwana wake, Enosi.

¹⁴⁴ Mpaka mmusi kwa Tubala, mpaka pansi, pakuti iwo anayamba, kunabwera okonza zin’gwenyen’gwenye, nyimbo, ndi zina zotero. Chitukuko chinabwera ndi Kaini, kulondola, kumanga mizinda, zida. Amuna asayansi anabwera ndi Kaini, mbewu ya serpenti. Tsopano zindikirani ndime ya 25.

Ndipo Adamu anamudziwa mkazi wake kachiwiri;

¹⁴⁵ Tsopano, iye anamudziwa iye kamodzi ndipo iye anali ndi ana awiri. Fufuzani Lemba. Iye anali ndi Kaini ndi Abele. Kuchita kumodzi, ndipo ana awiri. Inu mukuti . . .

¹⁴⁶ Iwo anandiuza ine, osati kale litali, izo sizingakhoze, kuchitika. Ife tiri ndi nkhani mu Hollywood. Hollywood? Ife tiri nayo nkhani mu Tucson pakali pano, uko mu bwalo la mulandu. Mkazi anabala mwana wachikuda ndi mwana wachizungu, pa nthawi yomweyo. Iwo ankati iye sakanakhoza kuchita izo. Iye akhoza kukhala ndi mbewu ziwiri zachonde, naponso. Iwo ali nazo izo mu bwalo la mulandu tsopano. Ine ndikudziwa agaru angachite izo. Zinyama zingachite izo. Ndipo iye anali nawo uko. Mzunguyo anati, “Ine ndizimuthandiza mwana wanga wangayo, koma osati uyo.”

¹⁴⁷ Ndipo mkaziyo anavomereza. Iye anakhala ndi mwamuna wake mmawa umenewo, ndi bambo wachikuda madzulo amenewo. “Ngati ziri mu,” adotolo akuti, “mu danga la maora twente-foro, izo zingachitike ngati pali mbewu ina ya chonde apo.” Ndipo apo mkaziyo anazichita izo.

¹⁴⁸ Ndipo ndizo ndendende zomwe zinachitika apa. Kaini yemwe . . . Satana, mmawa umenewo, mwa serpenti; ndipo

Adamu, madzulo amenewo. Pamene iye...Ndipo mkaziyo analandira ana awiri.

Tsopano, *Adamu anamudziwa mkazi wake kachiwiri* (nthawi yachiwiri); *ndipo iye anabala mwana, . . .*

¹⁴⁹ Kumbukirani, palibe paliponse mu Baibulo pamene anati Kaini anali mwana wa Adamu. Anati, “Iye anali wa woipa uyo,” osati Adamu, “Mdierekezi.”

. . .anamudziwa wake (nthawi yachiwiri), ndipo anamudziwa . . .ndipo anakhala *ndi mwana, ndipo anamutcha dzina lake Seti: Pakuti Mulungu, anatero mkaziyo, wandisankhira . . .*(Imeneyo sinali Mbewu yeniyeni.) . . .*wandisankhira ine mbewu ina mmalo mwa Adamu, yemwe Kaini anamupha. Kotero . . .*

Ndipo kwa Seti, kwa iyenso kunabadwa mwana wamwamuna; ndipo iye anamutcha dzina lake Enosi: ndiyeno anthu anayamba kuitanira pa dzina la AMBUYE.

¹⁵⁰ Osati kuchokera kwa Kaini, mzere wa m’badwo uwo, koma kuchokera ku m’badwo wa Seti.

Kotero, “Kaini ndi woipayo.” Apo pakudzano serpenti.

¹⁵¹ Tsopano zindikirani. Baibulo limanena mwachimvekere apa, kuti, “Mwamuna wake woyamba ayenera akhale atafa,” osati kungosiyidwa. Iye ayenera kukhala atafa.

¹⁵² Ine ndangotsiriza kumene kulalikirira pa *Chikwati Ndi Chilekano*, ndipo inu nonse mukudziwa za izo. Ine sindiri kuyankhula tsopano, zonse palimodzi, kwa gulu lino pano, koma ku fuko lonseli. Chabwino. Tsopano inu mukuona zomwe zinachitika uko, mu *Chikwati Ndi Chilekano*. Pamene . . .?. . . Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri zinatsegulidwa, izo zinabweretsapo Choonadi chenicheni cha izo.

¹⁵³ Kotero, kuti ukwatiwe kwa Adamu Wachiwiri, Khristu, Mawu, iwe uyenera kuti udzilekanitse wekha mwa imfa, kuchokera kwa mwamuna wako woyamba wachipembedzo, chifukwa kulibe chimodzi cha izo chomwe chingakhoze kuwatenga Mawu onse a Mulungu. Mungondisonyeza ine kumene chimodzi icho chiri. “O,” inu mukuti, “changa.” munthu winayo ati chake, nayenso. Ziikeni izo palimodzi, ndipo inu mupeza kuti nonsenu mukulakwitsa, mwamsanga pamene inu mupanga chipembedzo. Kawerengeni Chivumbulutso 17. Kotero, inu mukuwona, inu muyenera mukhale mutafa kwa chinthu chimenecho.

¹⁵⁴ Tsopano, ine sindikunena gulu lapanoli. Ine ndikuyankhula kwa onse palimodzi ku fuko lonseli. Inu muyenera mukhale mutafa kwa mwamuna wanu woyamba. Ngati inu mwalumikizidwa kwa Khristu ndipo nkukhala muli okwatiwabe kwa chipembedzo, ndinu wachigololo. Ndinu wachi Laodikaya.

155 Mpingo mu fuko lonseli, ife tikumutsatira Yesu Khristu, Mawu. Kuti mukakhale mwa Mkwatibwi, inu muyenera kuti mukwatitsidwenso kwa Mawu a Mulungu, omwe ali Khristu. “Pachiyambi panali Mawu; Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu. Ndipo Mawu anapangidwa thupi ndipo anadzakhala pakati pathu.”

156 Utali wonse womwe inu mukugwiritsa ku mwambo wa anthu wa zipembedzo, inu mukutchedwa, mu Mawu a Mulungu, “wachigololo.” Utali wonse womwe inu muli wachipembedzo wofunafuna-kachikhulupiriro, kukhala wa mu mpingo wachipembedzo womwe umawakana Mawu, inu ndinu “wachigololo,” nzomwe Baibulo linanena.

157 Yesu anati, “Inu simungakhoze kutumikira amulungu awiri pa nthawi yomweyo. Inu mwina muzimutumikira Mulungu kapena mamoni.” *Mammon* ndi “dziko.” “Iye amene akonda dziko, kapena zinthu za mdziko, chikondi cha Mulungu sichiri nkomwe mwa iye.” Mbewu ya Mulungu siingakhoze kukhala mwa iye nthawi yomweyo (chikondi cha Mulungu) chikondi cha dziko chiri mmenemo. Pamene Mbewu ya Mulungu ikugwira ntchito kupyolera mwa inu, amenewo ndi Mawu a Mulungu. Chikondi cha dziko sichingakhoze kukhala mmenemo pa nthawi yomweyo. Tsopano tsitsi lalifupi liri pati, ndi zazifupi, ndi nkhope zolochedwa? Tsopano ziri pati izo?

158 Iwe sungakhoze kukhala waukoma kwa Khristu, Mawu a Mulungu, ndi kumatumikira chipembedzo chopangidwa ndi anthu pa nthawi yomweyo. Ndi zosiyana ndi Mawu. Paulo ananena apa. “Patipo?” Aroma 7.

159 Ngakhalenso kuti inu simungakhoze kumabala ana a Mulungu, a Mawu Ake, kwa gulu ili lapathengo la chipembedzo. Inu simungakhoze kuchita izo. Mu chofungatira chanucho, inu simungakhoze kubaliramo mwana wa Mawu a Mulungu. Ine ndikuyankhula kwa mpingo. Komabe inu mukumadzinenera kuti ndinu achipembedzo kwambiri. Chomwecho anali Kaini, mwana wa wachiwerewere Eva, wachipembedzo kwambiri, anamanga maguwa ndipo anapereka nsembe, ndipo ankapereka zakhumi zake ndi kumachita chirichonse chomwe munthu aliyense wachipembedzo akanakhoza kuchita. Koma iye analephera kuti awasunge Mawu awo. Iye analephera kuti akhale ndi vumbulutso.

160 Ndipo vumbulutso ndi chinthu chokha, vumbulutso la Mawu. Ndi chiani. . . Kodi vumbulutso ndi chiani? Yesu anati, “Pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga, ndipo zipata za gehena sizingakhoze kuulaka Iwo.” Chikhulupiriro ndi vumbulutso; chifukwa Chikhulupiriro chaululidwira kwa iwe.

161 “Abele, mwa Chikhulupiriro, anapereka mwa vumbulutso (Chikhulupiriro), anapereka kwa Mulungu nsembe yopambana kwambiri kuposa ija ya Kaini.”

¹⁶² Kaini ankaganiza kuti iwo anadya maapulo. Iwo akadali nalobe lingaliro limenelo, koma izo sizinali. Icho chinali chigololo, mbewu ya serpenti. Ndipo uko pamene Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri zinatsegulidwa, izo zinalongosola izo ndi kuzitsimikizira izo. Bukhu langa lomwe langotulutsidwa pa izo. Ndikuganiza, ife tiri nawo chikwi pano tsopano. Mwaona? Zindikirani. Izo ndi Mwamalemba, kuchokera ku Genesis mpaka Chivumbulutso.

¹⁶³ Pa nthawi yotsiriza, mitengo yonseyo ikubwera pokhala mbewu ndi kuzitsimikizira yokha. Pano ife tiri, lero lomwe, laodikaya ndi Mkwatibwi, momveka basi ndi mokongola momwe izo zingakhoze kukhalira mu Lemba, ndipo ziri patsogolo pomwe pa nkhope zanu. “Inu simungakhoze, kumatumikira Mulungu ndi mamoni.” Inu simungakhoze kukhala Mkristu wokhulupirira-Baibulo waukoma ndi kumadziyanjanitsa nokha mu zochitika zazipembedzo. Inu simungakhoze basi kumachita izo pa nthawi yomweyo. Mmodzi ayenera kuti afe, ndi kumulola winayo azikhala moyo.

¹⁶⁴ Ngakhalenso kuti simungabale mwana wa Mawu a Mulungu. Ngakhalenso kuti mpingo sungakhoze kumabala. Iwo samafuna mmodzi—mmodzi wa iwo, ana okuwa, ofuula ndi kumayankhula mu malirime, ndi zinthu zonse izo. Iwo, inu simungakhoze kumachita izo mu mpingo wachipembedzo. Iwo sangakhale nawe iwe. Iwo samawalera iwo monga choncho. Iwo amawatenga iwo ndi kuwagwedeza dzanja lawo ndi kuti, “Ngati inu mwakhulupirira, inu muli nawo Iwo. Bola ngati inu mwalembetsa dzina lanu pa bukhu, ndizo zonse zomwe inu mukuyenera kuti muchite.” Mukuona? Ndi—ana apathengo kwa Mawu, nkumadzinenerabe kuti ndi opembedza.

¹⁶⁵ Ali ndi pakati kwambiri ndi nzeru za Satana ndi chidziwitso, mpingo wakhalano! Iwo amawatumiza anthu awo kwina ku sukulu, kuti akaphunzire momwe angamanenere “ameni” molondola basi. Iwo amawaphunzitsa iwo momwe angamanenere zonse izi, ndi kukhala aluntha kwambiri. Ndi chiani icho? Ndi kupereka pakati kwa Mdierekezi. Kodi Satana anamupatsa pakati Eva ndi chiani? Kuti asawakhulupirire Mawu, pofuna zaluntha, luntha, ndipo izo zinawononga chirengedwe chonse. Ndizo ndendende zomwe iye wachita mu Mawu lero, mpingo. Iye wadzipatsa pakati yekha ndi masukulu a Baibulo ndi makoleji, ndi zinthu zonga izo, kuwerenga, kulemba, masamu, ndipo iwo sakudziwa nkomwe za Mulungu kuposa momwe Nkafula angadziwire za wonyamula lupanga wachi Igupto. Iwo amadziwa tizikhulupiriro tawo tonse, mabuku awo pa pemphero, china chirichonse, koma samadziwa kanthu za Mulungu.

¹⁶⁶ Iwo amadziwa kuti pamene Mawu atsimikiziridwa, pamene Mulungu ankayankhula mmbuyo umo ndi kuikapo Mawu ake a kwa kam’badwo kalikonse pamene iko kamabwerapo motsatira.

Apa panadza Nowa motsatira, ndipo iye analalikira kwa kam'badwo kameneko.

¹⁶⁷ Tsopano, bwanji ngati Mose akanabwera motsatira, nati, “Tiyeni timange chombo”? Iye akanakhala yense kunjwa kwa zochitika. Koma iye anali mneneri. Iye anali nalo vumbulutso la Mulungu.

¹⁶⁸ Mulungu anazitsimikizira izo kuti ndi Choonadi. Iye anawatulutsa ana pafupi, kumutulutsa Israeli, ndipo anasonyeza Lawi la Moto patsogolo pawo, ndipo anamutsimikizira mneneriyo; ndipo ananena ndendende basi zomwe Iye akanati achite, ndipo Iye anazichita izo.

¹⁶⁹ Iwo anati, “Musamulole Mulungu kuti aziyankhula. Muloleni Mose aziyankhula, kuwopa kuti ife tingafe.”

¹⁷⁰ Iye anati, “Ine sindidzayankhula kwa iwo kenanso monga choncho, koma ine ndiziwadzutsira iwo aneneri, ndipo iwowo aziyankhula.”

¹⁷¹ Apo panaima Yesaya ataima pamenepo, anati, “Namwali adzaima.” Bambo ngati iyeyo mu tsiku pamene. . . Kodi namwali akanati ayime chotani? “Kwa ife Mwana wamwamuna wabadwa: mwana wabadwa, Mwana wamwamuna waperekedwa. Dzina Lake azidzatchedwa Wauphungu, Kalonga wa Mtendere, Mulungu Wamphamvu, Atate Wosatha. Ali pa mpandowachifumu wa atate Ake, Davide, Iye azidzalamulira. Sipadzakhala mapeto ku ulamuliro wa Ufumu Wake.” Kodi izo zizidzakhala motani? Iye sanali kudziwa. Iye ankangoyankhula zomwe Mulungu akananena. Ndi zopitirira kulingalira kulikonse, kwaluntha. Ndi zopitirira kafukufuku aliyense wasayansi. Ndi Mawu a Mulungu.

¹⁷² Tsopano ife timawaphunzitsa ophunzira athu a mmaseminare mu mitundu yonse ya fioroje za Baibulo ndi zinthu zonga izo, fioroje yopangidwa ndi anthu, tiri ndi gulu la mpingo chimodzimodzi basi la Laodikaya, monga Mulungu anati izo zikanadzakhala ziri. O, mai! Pamene ine ndiyang'ana pa izo, ndipo zimandipangitsa ine kunjenjemera. Kupatsidwa pakati pa lingaliro laluntha! Iwe uyenera kukhala wochokera ku sukulu yapamwamba iwe usanalowe nkomwe. Iwe uyenera kuti ukhale nazo. . . uyenera kukaima pamaso pa wopima zamisala iwe usanati udzozedwe.

¹⁷³ Kodi inu mungalingalire Petro, Yakobo, ndi Yohane akupita pamaso pa wopima zamisala? Mukukumbukira handiredi n twente aja pamwamba paja, sankakhoza ngakhale kulemba dzina lawo lomwe? Kuima patsogolo pa wopima zamisala, kuti awone ngati iwo. . . ngati zonse zawo. . . ngati kuganiza kwawo kunali kwabwino basi, ndi zina zotero? Iwo anali ndi kuganiza, koma iko sikunali kwa lingaliro laluntha kapena kafukufuku wasayansi. Izo zinali kupyolera mu mphamvu ya Mulungu. Pamene Iyo inkawakhudza iwo, iwo sankadziwa kanthu koti

achite koma kuchita zomwe Mzimu Woyera unati achite. Iwo sankapereka tcheru chirichonse ku luntha lirilonse, zomwe mpingo unanena, ndi zomwe ansembe ananena, zomwe *awa* ananena, *awo* ananena. Iwo ankasuntha mwa Mzimu; amuna opanda mantha.

¹⁷⁴ Yohane Woyamba 2:15, Iye anati, “Ngati inu mukonda dziko, kapena zinthu za mdziko, chikondi cha Mulungu sichiri nkomwe mwa inu.” Mwaona? Kotero inu mungakhoze bwanji kupatsidwa pakati ndi Mawu a Mulungu omwe amalitsutsa dziko, amaitsutsa Hollywood, amawatsutsa mafashoni ake onse, amatsutsa maphwando onse awa ndi kupitiriza, ndi zotchedwazo zomwe iwo ali nazo mu dzina la chipembedzo? Iwo amazitsutsa izo. Mawu angakhoze bwanji kumupatsa pakati munthu: mkazi wa tsitsi lodula angakhoze bwanji, wa nkhope yolochedwa, wovala zazifupi?

¹⁷⁵ Mlaliki angakhoze bwanji, kumapita kunja uko ku seminare, ndi kumayang’ana pa Machitidwe 2:38 ndi kuwona kuti palibe munthu mu Baibulo yemwe anayamba wabatizidwapo mu maudindo amenewo, ndiyeno nkumanenabe kuti iye ali ndi pakati pa Mawu a Mulungu? Akukuuzani inu bodza! Iye wagulitsa ufulu wake wobadwa nao. Iye wachita chigololo motsutsa Chinthu chomwecho chimene iye amachinena. Iye wasiyidwa, mu chilekano.

Mulungu akhala nawo Mpingo wangwiwo, ndendende basi, Mkwatibwi.

¹⁷⁶ Baibulo linati, “Mawu sali mwa inu.” Kotero ndi ana a mtundu wanji omwe inu mukuwabala? Zipembedzo zopatsidwa pakati. Sipanakhale imfa yoti ikulekanitseni inu kwa wokondana nanu woyamba.

¹⁷⁷ “Kodi a Jones aziganiza chiani ngati ine nditi ndiyambe kumalira ndi kumayankhula mu lirime? Kodi iwo aziganiza chiani ngati ine nditi ndibatizidwenso?” Ndi zamkutu bwanji! Kodi inu mwakwatiwa kwa a Jones? Kodi inu mwakwatiwa kwa mpingo? Kodi inu mwakwatiwa kwa Khristu, Mawu?

¹⁷⁸ Tsopano, ndicho chifukwa iye akubalabe ana ake. Kodi iye ali ndi ana a mtundu wanji? Pano pali maina awo ena omwe iwo akuwacha lero: amphaka, zimfutandowe, zinkhanira, marickie, maricketta. Amphaka, zimfutandowe, amenewo ndi mamembala a mpingo. Zedi. Onsewo ndi ana ake, ana a Kaini, omwe ali ana a chirombo chothyathyalika, osalala basi monga iwo angakhoze kukhalira.

¹⁷⁹ Tsopano tatangani kuyang’ana kwabwino kwa mphindi, ndi kupenya kwanu komwe kwauzimu, pa solo yanu. Ingoyang’anani pozungulira. Ine ndikuyankhula kwa fuko lonseli tsopano. Tayang’anani maminiti pang’ono okha, inu kunja uko mu Branham Tabernacle, inu muli mu makachisi ku Gombe Lakumadzulo, ndi Arizona, ndi kulikonse komwe inu muli.

Tadziyang'anani pa inu eni kwa maminiti pang'ono. Inu mukuti, "Uthenga uwo womwe inu mukuulalikira, M'bale Branham, ndi wolakwika." Tadziyang'anani pa inu eni pang'ono pokha. Muulole Mzimu Woyera uwafufuze malingaliro anu ndi Mawu, inu muvomerezana nao Uthengawu. Muloleni Khristu, Mawu odzozedwa, achifufuze chikumbumtima chanu chomwecho. Muloleni Iye abwere mwa inu, muwone ngati Iwo ali olakwika kapena ayi. Ndipo izo ndi chinthu chimodzi kapena ziwiri zomwe ine ndazitchula, pamene ziripo mazana a izo.

¹⁸⁰ Kodi Baibulo limavomereza mkazi kuti azidula tsitsi lake? [Osonkhana ati, "Ayi."—Mkonzi.] Kodi Baibulo limakhulupirira, limagwirizana ndi maubatizo, a utatu mu dzina la "Atate, Mwana, Mzimu Woyera"? ["Ayi."] Osati chinthu choterocho. Kodi Baibulo limagwirizana ndi mkazi kumavala zovala zachimuna? ["Ayi."] Chabwino, tangotenga zitatu izo apo, pamene ziripo mazana enanso. Kafufuzeni izo mu Kuwala kwa Mawu a Mulungu.

¹⁸¹ Inu mukuti, "Ine ndine membala wa mpingo." Chomwechonso anali Kaini. Chomwechonso anali Eva. Baibulo limaneneratu, mu masiku otsiriza, kuti Laodikaya akanadzakhala chimodzimodzi.

¹⁸² Uloleni Mzimu Woyera ufufuze chikumbumtima chanu, ndipo inu muvomerezana ndi Daniele 5:12. Pamene mfumukazi anabwera pamaso pa Beltesaza, ndipo anati iye anapeza kuti kunali mneneri, Daniele, anali pakati pa iwo, ndipo iye anali wosungunula zokaika. Inu muulole Mzimu Woyera. Iyeyo ndiye Mneneri wa tsikuli. Muloleni Iye abwere mu mtima mwanu pakali pano ndipo awufufuze ndi Mawu a Mulungu, ndi zokaikazo pa Uthenga zikhala zonse zitakonzedwa. Iye amasungunula zokaika zonse. Inu mupeza kuti, izo ziri ndendende pa Mawu a tsiku lino.

¹⁸³ Inu simungakhoze kumalalikira uthenga wa Lutera lero. Iwo ukupita mmenemo, koma awo ndi mapazi. U-nhu. U-nhu. Simungakhoze kulalikira wa Wesile. Simungakhoze kulalikira Chipentekoste. Ife tazidutsa kale zimenezo. Iwo achita chipembedzo ndipo afa. Iwo ali phesi.

¹⁸⁴ Phesi linatulukira ndi tsamba, pa chikhalidwe choyamba cha mpingo. Tsopano, izo sizimawoneka monga njere yoyamba yomwe inapita mu nthaka, tirigu.

¹⁸⁵ Chachiwiri kubwerapo chinali utuchi. Iwo sumawonekabe monga njere. Umawoneka mochulukirapo monga izo. Izo zikubwera mochulukira ku chifanizo cha njere yeniyeni. Koma masamba ndithudi samawoneka ngati njere yomwe inapita mu nthaka. Iwo ndi chonyamulira cha moyo womwe unali mu njere. Koma kodi iwo anachita chiani? Iwo anachita chipembedzo, basi monga chirengedwe china chonse chimagwiriza mmenemo ndi izo. Izo zinafa.

¹⁸⁶ Ndiye chiani? Moyo umayenderera mpaka ku ngayaye. Izo zimakhala ndi tating'ono tambiri—timipira tating'ono titakanirira pa icho, timawoneka ngati tinjere tating'ono—ting'ono mwa icho. Ito timawoneka ngati njere zenizeni, koma izo siziri.

¹⁸⁷ Ndiye ito timagwera mu nkhusu. Ndipo kodi ito timabweretsapo chiani? Nkhusu.

¹⁸⁸ Tsopano, inu mukatenga njere ya tirigu, pamene tirigu akutulukira koyamba. Ndipo Yesu anati, “Njere ya tirigu.” Ndipo inu mukamutenga tirigu uyo ndi kumutsegula iye. Inu mukamusolola mu phesi. Inu mukayang'ana pa iye. Inu mumati, “Ife tiri ndi njere ya tirigu.” Samalirani. Izo ziri ndendende basi monga njere, koma mulibe kakang'ono ka njere mmenemo. Ndi nkhusu.

¹⁸⁹ Apo pali Achipentekoste, “Mochuluka kwambiri,” monga Mateyu 24:24 anati, “nkunyenga Osankhidwa omwe mu masiku otsirizawa, ngati kukanakhala kotheke.” Koma inu mukakankhira mmbuyo tsamba ndi tsamba, inu mulibe njere ayi. Njere ili kumbuyo komwe kwa iyo. Mwaona?

¹⁹⁰ Ndiyeno Moyo umatuluka kuchokera ku chipembedzo chimenecho, umapita mu njere. Ndiye chimachitika ndi chiani? Pamene njere iyamba kukula, ndi kufika pokulirapo moti Iyo ikhoza kuphimba pa chinachake, chipembedzo chimakang'anuka pa Iyo. Nchifukwa chiani ife sitinakhale ndi chipembedzo kuchokera mu Izi? Sipadzakhala pali konse. Ayi. Ndi mbewu. Iyo siingakhoze kupita patsogolo penanso. Ife tiri pa nthawi yotsiriza. Kotero kodi Iyo ikuyenera kuti izichita chiani tsopano? Kugona mu kukhalapo kwa Mwana, kuti iche, ndizo ndendende, Mawu kuti ache mu mtima mwanu, kuti azibala ndi kukhala moyo zomwe ife tiri kuzikambazi. Inde, bwana.

¹⁹¹ Ndiye inu simudzakhala nazonso zokaikira, ngati inu muulola Mzimu Woyera kuti uwululire Izo kwa inu, monga mfumukazi inaenenera pokhudza za Daniele.

¹⁹² Inu mukhoza kunena, “Kodi zonse izi ziri ndi chochita chanji ndi kupereka mathokozo? Kodi inu mukulankhula za chiani, M'bale Branham? Ndi iyi pano, kotala tu naini. Inu simunanene kalikonse kokhudza kupereka mathokozo.” Uthenga wakewo wa nthawi, kwa ine! Inde, ndithudi.

¹⁹³ Makolo a paulendo anali othokoza kwambiri chifukwa cha njira yawo yatsopano yomwe anaipeza, pokhala atalekanitsidwa kwa zipembedzo zakale za Angelezi ndi tizikhulupiriro. Iwo anakwatiwa ndi Mawu atsopano, odzozedwa a m'badwo wawo; ndiko kulondola, Mawu atsopano, odzozedwa a m'badwo wawo, a tsiku lawo.

¹⁹⁴ Kotero ifenso tikhoza kukhala othokoza kwambiri, monga apaulendo, monga Abrahamu, kudzilekanitsa tokha ku zinthu za mdziko, zonse zoyanjana nazo zathu. Abrahamu

anali wapaulendo. Mulungu watilekanitsa ife kuchokera ku zipembedzo zakufa zonse. Ine ndikuyankhula kwa fuko lonseli tsopano, tizikhulupiriro tonse takufato. Ndi kupita kuti? Watilekanitsa ife, ndipo watsegulira kwa ife dziko latsopano, Uthenga watsopano wa tsiku lino.

¹⁹⁵ Chipentekoste chaumapo ndipo chafa, monga Lutera, Wesile, ndi onse a iwo. Sizerinso gulu la mipingo ikukokera palimodzi. Anthu abwino ali mmenemo, komabe, ayenera kuti atulukemo.

¹⁹⁶ Kodi Iye anachita chiani? Iye anazitsegula Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri za Uthenga wotsiriza. Inu mukuzindikira zimenezo? Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri, zomwe, zinsinsi zonse za mibadwo ya mpingo isanu ndi iwiri zinasindikizidwa ndi Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri. Okonzanso analibe nthawi yoti achite izo mu masiku awo. Iwo sanakhale moyo wotalika wokwanira. Koma vumbulutso lodala ili la Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri, ilo latsegulira kwa ife mu masiku otsiriza ano, kuchokera ku uneneri umene unachitika mu Arizona.

¹⁹⁷ Momwe ine ndinamufunsira Mulungu, tsiku lina, “Kodi Inu mukuchita chiani ndi ine kunjja kuno mu chipululu ichi?”

¹⁹⁸ Kodi inu mumadziwa kuti Mose analemba Chipangano Chatsopano...kapena Chipangano Chakale? Iye ndithudi anatero. Mabuku anai oyambirirawo amapereka malamulo, chirichonse; Genesis, Eksodo, Levitiko, ndi Deoteronomie. Iye analemba Chipangano Chakale. Kuti achite izo, iye anachita kuwasiya onse oyanjana nawo ndi owakonda ake, ndi kupita ku chipululu.

¹⁹⁹ Paulo analemba Chipangano Chatsopano. Uko nkulondola. Iye analemba Aroma, ndi Aroma ndi ena onse a Iwo uko, Ahebrini ndi Timoteo, ndi ena otero. Ndipo kuti achite izo, iye anachita kudzipatula yekha, ndi kupita uko mu Arabia, mu chipululu, kwa zaka zitatu, kukapeza vumbulutso la Mulungu.

²⁰⁰ “O,” inu mukuti, “nanga bwanji Mateyu, Marko, Luka, ndi Yohane?” Iwo anali alembi omwe ankangolembe zomwe Yesu ankazichita.

²⁰¹ Paulo anadzipatula, anawaika Mawu palimodzi. Ndiko kulondola. Chabwino, ndiye, onani, ngati izo zinatengera izo, ndipo anachita kupita ku chipululu, kutali ndi owakonda awo.

²⁰² Mukukumbukira kuti, *Ndi Nthawi Yanji Ino, Bwana?* Ndi angati anayamba amvapo izo? Itini, “Ameni.” [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Kodi izo zinali ndendende zolondola? [“Ameni.”] Ndiye ife tiri nalo vumbulutso mu masiku otsiriza ano, la Uthenga wa Ambuye Mulungu kuti asonkhanitsire Mkwatibwi Wake palimodzi. Palibe m’badwo wina womwe izo zinalonjezedwa. Izo zinalonjezedwa mu m’badwo uno: Malaki 4, Luka 17:30, Yohane Woyera 14:12, Yoweli 2:38.

Malonjezo amenewo ali ndendende basi monga Yohane M^obatizi anadzizindikiritsira yekha mu Lembu.

²⁰³ Yesu anadzizindikiritsa Yekha. Kodi iwo ananena chiani? “Talikiranani naye munthu wotereyu!” “Yohane ndi munthu wakuthengo.” Mpingo sunali wokhoza kuti uzilandire izo. Iyo ndi ndondomeko yake. Ngakhalenso mpingo suzilandira izo lero.

²⁰⁴ Koma, kwa Osankhidwa, Mulungu akuitanira kwa Osankhidwa. Iwo akudziwa izo: akumuitana Mkwatibwi waukoma, Mawu, Mpingo wa tsiku lotsiriza, Dona wosankhidwa wa Ambuye wathu Yesu Khristu, Mawu. Ngati... Yesu ndi Mawu. Ndi angati akukhulupirira izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Chabwino. Ndiye, Mkwatibwi nthawizonse ali gawo la Mkwati, koteri Mkwatibwi sadzakhala ali chipembedzo. Iye ayenera kukhala ali Mawu, akuwonetseredwa, kuti akhale Mkwatibwi wa Khristu. Iye analonjeza kuti adzachita izo. Iye ananena momwe Iye akanadzachitira izo. Samagwiritsa ntchito konse...kutaya ndondomeko Yake. Iye nthawizonse ankazichita izo mwa ndondomekoyo. Iye anachita izo, nthawi iliyonse, mwa ndondomeko. Iye akuzichita izo kachiwiri, kumuitana Mkwatibwi Wake waukoma kuti atuluke alowe mu tsiku lotsirizali, Rebekah wokondeka akumuyembekezera Isaki Wake. Ndi nthawi yokongola bwanji!

²⁰⁵ Apa izo zikubweretsa powonekera, mabuku awiri omwe ati akhale achinsinsi kwa inu pamene inu muziwerenga bukhu la *Mibadwo Isanu ndi iwiri ya Mpingo*. Mabuku awiri: bukhu la moyo, akuti, ena amati iwe ukhoza kulembetsa dzina lako, iwe sumachokamo; wina amati umalichotsapo dzina lake pa Bukhu la Moyo. Ili likuzibweretsa izo powonekera mwangwiro, pomwe pano. Ine ndiima maminiti pang’ono, mwinamwake, pa zozilemba zingapo apa, ndi kuzigwira izi ife tisanatseke.

²⁰⁶ Moyo ndi chinthu chopatulika, kwa Mulungu, ndipo iwo unalembedwa mu bukhu. Mulungu ndi mwini wa moyo. Kodi inu mukukhulupirira izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

²⁰⁷ Moyo wathu wachibadwa kuno, ife tiri nawowu, ndi chopotozedwa chabe. Iwo umayenera kwenikweni kuti ukhale moyo woyenera, pakuyamba pomwe, koma iwo unapotozedwa ndi kubadwa kwachilengedwe. Moyo woyamba, kapena chilumikizano chanu choyamba, inu munalumikizidwira umo pa kubadwa, mwa chilengedwe, kuchita kwa chilengedwe. Munthu wokhalapo wachilengedwe atayanjana, mwamuna ndi mkazi palimodzi, atayanjana palimodzi mu kachitidwe ka kugonana, zomwe zinaubweretsa moyo wanu woyamba kuno, ndipo umenewo ndi woyanjana nalo tchimo ndi imfa. Inu mungakhoze bwanji kuphonya kuiwona mbewu ya serpenti?

²⁰⁸ Pamene inu mukumuwona mkazi, chochokera mwa china; palibe chachikazi china chonga iye; chinapangidwa mwa

dongosolo limenelo, podziwa kuti iye akanakhoza kunyengedwa. Mulungu ankadziwa. Ngati Iye akanati asadziwe mapeto kuchokera ku chiyambi, ndiye Iye sanali Mulungu. Ngati Iye sali wopanda malire, ngati Iye sali . . . Ndipo Iye sangakhoze kukhala wopandamalire popanda kukhala wodziwazonse, wopezeka paliponse, wodziwa zinthu zonse, Wamuyaya. Kotero Iye ankadziwa zinthu zonse, ndipo Iye ankayenera kuti amupange mkazi ameneyo.

²⁰⁹ Mwamunayo analibe mkazi. Mkazi ndi mwamuna anali chinthu chomwecho. Iye anali ndi mzimu wachikazi ndi wachimuna mwa iyeyekha.

²¹⁰ Iye anachita kulekanitsa, anatenga chochokera mwa china, atatha kupanga chirengedwe chonse. Palibe chachikazi chimene chinalengedwa ndi Mulungu, mu kulenga koyamba, chingakhoze kuchita chinthu monga choncho. Iye anapangidwa motero, kuti azichita izo. Iye ankadziwa kuti mkaziyo akanadzachita izo. Ngati Iye akanati asatero, Iye sanali Mulungu.

²¹¹ Koma, taonani, zikhumbo zomwe ziri mwa Mulungu zinkayenera kuti ziwonetseredwe. I—Iye anali woti adzakhale Mpulumutsi. Ndipo kuti apange chirichonse mwangwiro, momwe Iye analiri nazo izo, ndiye sipakanadzakhala kanthu kena komwe kakanadzatayika. O, musati mukhale ana. Khalani amuna ndi akazi. Ife tiri pamapeto a msewu. Zindikirani.

²¹² Tsopano, icho chinali chilengedwe, choyanjana ndi imfa. Mwamuna wanu woyamba, yemwe anali ndi ulamuliro pa inu, chinali chilengedwe chanu mwa kubadwa kwa chilengedwe. Mwachilengedwe, inu mumalikonda dziko chifukwa ndinu dziko, ndi gawo la dziko. Uko nkulondola? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi] Zokhumba zanu zinali, mwa chilengedwe kuti, muzilikonda dziko lomwe inu muli gawo lake. Ndinu gawo la chirengedwe. Inu mukukhulupirira izo? [“Ameni.”] Ndipo icho ndi chinthu chanu chachilengedwe.

²¹³ Ndicho chifukwa inu mumayenera kuti mubadwe kachiwiri. Inu mumayenera kuti mudzilekanitse; inu mumayenera kuti mufe kwa mwamuna woyamba uyo. Inu simungakhoze kumakhala moyo ndi iye. Inu simungakhoze kungonena, “Chabwino, ine ndimusudzula iye, ndi kumupachika iye pamwamba apa kwa kanthawi.” Ayi, bwana. Palibe kulemba kwa chisudzulo! Iye amafa. Chikhalidwe cha chidziko chiyenera kuti chife. Gawo lililonse la iye liyenera kuti life. Inu muyenera kuti mulumikizidwenso, kachiwiri, ndi Chilengedwe china.

²¹⁴ Dzina lanu la chilengedwe choyamba, chinabadwa, ndipo chinaikidwa mu bukhu la moyo. Ntchito zanu zonse zinalembedwa mmenemo, nazonso. Chirichonse chomwe inu munachichita pansu pa chilengedwe chimenecho chinaikidwa mu bukhu, lotchedwa bukhu la moyo.

215 Inu mukuzindikira, mu Daniele, pamene iye anabwera kwa “Wa Masiku Amakezana, Yemwe tsitsi lake linali loyera ngati ubweya. Zikwi khumi kuphatikiza zikwi khumi anadza ndi Iye, kudzatumikira kwa Iye; m—Mkwatibwi. Ndiyeno mabuku anatsegulidwa.” “Ndipo Bukhu lina linatsegulidwa, lomwe linali Bukhu la Moyo.” Mwaona? Uko kuli oyera kale kumeneko, Mpingo, Mkwatibwi. “Bukhu lina linatsegulidwa, lomwe linali Bukhu la Moyo.”

216 Tsopano, inu, koma pamene inu munalekanitsidwa kwa chilumikizano icho, ndi imfa yauzimu. Chikhumbo chanu chachilengedwe nkuti muzidula tsitsi lanu. Chikhumbo chanu chachilengedwe nkuti muzivala zazifupi, kulocha nkhope zanu. Chikhumbo chanu chachilengedwe nkuti mukhale waluntha, munthu wanzeru, wodziwa chinachake bwinoko kuposa ena. Ndicho chimene Eva ankafuna. Ndicho chinthu chomwe chimene iye ankachifuna.

217 “Chabwino, mukuti! Iwe wamng’ono kwambiri pawiri, mlaliki wa thuu-bai-foro, ukuima apo ndi kumandiiza ine? Ine ndiri nayo Ph.D., LL.” Izo zimangokupangitsani inu kutalikira kwambiri ndi Mulungu, nthawi iliyonse yomwe inu mumawonjezera chinthu chimodzicho. Mwaona? Mwaona? Ndiko kulondola. Ndi zoon. Mwaona?

218 Ndicho chomwe Eva anatenga. Iye anapatsidwa pakati ndi mtundu uwo wa kupereka pakati. Ndicho chomwe mpingo uli lero, mwa masukulu a Baibulo ndi zaluntha. Ndipo, taonani, aliyense akutsutsana ndi winayo, nyansi zazikulu chimodzimidzi basi zomwe Baibulo linanena, “Babeloni.”

219 Mkwatibwi akudziwa pamene Iye waima. Iye ndi apang’ono kwambiri. Sipadzakhala ambiri ati adzapulumutsidwe; apang’ono basi, kwambiri, mbiri. Inu mukuti, “Chabwino, apo, anati, ‘zikwi.’” Inde. Koma iwo abwerapo kudutsa mu zaka zikwi ziwiri, nawonso, pa m’badwo uliwonse umene Iwo anatulukamo. Uliwonse . . .

220 M’badwo wa Lutera ndi gulu limenelo; ndiyeno anafamo, ndipo iwo anapita, anapanga chipembedzo; ndiye Wesile; nayeno kunabwera achipentekoste, ndi zina zotero. Nthambi zonse zazing’ono zotulukirapo za Chibaptisti, Chipresbateria, Chimethodisti, Chinazerini, Pilgrim Holiness, ndi zina zotero, onani, zonse izo zinapanga nthambi kuchokera apo monga tsamba.

221 Koma, kumbukirani, pamene iyo inapita pansu; ndipo njereyo inayamba kucha. Inu mupeza, njere imeneyo isanache, chirichonse mu phesi limenelo chimayenera kukhala chitafa. Aleluya! Kodi inu simukukhoza kuwona pamene ife taima? Moyo uli mu njere kachiwiri. Ndi chiani icho? Ndendende basi monga njere yomwe ija imene inapita mu nthaka, Yesu yemwe uja mu mawonekedwe a Mkwatibwi, mphamvu

yomweyo, Mpingo womwewo, chinthu chomwecho, Mawu omwewo. Mawu omwewo anakokedwera mmwamba kudutsa mu izi ndi kudzatulukira apa, ndi kudzabwera ku mutuwu apa. Ndipo Moyo wonse uwo umene unabwera podutsa apa, unawatengapo anthu ake. Tsopano iwo ukuwumbika ku mutuwo, wa ku Mkwatulo. Ndidzayankhula pa izo mawa usiku, kapena usiku wotsatira, wina, Ambuye akalola.

²²² Chabwino, inu munalekanitsidwa ku chilumikizano chanu choyamba, mwa imfa yauzimu. Tsopano inu mwabadwa kachiwiri, kapena mwakwatiwanso kachiwiri, ku chilumikizano chazimu chatsopano; osati cha moyo wanu chilengedwe cha zinthu za mdziko, koma wa Moyo Wamuyaya. Nyongolosi iyo yomwe inali mwa inu pachiyambi, inakupezani inu.

²²³ Tsopano, bukhu lanu lakale lapita, ndi chilumikizano chanu chakale. Tsopano, dzina lanu mu lakale lanu, mu lanu... lasamutsidwamo. Tsopano, inu mukuti, “Kodi inu mukutanthauza kuti mudiuze ine kuti bukhu langa lakale...” Mulungu analiyika ilo mu Nyanja ya Kuiwala Lake. Inu mukuima mwangwirowo pamaso pa Mulungu.

²²⁴ Tsopano, dzina lanu pano liri mu Bukhu latsopano; osati bukhu la moyo, koma Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa, omwe Mwanawankhosa anawawombola. Osati bukhu lakale la kulumikizana kwanu kwa chilengedwe, koma kwanu kwatsopano, Mkwatibwi. Aleluya! Moyo wanu watsopano uli mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa, chikalata chanu cha chikwati, aleluya, komwe nyongolosi yanu yowona Yamuyaya, kuchokera pachiyambi, imagwirako. Tsopano inu simunali okhululukidwa kokha, koma inu muli olungamitsidwa. Ulemerero! “Olungamitsidwa,” Aroma 5:1 anati. Eya. Aroma 5:1 anati, “Chotero pokhala olungamitsidwa mwa chikhulupiro.”

²²⁵ Tayang’anani pa mawuwo. Mawuwo sakutanthauza kukhululukidwa. Mawuwo akutanthauza kulungamitsidwa. Iwo sakutanthauza kuti iwe wakhululukidwa.

²²⁶ Mwachitsanzo, inu mutamva kuti ine nditaledzera n—ndipo ndimachita zinthu zina zoipa, ndi chirichonse. Ndiye inu nkubwera apo, nkudzanena ndi ine. Inu nkudzapeza kuti ine sindinachite izo, ndiye inu nkubwera apo, nkuti, “M’bale Branham, ine ndakukhululukirani inu.” Mwandikhululukira ine? Ine sindinazichite izo, pa kuyamba pomwe. Mwaona?

²²⁷ Tsopano, ngati ine ndinazichita izo, ndine wolakwa. Koma inu mukhoza kundikhululukira ine, ndipo ine sindikanakhala wochimwa. Komabe ine sindili wolungamitsidwa, chifukwa ine ndinachichita kumene icho.

²²⁸ Koma mawu oti, *kulungamitsidwa*, ali ngati kuti iwe sunazichite konse izo. Amen. Izo siziri kuwerengedwa ngakhale, konse. Zachitika motani? Mu Bukhu la Mulungu la Nyanja ya Kuyiwalira, bukhu lanu lakale ndi chikwati

chasudzulidwa ndipo nchakufa. Izo siziri ngakhale mu zokumbukira za Mulungu. Amen. Inu muli olungamitsidwa. “Chotero pokhala olungamitsidwa.” Izo zinali kutsutsidwa. Inu munali kutsutsidwa. Inu simunazichite konse izo, mu malo oyambirira omwe. Chilumikizano chakale chiri mu Nyanja ya Mulungu ya Kwiwala. Inu simunakwatitsidwe kwa izo, pa kuyamba pomwe. Iye, Mkwati, ananyamula manyazi anu, Iyemwini, chifukwa cha inu, mmalo mwanu. Iye anatenga malo anu, pakuti inu munakonzedweratu kwa Iye, kuti mudzakhale mwa Mkwatibwi Wake, asanaikidwe maziko a dziko. Baibulo linanena chomwecho. Inu ndinu Mbewu yokonzedweratu.

229 Kodi inu munafika chotani pomachita izi? Inu munanyengedwera mu izo ndi chikwati chanu choyamba, kwa kholo lanu lachigololo, Eva. Iko si kulakwitsa kwanu kwanu. Mwa kubadwa kwanu kwa chilengedwe, inu munabwera motsatira Eva, yemwe anachita chigololo. Ndicho chifukwa inu munabadwira mu chigololo. Ndinu wochimwa, pa kuyamba pomwe. Ndiko kulondola. Inu munanyengedwera mu izo. Inu munalibe . . . Ayi, inu, ilo silinali vuto lanu.

230 Inu simunazichite konse izo. Chifukwa, nyongolosi yaing’ono iyo yomwe inali mwa inu, inali yoti idzakhale inu, asanaikidwe maziko a dziko. Mulungu anaika dzina lanu mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa.

231 Monga nkhani yanga yaing’ono ya mphungu, nonse inu munaimva iyo. Nkhuku. . . Mlimi wachikulire anaika—nkhuku, nthawi ina. Kotero iye analibe nkhuu zokwanira uko. . . mazira oti akhale pansu pa nkhuu. Kotero ndiye iye anakapeza dzira la mphungu, ndipo iwo anakaliyika ilo pansu pa iyo. Pamene mphungu inabadwa, iyo inali nkhuu yowoneka-moseketsa yomwe nkhuu izo zinayamba zaiwonapo, mphungu yaing’ono yakaleyo ikupita limodzi. Ndipo nkhuu zinkati, “Kuluku, kuluku, kuluku, kuluku.”

232 Mphungu yaing’ono inkati, “Ine sindikudziwa momwe chinthu icho chikumvekera, koma ine ndikumutsatira iye, mulimonse.”

233 Ndipo izo zinapita kunja kwa kholalo ndi kukayamba kupalasa pa mulu wa manyowa. Ndipo iyo, “Kuluku, kuluku, kuluku. Izi ndi zabwino. Izi ndi zabwino. Inu dzajowinini chathuchi. Ndipo izi ndi zomwe. . .”

234 Mphungu yaing’ono yakaleyo, iyo siinkakhoza kuzidya zinthu zimenezo. Mwaona? Iyo basi—iyo inkangopitira limodzi ndi nkhuu chifukwa iyo siinkadziwa. Iyo siinkadziwa choti ichite. Ndiyeno iyo inkapita kunja uko, ndipo iyo inkakhoza kutola *ichi* kapena *icho*. Mphungu yaing’ono yaing’ono basi. . . iyo inkayenera basi kuti izimeze izo, koma i—iyo siinkadziwa momwe ikanamachitira izo. Koma iyo inali itawona zonse

zomwe nkhekuzo zinkachita, koma pali chinachake chosiyana. Iyo siinkazikonda izo.

²³⁵ Kotero, tsiku lina, mayiyo anadziwa kuti iye anali atayikira mazira awiri. Kotero iye anayamba kukalisaka limodzi lina lija, kuwuluka mozungulira, akufunafuna, monga Mzimu Woyera waukulu. Tsiku lina iye anawulukira pamwamba pa khola, chipembedzo chija. Iye anayang'ana pansi apo, ndipo iye anamuwona mwana wake. Iye anafuula. Ilo linali Liwu la chinachake lomwe linkamvekera kuchokera mkati mwake. [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] O, Izo zikumveka bwino! O! Mulole nyongolosi yokonzedweratu yeniyeni, yobadwa ndi Mulungu, iwamve Mawu a Mulungu, Iyo ndi nyimbo kwa iye. Iyo imadziwa kuti Icho ndi Choonadi.

²³⁶ Iye watopa nazo zinthu za chipembedzo izo, mulimonse, “Dzati jowine ife. Bwera, uzipita ndi ife. Ife tikakhala ndi phwando lachitukuko. Ife tiri ndi *izi*. Ife tiri. . .” Izo basi sizinali kumveka bwino, kwa kanthu kakang'onoko.

²³⁷ Iye anati, “Mwananga, iwe si wa mu gulu limenelo, mulimonse. Iwe ndi wa ine. Ndiwe wanga.”

²³⁸ Iye anati, “Amayi, izo zikumveka zenizeni. Ine ndichokako bwanji?”

²³⁹ “Ingopanga kulumpha. Ine ndikugwira iwe.” U-nhu. Ndizo zonse zomwe iwe ukuyenera kuzichita.

²⁴⁰ Mawu odzozedwa a Mulungu ali kutsimikiziridwa pamaso pa munthu aliyense yemwe anabadwa kuti akhale mwana wa Mulungu, ndi nyongolosi yokonzedweratu mwa iye ya ku ora lino, iye adzawuona Uthenga wa Mulungu motsimikiza basi momwe aliripo Mulungu Kumwamba. Marteni Lutera anawaona Iwo kwa ake. Wesile anawaona Iwo kwa ake. Achipentekoste anawawona Iwo kwa ake. Tsopano nanga bwanji inu? Mwaona? Iwo anapita mu chipembedzo. Pano pali Mawu akuzitsutsa izo; akukuuzani inu zomwe ife tikuyenera kuti tikhale nazo lero, ndipo ziri ndendende basi Malaki 4 ndi malonjezano onse awa a ku orali. Kodi inu mukuona chiani? Kodi inu mukuyang'ana pa chiani? Ameni. Ndife tiri pano. Mphungu zenizeni, zoonza zimamva. “Nkhosa Zanga zimawadziwa Mawu Anga. Mlendo sizingamutsatire.”

²⁴¹ Bwanji? Izo zinaikidwa mmenemo mwa kukonzedweratu. Inu munadzozedweratu kudzakhala mwana wa Mulungu. Inu munali mwa Mulungu asanaikidwe maziko a dziko. Inu mukungowonetseredwa mu tsiku lino kwa ulemu ndi ulemurero Wake. Kodi inu mungachite motani izo popanda kulemekeza Mawu Ake, ndi kuima ndi Mawu aliwonse a Mulungu? Inde, bwana. Chomwe, inu muli gawo la Mawu amenewo, mwa kukonzedweratu. Chifukwa, taonani, Mulungu ndi Mawu. Inu mukukhulupirira izi? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Chabwino, ndiye, ngati. . . Iye nthawizonse anali Mawu.

“Pachiyambi panali Mawu.” Ndipo ngati Mawu anali Mulungu, ndiye inu munali mwa Mulungu. Mawu, gawo lomwe inu muli woti mulisewere, linali mwa Mulungu asanaikidwe maziko a dziko. Iye anakuwonani inu. Iye anakudziwani inu. Iye anakukonzereranitu inu kwa izo.

²⁴² Ine ndikukuuzani inu, chimodzimodzi monga mphungu ija inalizindikirira liwu lija, chomwechonso amachita Mkristu w—weniweni, wobadwa-kachiwiri amalizindikira Liwu la Mulungu likamalankhula kupyolera mu Mawu, pamene iwo awaona Iwo akudzozedwa ndi kutsimikiziridwa. Taonani. Iye anayang’ana pamwamba Apo. Iye sanaiwone nkuku yokalamba iyi ikuchita kuluku-kuluku kuzungulira *apa*, “Tijowineni ife ndi kumapita *kuno*. Ndi kumapita *uku*, ndi kumapita kwa *ichi* ndi *icho*.” Iye anawona—chinthu chonga chomwe iye ankafuna kuti akhale ali, chikuyandama mu mlengalenga, chikufuula, mfulu, mmwamba umo patali, pamwamba pa miimba yonse ndi zinthu za mdziko lapansi. Alaluya! Iye ankafuna kuti akhale wotero chifukwa izo zinali mwa iye kuti akhale wotero.

²⁴³ Ndipo munthu yemwe ali wobadwa ndi Mulungu, mwana wa Mulungu, ayenera kumakhala ndi chikhalidwe cha Mulungu. Iye ayenera kumakhala monga Mulungu. Iye amamulemekeza Mulungu. Iye ali gawo la Mawu a Mulungu. Ndipo mu masiku otsiriza ano, a Mkwatibwi uyu akutenga mawonekedwe, ndendende basi mphamvu yomweyo yomwe Iye anali pachiyambi, yabwera kudutsa mu mabungwe awa, ndi zina zotero, ndi kutulukira kwa Mkwatibwi. Iye sangakhoze kukhala chinachakenso koma chimenecho.

²⁴⁴ Iwo ankayenera kuti achiwone Icho, Ayuda aja mu masiku awo, pamene iwo anachiwona Icho chikuwonetseredwa pamaso pawo, momwe mneneri ananenera kuti Iye anali. Iye anati, “Kafufuzeni Malemba; mwa Iwo inu mumaganiza kuti muli nawo Moyo Wamuyaya. Iwo ali Iwo omwe amachitira umboni za Ine. Ngati Ine sindikuchita ntchito za Atate Anga, musati mundikhulupirire Ine. Koma ngakhale inu simungati mundikhulupirire Ine, zikhulupirirani ntchito zomwe Ine ndazichita.”

²⁴⁵ Iwo anati, “Makolo athu ankadya mana mu chipululu kwa zaka forte. Ife tikudziwa pamene ife tiri.”

²⁴⁶ Iye anati, “Ndipo iwo aliyense wa iwo ali okufa,” ndiko, kulekanitsidwa Kwamuyaya. Aliyense anafa. Analipo atatu okha, awiri anatuluka kuchokera mu milioni, mamilioni thuu. Ndizo mmodzi mu milioni.

²⁴⁷ Bwanji, kubaira, umuna wochokera kwa yamphongo ndi yaikazi, kawirikawiri pamakhala dzira limodzi lachonde. Pamakhala dzira limodzi, nyongolosi imodzi zomwe ziri zachonde, kodi inu munayamba mwawonapo kupanga haiburidi mu ng’ombe. Zindikirani. *Apa* pali—mazira milioni; *pano*

pali nyongolosi milioni; ndipo pamene izo—zitulutsidwa, kuti zibwere limodzi mu chiberekero, kubwera nizidutsa mu kathumbo ndi kudzalowa mu chiberekero, izo zimakomana. China cha izo ndi mazira. Mazira milioni; nyongolosi milioni. Pali dzira limodzi lokha mmenemo lachonde. Pali nyongolosi imodzi yokha yachonde. Zonsezo ziri moyo. Inu mukhoza kutiwona tiana ta ng'ombe ito tikugundana cha mmenemo, kadhonthe komwe inu mungakhoze kukaika pa mtengo wa machesi.

²⁴⁸ Ndipo Demos ndi iwo akumvetsera usikuuno, ndipo iye akukumbukira pamene ife tinazitenga izo. Iye ananditengera ine kumusi uko, anakandisonyeza ine momwe izo zimagwirira ntchito. Machubu oyeseramo, ndipo anayika zongokwanira zomwe inu mungakhoze kuziyika pa mapeto a machesi. Zimenezo zinali zikwi za ting'ombe tating'ono tatikazi ndi nkHUDZI mmenemo, koma imodzi yokha ya izo ndi yomwe ingakhoze kukhala moyo. Imodzi yokha ya izo! Ndipo pano pali mpira waukulu wa izo, *apa*. Ndipo inu muzindikira, imodzi ikwawa kuchokera pakati pa awa *apa*, kupita pamwamba pakepo, nyongolosiyo nkubwera cha *apa*; ndipo dziralo nkubwera kuchokera pakati pa mazira ena awa *apa*, ndipo izo nkukomana limodzi. Ndipo zina zonsezo zimafa. Komabe, izo nza moyo, koma izo zimafa.

²⁴⁹ Chifukwa, pali Chinachake, Winawake analipanga limodzi *ili* kukhala lachonde, ndi kuidzoza *iyi*, nayonso. Ndi kukonzedweratu, m'bale wanga. Zedi. Mulungu amayenera kutsimikizira ngati ati akhale mnyamata kapena mtsikana, wa mutu-wofiira, wa mutu-wakuda, kapena chirichonse chomwe chiri. Izo zimatsimikizidwira ndi Mulungu. Nchinsinsi chochuluka kuposa kubadwa kuchokera kwa namwali, kwa ine. Koma, zindikirani, zina zonsezo zimafa.

²⁵⁰ Analipo anthu thuu milioni anatuluka, ankaimba, ankafuula, ankachita chirichonse. Ankayankhula mu... sanayankhulepo konse mmalirime. Koma iwo anafuula, n—ndipo ankamupatsa Mulungu ulemerero, ndipo anavina chokwera-ndi-chotsika ndi nyanja, ndipo anachita chirichonse chomwe ena onse a iwo anachichita, koma analipo awiri okha omwe anakalowa mu dziko lolonjezedwa. Kalebu anakalowamo, Kalebu ndi Yoswa, awiri okha. Ndiwo mmodzi pa milioni. Ndi mmodzi kuchokera pa milioni mu kubadwa kwa chilengedwe. Mmodzi aliyense wa iwo anali ndi dalitso lomwelo.

O, inu Achipentekoste, ine ndikuyembekeza inu simudzuka mochedwa kwambiri.

²⁵¹ Mmodzi pa milioni. Taonani. Pakuyenera kuti alipo faifi handiredi milioni otchedwa Akhristu mu dziko lero. Ngati Yesu angabwere, angakhalepo faifi handiredi okha oti apite ndi Iye, ndiye, ngati kuwerengera uko kukanakhala koyendera mowona.

Pakuti, pali ambiri kuposa awo akumasowa tsiku lililonse, mu dzikoli. Iwo samadziwa kanthu za izo.

²⁵² “Ine ndamvetsedwa,’ anatero alembi, ‘inu mukudziwa kuti . . .’ Bwanji alembi amanena ku—kuti, ‘Eliya ayenera kudza poyamba?’” Iwo anatero kwa Yesu.

²⁵³ Iye anati, “Eliya anadza kale ndipo inu simunazidziwe izo.” Mwaona? Iye anachita ndendende basi zomwe Malemba anati zikanadzachitika kwa Iye. Mwaona? “Kotero ayenera Mwana wa munthu avutike. Pansi . . .” Iwo sanamuzindikire Iye. Komabe, iwo onse anali mu mpingo. Onse ankadzinenera kuti ali moyo.

²⁵⁴ Inu mumukhazikepo Mkhristu, wobadwa kachiwiri weniweni, wantchito wa Mulungu weniweni, akamva Mawu a Mulungu awo, iye abwera kumene kudutsa mu chipembedzo chirichonse, kupita ku nthaka yachonde kwenikweni iyo, mwa Mawu, nthaka yobalirapo. Iye adzangochita izo. Ine sindikudziwa momwe iye amachitira izo. Mulungu anadzoza kuti izo zidzachitike.

²⁵⁵ Inu munanyengedwa pachiyambi, ndi chikwati chanu choyamba. Tsopano inu mukudziwa zomwe ziri zoonā. Chimodzimodzi monga ine ndinanena, mphungu yaing’ono pamene iyo inamva Liwu la Mkwati, iyo inapita kwa Ilo, Mawu a Mulungu odzozedwa, otsimikiziridwa a tsiku lotsirizali.

²⁵⁶ Nowa anali Mawu otsimikiziridwa a ku tsiku lake. Kodi inu mukukhulupirira izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Chabwino, uthenga wake sungagwire ntchito lero.

²⁵⁷ Mose anali Mawu otsimikiziridwa a ku tsiku lake. Inu mukukhulupirira izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Iwo sangagwire ntchito tsopano. Yesu anali . . .

²⁵⁸ Yohane anali Mawu otsimikiziridwa. Kodi inu mukukhulupirira izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi] Iwo sakanagwira ntchito mu nthawi ya Yesu. Ndithudi ayi. Ayi, bwana. “Malamulo ndi aneneri analipo mpaka pa Yohane; kuchokera apo, Ufumu wa Kumwamba.”

²⁵⁹ Atumwi, iwo omwe analikhazikitsa Baibulo. Apo anadza Lutera natuluka, mu kukonzanso, mawu ake, awo, mpingo wake, sungagwire ntchito lero. Wa Wesile sungati. Wa Chipentekoste sungati. Iwo unagwira ntchito mu tsiku lawo.

²⁶⁰ Koma ili ndi tsiku lina. Uku ndi kutsegula kwa Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri. Ine ndikudziwa kuti Izi zikumveka mwachirendo kwa inu, koma Mulungu wazitsimikizira izo mwangwiro kwambiri. Palibe—palibe funso mu Izo. Mwangwiro basi! Ine sindiri kumwazira izo kwa gulu lapanoli kuno. Ine ndikuyankhula kwa anthu ku fuko lonse. Mwaona? Zichitani zomwe inu mukufuna kumachita.

²⁶¹ Tsopano zindikirani Mawu odzozedwa a tsiku lake, omwe inu muli gawo lake, mwa kukonzedweratu. Inu

mwamsanga, ngati, munadziwa. Pamene inu munaumva Iwo, inu munadziwa mwamsanga kumene kuti inu munali mphungu. Inu munazindikiranso kuti inu simunali nkukhu yachipembedzo, pa kuyamba pomwe. Inu munkadziwa kuti panali chinachake cholakwika mmenemo. Pali chinachake cholakwika, ndiko kulondola, pakuti inu mukudziwa kuti inu munakoledwera umo, pachiyambipo.

²⁶² Iye, Mkwati, anawachotsa manyazi anu, “Ndipo anakawaika iwo mu Nyanja ya Kuiwala, mwa kutsuka kwa Madzi a Mawu ndi Magazi a Moyo.” Ndi zomwe Baibulo linanena. Mwamuna wanu woyamba yemwe inu munakwatiwa naye, dziko; Mkwati wodzowedwa, yemwe anakudzozeranitu inu, wakutsukani inu mwa kutsuka kwa Madzi. Mwa “mpingo”? [Osonkhana ati, “Ayi.”—Mkonzi.] Izo sizikumveka bwino. Sichoncho izo? [“Ayi.”] Inu mukhoza kuzipeza izo mu almanac, koma osati mu Baibulo la Mulungu. “Mwa kutsuka kwa Madzi mwa Mawu.” Mu Mawu! Mwaona? Mwa . . .

²⁶³ Inu mukuima olungamitsidwa kwathunthu, ngati kuti inu simunazichitepo izo pachiyambi. Uwu ndi Uthenga wanga kwa Mpingo tsopano. Pamene inu . . . pamene ife tizichoka pa kuulutsa, mu miniti yokha. Inu mukuima, ngati inu mukuima pa Mawu a Mulungu ndi Mawu a Mulungu, ameni aliyense, dontho lirilonse, kanusu kalikonse. Inu mwaima pati? Ine ndikuyesera kukuuzani inu, kanganukani nkuchoka mu mankhusu awo. Ndipo dzaloweni umu mu tirigu, komwe inu mungakhoze kucha pamaso pa Mwana. Ine ndikumva kubwera kwa chokolola. Inu mwaima olungamitsidwa kwathunthu, ngati kuti inu simunazichitepo izo pa malo oyambirira. Aleluya!

²⁶⁴ Mukayankhula za kupereka mathokoza! Ine ndikumverera bwino kwenikweni. Ndine wothokoza kwambiri chifukwa cha izo kuposa chirichonse chomwe ine ndikuchidziwa.

²⁶⁵ Inu ndinu Mkwatibwi wangwirowo, waukoma, wopanda tchimo wa Mwana wa Mulungu wamoyo. Mwamuna ndi mkazi aliyense yemwe ali wobadwa ndi Mzimu wa Mulungu, ndi wotsukidwa m’Magazi a Yesu Khristu, ndi kumakhulupirira Mawu aliwonse a Mulungu, mukuima ngati kuti simunachimwepo pa malo oyambirira. Inu ndinu angwirowo. Magazi a Yesu Khristu! Inu mungakhoze bwanji . . . Ngati munthu . . .

²⁶⁶ Ngati ine ndimayenera kuti ndife mmawa, munthu nkutenga malo anga, ine sindingakhoze kufa chifukwa cha tchimo limenelo. Winawake anatenga malo anga.

²⁶⁷ Ndipo Yesu, Mawu, anatenga malo anga. Iye anadzakhala ine, kuti wochimwa, kuti ine ndikhoze kukhala Iye, Mawu. Ameni. Ndisiyeni ine ndigwire mowona kwa Iwo, osati mpingo. Mawu! Ameni.

268 O, chilumikizano chauzimu chija cha Khristu ndi Mpingo Wake tsopano, pamene mnofu ukusandulika Mawu, ndipo Mawu akusandulika mnofu, kuwonetseredwa, kutsimikiziridwa. Basi zomwe Baibulo linati zikanadzachitika mu tsiku lino, izo zikuchitika, tsiku ndi tsiku. Bwanji, izo zikuwunjikana mofulumira kwambiri kunjira uko, mu zipululu izo, ndi zinthu zomwe zikuchitika, mokuti ine sindingakhoze ngakhale kuyendera limodzi nazo izo. Iye tayandikira Kudza kwa Yesu, kuti alumikizane ndi Mpingo Wake, komwe Mawu akusandulika Mawu. Kuitana kwa Mzimu Woyera, ukufufuza mitima!

269 Inu mukuima, amphumphu. Inu simunayambe mwachimwapo pa malo oyambirira. Mulungu sakuzidziwa nkomwe. Izo ziri mu Nyanja ya Kuiwala. Inu simunazichite izo konse. Inu munkaneneredwa nazo izo, ndi wotinenerayo. Koma kwenikweni, kuchokera pachiyambi, inu munakonzedweratu kuti mudzakhale mwana wamwamuna ndi wamkazi wa Mulungu. Inu mwaima apo, otsukidwa. Ndipo bukhu lanu lakale la chisudzulo laikidwa kumbali, ndipo ilo ndi lakufa, mwamtheradi mosadzapezekanso, ngakhale mu malingaliro a Mulungu.

270 Ndinu Mkwatibwi waukoma wa Khristu, wotsukidwa mu Magazi a Khristu. Mwana wa Mulungu wofunika, waukoma, wopanda tchimo akuima ndi Mawu a Mkwatibwi angwiwo, osaipitsidwa kuti Iye anamutsuka ndi Madzi a Magazi Ake Omwe; yemwe anasandulika thupi ndi kuwonetseredwa, kuti Iye akhoze kukutengani inu omwe munakonzedweratu mu chifuwa cha Atate, chisanayambe, chimodzimodzi monga Iye anali. Iye analiri chikhumbo chachikulu chija cha Mulungu, chotchchedwa “chikondi.”

271 Chirichonse chomwe inu muli, inu ndinu antchito a Mulungu, chirichonse chimene Mulungu akufuna kuti inu muzichita, komwe malo anu ali. “Mulungu anaika mu Mpingo, ena atumwi, aneneri, aphunzitsi, abusa . . .” Iye anaika izo mwa ukoma wa kukonzedweratu Kwake Komwe. Ndipo inu munali chimenecho, pakuyamba pomwe.

272 Chikwati chanu choyamba chinathetsedwa. Icho chinali. Inu simunachichite icho konse, pa malo oyambirira. Chifukwa, pali chinthu chimodzi chokha chomwe chingakhoze kuchita izo, icho chikanakhala Mulungu kutsika, Mwiniwake, ndi kutenga malo anu mu mawonekedwe a Mwana wa Mulungu, Yesu Khristu, ndipo anakutsukani inu ndi Madzi, pakutsuka kwa Madzi mwa Mawu. Mawu; osati chipembedzo! Mawu anakutsukani inu. Koma ngati inu simuima mu Madzi a Mawu, inu mudzatsukidwa chotani? Inu mukadali ndi banga monga Eva anali.

O, Mwanawankhosa wakufa, Magazi Anu ofunika

Sadzataya konse mphamvu Yake,

Mpaka Mpingo wonse wolipidwira dipo wa
Mulungu

Ukhale utapulumsidwa kuti usadzachimwe
kenanso.

²⁷³ Kodi tchimo ndi chiani? *Tchimo* ndi “kusakhulupirira.” Kusakhulupirira mu (chiani?) Mawu; kusakhulupirira mwa Mulungu, yemwe ali Mawu.

²⁷⁴ Angwiro, osaipitsidwa; o, aleluya; tizichoka posachedwapa waku mlengalenga; ameni; tikuima okonzeka. Taganizani. Zovala zanu, zitatsukidwa ndi Madzi a Mawu owukha magazi! Mawu anakhala Magazi. Mawu anakuukhirani inu, ndipo inu mwatsukidwa mu Mawu owukha. Mawu, kuwukha! Moyo wa Mulungu mu Mawu, ndipo Mawu anaukhitsidwira kwa inu, kuti mukhoze kukhala otsukidwa ku nyansi za aziwerewere awa, ndi kukhala otsukidwa ndi oyeretsedwa mwa kutsuka kwa Madzi a Mawu, ndi kupangitsa malingaliro anu ndi mtima kukhazikika pa Mulungu ndi pa Mawu Ake.

²⁷⁵ Tsopano, inu mumadziwa bwanji kuti Izo ndi zoonaa? Pamene Mulungu atsika pansi ndi kudzawatsimikizira Iwo ndi kutsimikiza.

²⁷⁶ Inu mukuti, “Chabwino, ine sindimakhulupirira Izo mwanjira imeneyo.” Iwo sanali kukhulupirira Izo mwanjira ya Yesu, koma Mulungu anazitsimikizira Izo. Iwo sankazikhulupirira Izo mwanjira ya Nowa. Iwo sankazikhulupirira Izo mwanjira ya Mose. Iwo anali kulolera kuti atenge mawu a Balaamu pa Izo, “Ndife tonse ofanana, kotero tiyeni tizingoyanjana limodzi.”

“Dzipatuleni nokha,” Baibulo linatelo, “ku kusakhulupirira.”

²⁷⁷ Aleluya! Tsopano zindikirani. Inu simuli kokha icho ayi, koma inu mukupita ku Chikwati mu mlengalenga. Ndipo inu mwavala mphete ya chikwati ya okonzedweratu, chisomo chosakuyenerani, mphete ya chikwati ya chisomo chosachipindula mwa nokha. Mulungu anazichita izo, Yekha. Iye anakudziwani inu asanaikidwe maziko a dziko, kotero Iye anaika mphete ya chikwati pa inu Kumeneko, anaika dzina lanu pa Bukhu. Kupereka mathokozo kwakeko! Aleluya! Mulungu wathu alemenzeke!

²⁷⁸ Tsopano, potseka, ine ndikhoze kunena izi. Ife tonse tikudziwa kuti mpingo wamakono, Wachipentekoste, mu chikhalidwe chake cha pakali panochi, zipembedzo zonse palimodzi! Ine ndikuwaponyera iwo onse mu mtolo umodzi, chifukwa iwo ali. Kumbukirani, Iye ayamba wamanga mtolo wa maudzu, poyamba, ndi kuwathenta iwo. Kutenga . . . Iye atenga mapesi onse a tirigu ndi kuwathenta iwo, poyamba; kenako Iye atenga, abwera ndi kudzatenga tirigu Wake ndi kumutengera iye Kwawo. Iwo onse akusonkhana mu mtolo, mtolo wa

Chimethodisti, Chibaptisti, Chipentekoste, onsewo akupita ku Ecumenical Council. Ndizo zonse. Onsewo awotchedwa. Mwaona?

²⁷⁹ Ife tonse tikudziwa kuti mpingo wamakono, mu chikhalidwe chake cha pakali panochi ndi momwe iwo uliri pakali pano, iwo suli mu chikhalidwe choti ungatsirizitse kutuma kwakukulu komwe Mulungu anaupatsa Mpingo wa tsiku lino. Ndi angati Achipentekoste angakhoze kunena “ameni” kwa izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Kulondola. Mwaona? Izo ziri mu . . .

²⁸⁰ Ndife aumodzi, auwiri, autatu, *ichi*, *icho*, *chinacho*, kukangana, kumenyana. Wina *ichi*, ndi wina *icho*, ndi *chinacho*. Ndipo aliyense wa iwo, akuwopa kuti ayang’anizane nawo Mawu, mpaka pa kuyesedwa pomwe. Mwaona? Iwo akudziwa. Iwe ukawauza iwo za Iwo; iwo amati, “I—ine sindingakhoze kuchitira mwina. Ine sindingakhoze kuwakhulupirira Iwo. Ine ndiribe nazo ntchito zomwe iye akuchita. I . . .” Mwaona? Mwaona? Zimasonyeza amanu ndi ababa omwe inu muli nawo. “Inu mukhoza kukhala woyang’anira dziko tsiku lina. Inu mukhoza kukhala *ichi*, *icho*, kapena *chinacho*.” Inu kulibwino mukhale mwana wa Mulungu.

²⁸¹ Tsopano, ife tikudziwa kuti mpingo sungakhoze ayi, mpingo wa Chipentekoste, mwanjira iliyonse, mwanjira iliyonse, sungakhoze kunyamula Uthenga wa tsiku lotsirizawu, mu chikhalidwe chake cha pakali panochi. Ungakhoze iwo? [Osonkhana ati, “Ayi.”—Mkonzi.] Chifukwa, iwo sakukhoza ngakhale kugwirizana pa Mawu amodzi kapena awiri mu Baibulo. Inu muzichita chotani izo? Izo sizingakhoze kuchita izo. Kotero, inu mukuchiona, chipembedzo chiri kunjira. Ndiko kulondola.

Awo adzakhala anthu osankhidwa omwe ali osankhidwira ku izo. Mwaona?

²⁸² Tsopano dziwani, ndipo kotero wina aliyense wa ife akudziwa, kuti mndandanda wonse wa zazipembedzo, Chipentekoste ndi onse, zafa, nzomwe ziri, kwa Mkristu wa Uthenga wobadwa kachiwiri. U-nhu. Mwamuna wanu woyamba anafa. Inu mukudziwa kuti iye anafa. Mulungu anazilola izo kuti zife. Izo zinatha. Njira zake zonse za mwasayansi, zaluntha, zamaphunziro, njira za mwasayansi za zake zotchedwa masukulu a Baibulo ndi zinthuzo zawonongeka. Zachita chiani? Zalekanitsa, aumodzi *apa*, ndi autatu *apa*, ndi auwiri *apa*, ndi cha *apa*, ndi pansu *apa*, ndi kunyansitsa koteroko, ndipo nkumadzitcha okha Achipentekoste.

²⁸³ Bwanji, ine ndinapita kwa mnyamata, tsiku lina; akumvetsera momwe muno, pakali pano. Ndipo Msungwana, iye anali wa mu mpingo winawake. Iye anati . . . Ine ndinati . . . Iwo analekanitsidwa. Ine ndinati, “Chavuta ndi chiani?”

Anati, “Ndife a chikhulupiriro chosiyana.”

Ine ndinati, “O, ine ndikupepesa. Kodi ndinu Mkatolika?”

²⁸⁴ Iye anati, “Ayi.” Iye anandiuza ine mpingo wa chipembedzo chomwe iye ali wa icho, wa Chipentekoste.

²⁸⁵ Ine ndinati, “*Iwe* ndi ndani?” Iye ndi wa Chipentekoste, nayenso, koma chipembedzo chinanso. O!

²⁸⁶ Inu mukudziwa, mpingo wa Chiroma Katolika unayamba, Mwachipentekoste? Ndi angati akudziwa kuti izo nzoona? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Zinautengera iwo zaka zikwi ziwiri kuti ufike pamene iwo wafikapo tsopano, sakutenga basi kalikonse ka Lemba panonso. Palibe. Bwanji, Achipentekoste, mu zaka makumi awiri kuchokera pano, adzakhala moipa kuposa momwe iwo aliri tsopano, izo zikakhala zikupitirirabe momwe izo ziririmu tsopano. Bwanji, zedi. Mwaona? Ndi chiani kodi? Ndi chiani kodi? Taonani yemwe bambo ndi mayi wao ali. Amawalola akazi awo kumadula tsitsi lawo. Iwo akhoza kumachita pafupi chirichonse chomwe iwo akufuna kuchichita. “Bola ngati iwo ali a mu mpingo uwu, ndizo zonse zomwe ziri zofunika.”

²⁸⁷ O, palibe zodabwitsa, palibe zodabwitsa kuti thembelero la Mulungu lawunjikana! Mulungu anaziyika Izo pamaso panu pomwe. Inu mumatseka maso anu ndi kulephera kuti muyang’ane pa Iwo. Eya. Kutseka matumbo anu a chifundo, pamene inu mukuwawona Mawu owona a Mulungu ndi Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri izi ziri kuwonetseredwa ndi kutsimikiziridwa kuti ziri chomwecho. Ndi kuchitiridwa umboni mmiyamba, mu mafuko onse ndi kwina kulikonse, mwa zizindikiro zazikulu ndi zodabwitsa zomwe Iye analonjeza kuti Iye akanadzazichita, ndiye inu mukudzitseka, nkuti, “I—ine sindikudziwa. I—ine sindingakhoze kuchitira mwina. I. . .” Mwaona? O, mai! Ndi okufa, ndipo sakudziwa izo. Mmachimo ndi zolakwitsa! Ndinu okufa. O, mai!

²⁸⁸ Ife tonse tikudziwa kuti mpingo mu chikhalidwe chimenecho sukanakhoza kulitsiriza tsiku lotsiriza lino. Kodi iwo ukanakhoza bwanji kumubweretsa Malaki 4 umo? Iwo ungakhoze bwanji kuzichita izo? Iwo sakhulupirira nkomwe mu chinthu choterocho. Iwo ungakhoze bwanji kukhulupirira, kubweretsa mmenemo Luka 17:30? Iwo ungakhoze bwanji kuwabweretsa umo Malemba ena onse awa omwe analonjezedwera ku tsiku lotsiriza lino? Izo sizingakhoze kuchita izo, chifukwa izo zimawakana Iwo. “Monga izo zinaliri mu masiku a Loti, chomwecho zidzakhala ziri mu Kudza kwa Mwana wa munthu.”

²⁸⁹ Tayang’anani pa chikhalidwe, Loti, chomwe Sodomu analimo, mu tsiku lija. Taonani, chikhalidwe cha mpingo wa lero. Taonani zomwe zinachitika kwa Abrahamu, Wosankhidwa.

290 Taonani zomwe zinachitika kwa Loti ndi iwo uko mu Sodomu. Tayang'anani pa Billy Graham ndi Oral Roberts, iwo kumusi uko mkati mwa zipembedzo izo. Tayang'anani pa Abrahamu Mpingo wosankhidwa, atadzikokera kunjia.

291 Taonani mtundu wa chizindikiro, womwe Yesu Mwiniwake, Mulungu wokhala mu thupi ataima apo mu mnofu wa umunthu. Inu mukuti, "Uyo anali Mngelo." Baibulo linati Iye anali Mulungu.

292 Ambuye Mulungu, Elohim, ataima apo mu mnofu wa umunthu, akusonyeza kuti Iye akanati adzaudzoze chotero Mpingo Wake mu masiku otsiriza. Kuti akanadzakhala Mulungu akugwira ntchito mu mnofu wa umunthu kachiwiri. "Monga momwe zinaliri mu masiku a Sodomu, chomwecho zidzakhala ziri mu Kudza kwa Mwana wa munthu." Mtundu womwewo wa chinthu. Iwo amaziwona izo umo momwe mu Malemba. "Ziwerengani Izo. Fufuzani Malemba, pakuti mwa Iwo inu mumaganiza kuti inu muli nawo Moyo Wamuyaya." Ndipo Iwo ndi Omwe amachitira umboni wa Izi. Mwaona? Mwaona?

293 Kotero ife tikudziwa kuti iwo ndi okufa. Mulungu wazilola izo zife mu zaumbombo zawozo, zasayansi, purogramu ya zamaphunziro.

294 Onse Achipentekoste ankachitira kuyankhula za—za kutumiza ana awo ku Baibulo sukulu, mmbuyomo pamene M'bale Loyate wachikulire, anali ali kuno, ndipo iwo akanakuthamangitsa iwe mu tchalitchicho. "Koma, o, tsopano ndi chinthu chachikulu. Mwana wanga ali kutali ku Baibulo sukulu." Iye akukumbako manda ake. Kotero, tsopano, inu mukuganiza kuti iwo angakhoze kuwatenga Iwo, lero?

295 Inu mukuganiza kuti ine ndikuyesera kuthandizira umbuli? Ine sindiri. Ine ndikukuuzani inu kuti pali kusiyana pakati pa m'badwo waluntha uno womwe ife tiri kukhalamo, mmene mpingo wapatsidwa pakati ndi sayansi ndi zonse izi zotchedwa "zolingaliridwa" ndi chirichonse. Inu simumamulingalira Mulungu.

296 Chabwino, iwo—ansembe awo anali atamulingalira Mulungu mwangwiwo kwambiri. Iwo ankadziwa momwe Mesiya akanati adzabwerere, koma Iye anabwera mosiyana kwambiri ndi zomwe iwo anali atalingalira. Izo sizinali mwasayansi. "Angakhoze bwanji Mwamuna uyu, pokhala Mwana wapathengo? Kodi Iye anapita sukulu yakuti? Kodi maphunziro Ake anachokera kuti? Kodi anakupeza kuti kuphunzira uku?"

297 Bwanji, Iwe ukuyesera kuti uzitiphunzitsa ife? Iwe unabadwa mu ziwerewere." Mwaona? O, chifukwa cha ubwino!

298 Mukuchiona chinthu chomwecho chikubwereza kachiwiri? [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.] Mukuona izo zikubwereza kachiwiri? Onse mu sayansi yawo yachipembedzo, sayansi

yachipembedzo malingana ndi zomwe Baibulo sukulu yawo inena, ndi momwe iwo amafunira Izo. “Ndi momwe Izo zikuyenera kuti zizikhala ziri, kapena Izo siziri.”

²⁹⁹ Mulungu amangowapusitsa iwo, nthawi iliyonse. Izo nthawizonse zimabwera mosiyana. Izo zinatero mu nthawi ya Nowa; zinatero mu nthawi ya Mose; zinatero mu nthawi ya Khristu; zinatero mu nthawi ya Yohane; zinatero mu nthawi ya atumwi; zinatero mu nthawi ya Wesile; zinatero mu nthawi ya Lutera; zinatero mu nthawi ya Chipentekoste; ndipo chotero zatero kachiwiri. Izo sizimasintha ndondomeko yake. Nthawizonse zimabwera ku chinthu chomwecho. Ndi okonzanso chabe kudutsa mu mibadwo isanu ndi iwiri, isanu ndi umodzi ija, mpaka wa chisanu ndi chiwiri. Ndipo Chivumbulutso 10 anati, mu ora ili izo zasintha. Ndipo izo zatero.

³⁰⁰ Tsopano ife tikutseka, ponena izi. Kudzatsirizitsa utumiki waukulu, iwo akanakhoza kuzichita motani izo? Ife tikudziwa kuti iwo anafa. Mulungu anzilola kuti izo zife mu m’badwo wa mwasayansi uno, zonse izo, k—kuti Iye akanakhoza (kuchita chiani?) kutsegula chinsinsi cha Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri kwa Mkwatibwi wosakhala mwa chipembedzo. Chipembedzo chingakhoze bwanji kuzivomereza Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri izo, pamene Izo ziri mwamtheradi zosiyana, mbewu ya serpenti ndi zinthu zina zonse izo? Zonse, zinsinsi zisanu ndi ziwiri zamphumphuzo ndi zosiyana ndi zomwe iwo akhala akuphunzitsidwa, chifukwa iwo anatenga sukulu yakale kuchokera ku sukulu yawo ya Baibulo.

³⁰¹ Ndipo Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri za Mulungu, pamene Izo zinatsegulidwa uko pa phiripo, Mulungu andilole ine kuti ndife pakali pano pa guwa ili ngati Icho si chiri Choonadi. Ndipo ine ndinakuuziranitu inu, chaka ndi miyezi sikisi izo zisanachitike, zomwe Iye anandiuzza ine, “Upite ku Arizona,” ndi zomwe zikanati zikachitike uko mu chipululu. Ndipo pali amuna omwe akhala pomwe pano, usikuuno, anali ataima uko komwe ndipo analipo pamene Angelo asanu ndi awiriwo anatsika. Ndipo ngakhale mag- . . .Magazini, *Life* magazine, inalemba nkhani ya Izo. Ziri uko komwe moyang’anira mmwamba, chirichonse. Tsopano iwo sakudziwa nkomwe kuti Izo nza chiani.

³⁰² Ndipo chirichonse chanenedwa kale, o, ngakhale ku kuwonongedwa kwa California, komwe kukubwerapo tsopano, ndi zinthu zina zonse izi. Ndi momwe ine ndinawauzira iwo masiku angati izo zikanadzakhallira ziri, momwe izo zikanadzakhala ziri momwe chivomezi chachikulu ichi chinachitikira mu Alaska, ndipo icho chikanakhala chiri chiyambi cha chizindikiro cha nthawiyo, ndi zomwe ziti zichitike. Ndipo basi liwu ndi liwu, zomwe Ilo linanena, izo sizinayambe zalepherapo nthawi imodzi. Inu simunayambe mwaziwonapo Izo zikulephera. Ndipo Izo sizingakhoze kulephera, chifukwa Izo ndi Mawu a Mulungu. “Ndipo

Kumwamba ndi dziko lapansi zidzachoka, koma Iwo sangakhoze kulephera.” Ndiko kulondola.

³⁰³ Mulungu ankayenera kuti atsegule Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri izo, osati mu chipemebedzo. Ine nthawizonse ndakhala ndikutsutsana nazo izo. Koma, kuchokera ku chipemebedzo, Iye angatengeko Mkwatibwi, osati mkwatibwi wachipemebedzo. Iye sangakhoze kuchita izo. Izo ndi zotsutsana ndi Mawu Ake Omwe. Iye anatsegula zinsinsi zisanu ndi ziwiri izo mmenemo. Izo zikusonyeza apo, zikubweretsa apo zinthu izo zomwe zakhala zitabisidwa kuchokera pa maziko a dziko, kuti zikhoze kuululidwa mu masiku otsiriza, kwa ana a Mulungu. Iwo azibweretsa Izo apo tsopano pamaso pa anthu, kuti iwo aziwone Izo apono, inu tsopano, kwa Mkwatibwi wosakhala wachipemebedzo uyu. O, mai!

³⁰⁴ Ndi awo apo mabuku anu awiri. Limodzi la iwo ndi Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa. Dzina lanu liri Pamenepo linakonzedweratu kukhala Pamenepo. Ilo silingakhoze kuchokapo, chifukwa inu simungakhozenso kulichotsapo ilo kuposa chirichonse, mwaona, chifukwa ilo linadzedwera kuti likhale liri Pamenepo. Koma bukhu lachizolowezi la moyo, akhoza kulichotsapo ilo nthawi iliyonse. Mwaona? Inu mukapanda kulapa, ilo lichotsedwapo, mulimonse, chifukwa inu mudzakaima pa Chiweruzo. Mkwatibwi sadzaima nkomwe pa Chiweruzo; akupita mu Mkwatulo. Basi monga . . .

³⁰⁵ Ine ndikunena izi, potseka. Izo zikufika pochedwa, kotero ili pafupi hafu pasiti naini. Ndipo ine titulukamo muno pofika hafu pasiti naini, Ambuye akalola. Basi molemekeza kwenikweni tsopano, mvetserani. Nthawi ina . . .

³⁰⁶ Ponena izi tsopano, izi zikupita mu fuko lonseli. Mu New York, tsopano ili twente-faifi minitsi pasiti leveni. Kutali uko mu Philadelphia ndi kuzungulira kumeneko, oyera okonedwa awo akhala ali uko akumvetsera, pakali pano, mu mipingo konse kozungulira. Kutali uko, kutali komwe kozungulira Mexico, kutali uko mu Canada ndi konse kozungulira, kudutsa. Mailosi thuu handiredi, kulikonse mkati mwa dera la North America kuno, pafupifupi, anthu ali kumeneko, akumvetsera pakali pano. Zikwi kuchulukitsa ka zikwi, akumvetsera.

³⁰⁷ Ndiwo Uthenga wanga kwa inu, Mpingo, inu omwe muli mchilumikizano, chilumikizano chauzimu mwa Mawu, kuti ndinu okufa kwa amunanu akale awa. Ndinu obadwa mwatsopano. Musati muyesere kuti mumukumbemo iye. Iye ndi wakufa. Ngati muli Mkhristu wobadwa kachwiri, nyongolosi yaing’ono iyo yomwe inakonzedweratu kwa inu, ndi Mawu akubwera pa Mawu, pa Mawu, pa Mawu, pa Mawu, ndi kubwera mu usinkhu wathunthu wa Khristu, ndi kulondola, kotero kuti Iye akhoza kubwera nkudzatenga Mkwatibwi Wake. Tsopano

ife tangokhala okonzekera chinthu chimodzi, ndiko Kudza kwa Ambuye.

³⁰⁸ Ndi ilo dzina lanu pa Bukhu la Moyo. Bukhu la Moyo ndi Mawu a Mulungu, chifukwa Mawu ndiwo Mulungu, ndipo Mulungu ndiye chinthu chokha chomwe chiri Moyo. Kotero dzina lanu linaimiridwa mu Baibulo Baibulolo lisanabwere pa Mawu. Ndipo ngati inu muli pano kuti mudzachite izo, kodi Ilo siliwatsimikizira Mawu amenewo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Kodi Mpingo sudzitsimikizira Wokha? Kodi Malaki 4, zinthu zina zonse izi, mwangwiro, ngwiro sizidzitsimikizira Zokha ndi kusonyeza kuti ndi zomwe Izo ziri? [“Ameni.”]

³⁰⁹ Pamene Yesu anadza, Iye anati, “Ngati ine sindikuchita ntchito zomwe zinalonjezedwera kuti Ine ndizichite, musandikhulupirire Ine.” Kodi ndi liti la maguluwo lomwe Iye analijowina? Iye anati, “Iwo onse . . . Ndinu a atate wanu, Mdierekezi, ndipo ntchito zake inu mukuzichita.” Mwaona? Mwaona?

³¹⁰ Ife tiri mu masiku otsiriza, Mpingo. Ndiwo Uthenga wanga wopereka mathokozo kwa inu.

³¹¹ Tsopano, tisanati titseke. Nthawi ina ine ndinali uko mu Glacier National Park. Ife tinamva, utali wa tsiku lonse, kuti iwo anali—iwo anali ndi kugwa, kwa moto wa pa mtsinje wa pa chisanu womwe amati ugwa usikuwo. Kotero anthu anali otangwanika, utali wa tsiku lonse, akukonzekeretsa chinthu chimenecho, chifukwa amati atsanulire moto umenewo, usiku umenewo. Iwo amaika moto wachiphala kuti uzigwa, ngati madzi a pa chisanu. Koma ndi . . . Zimawoneka ngati utawaleza, pafupi, pamene izo zimatuluka, wa moto uwo ukugwa kuchokera mu mtsinje wa pa chisanu uwu. Konse kuzungulira ku parkyo, mkazanga ndi ine, ndi ana, tinayendayenda kudutsa mtsikulo. Ife tinkafuna kuti tidikire kuti tiwone chiwonetsero cha moto icho. Kotero izo—izo—izo zinalonjezedwa kuti ife tikanaziwona izo, ndipo tikanachitira umboni izo kachiwiri. Iwo anati iwo amakhala nazo izo nthawizonse kudutsa mu nyengo za thirimwe ndi zina zotero. Ine ndinati, “Chabwino, kodi ife tikhoza kuziwona izo?”

³¹² Anati, “Ife tikulonjeza izo usikuuno. Ife tinalonjezedwa izo.” Anati, “Iwo ali pamwamba apo akukonzeketsera izo pano.”

³¹³ Zonse zinali zitatha kukonzeketseredwa kwa zodzachitikazo! Ndi zomwe ziri kuchitika pakali pano. Zonse zakonzeketseredwa kwa chochitikacho, Mpingo uli kutulutsidwa wa a Dzina Lake, akumutenga Mkwatibwi Wake atuluke kuchokera pakati pa dziko, zipembedzo izi ndi dziko lonse, ndi nyansi ndi zinthu za mdziko.

314 Aliyense; chochitikacho chinakonzeketseredwa. Aliyense anali ataima panja. Iwo anati, “Tsopano pitirirani kuyang’ana, pamwamba pomwe pa phiri apo.”

315 Ndi momwe nthawizonse iwo umadzera. Ndi momwe Iwo uti udzere nthawi ino. Ndi momwe nthawizonse Iwo umadzera. Osati kupyolera mu chipembedzo! Palibe nkomwe pamene Mulungu anagwiritsapo ntchito chipembedzo, palibe!

316 Wokonzanso akapitapo, iye amatenga Mawu a Ambuye. Ndiyeno pamene iye afa, iwo amamanga chipembedzo pa icho. Ndi zomwe Achipentekoste ndi onsewo anachita. Pamene nkhani zatsopano, chirichonse, basi ndiyo njira yake. Ndi momwe chinthucho chinabwerera apo. Mawu atsopano atawonjzedwera, ndiye iwo amamanga mpingo kuchokera pa izo, amapanga chipembedzo, amadzilekanitsa okha. Izo zimayenera kukhala ziri mwanjira imeneyo.

317 Tsopano, inu simungakhoze kuchigonjetsa—inu simungakhoze kuchigonjetsa chirengedwe. Chirengedwe chimatsatira mchitidwe womwewo, nthawi zonse: phesi, tsamba, ngayaye, zina zotero, nkhusu, kenako tirigu.

318 Tsopano zindikirani. Zonse zinali zokonzeka. Chirichonse chinali chitayatsidwa ndi kukonzeketseredwa. Ndipo aliyense anali ataima panja. Ine mutu wanga ndinali nditautukula mmwamba; nkono wanga mozungulira mkazi wanga. Ife tinali kuyang’ana. Ndipo ana ataima apo, tonse ife tikuyang’ana mmwamba, monga choncho. Mai! Ichu chinali chinachake, chifukwa ife tinali kuziyembekezera izo. Izo zinali zitalonjzedwa kwa ife.

319 Ameni! Mawu akulonjeza Izi. “Zidzafika pochitika, lisanadze tsiku lalikulu ndi lowopsya la Ambuye, taonani, ine ndidzakutumizirani inu Eliya mneneri. Iye adzatembenuzira mitima ya ana kwa atate.”...?... “Zidzafika pochitika mu masiku otsiriza, Ine ndidzatsanulira Mzimu Wanga kuchokera Kumwamba.” “Mvula yanyundo ndi yamasika idzadzala palimodzi mu tsiku lotsiriza.” Malonjezo onse awa, kudutsa mu Malemba, akuperekedwa. Ife tikuyang’ana mmwamba. Kuyang’ana pa Mkwatibwi woona mu fuko lonseli ora lino, akuyang’ana mmwamba. Mpingo, Iye akubwera, limodzi la masiku awa. Motsimikiza basi monga Iye anadza nthawi yoyamba, Iye akudza kachiwirinso. Pangitsani chirichonse chikhale chokonzeka. Dzipatuleni nokha kwa mankhusu. Dzigonekeni pamaso pa Mwana. Pitirirani kuyang’ana mmwamba. Khalani pansu pa chiyembekezera.

320 Zonse mwakamodzi, ife tinamva chinachake kuchokera pamwamba pa phiri, liwu linabwera pansipo kupyolera mu zofuulitsira moyankhula, linati, “Zinthu zonse zakonzeka.”

321 Ndiye bambo uyu, ataima apo pomwe pambali pa ine, anati, “Lolani moto ugwe.” Uwu ukudza apawu, ukutsanulirika

pansi kudutsa pa phiri limenelo, mtsinje wa moto ndi malawi akunyambita, mawonekedwe oti nkuwapenya.

³²² M'bale, tiyeni tikhale ndi zinthu zonse mokonzekera, chifukwa limodzi la masiku awa Moto udzagwa. Ife tikupita mmwamba. Tsopano tiyeni tikhale okonzekera nthawi ya kugwa kwa Moto. Ife tiri mu masiku otsiriza, ife tonse tikudziwa izo, ndipo ife tiri okonzekera Kudza kwa Ambuye. Chinthu choti tichite ndi kudzipatula wekha ku tchimo lonse. Kudzipatula nokha kwa chirichonse chomwe chiri cha mdziko. “Musati muzilikonda dziko kapena zinthu za mdziko.”

³²³ “Musamulole munthu wina, ndi kachikhulupiriro kake, akunyengeni inu.” Inu mukhale molunjika basi mu lonjezo la Mulungu, Mawu a Mulungu. Ndipo Mawu amenewo, ngati Iwo ali Mawu a tsiku lino, Mulungu amawatsimikizira Iwo chomwecho. Ngati Iye satero, iwo si Mawu a tsiku lino.

³²⁴ Mawu omwe anagwa pa Tsiku la Pentekoste sagwira ntchito mu tsiku lino. Ayi, bwana. Iwo anali a Pentekoste. Awa ndi a Mkwatibwi, kupita Kwawo kwa Mkwatibwi. Ife tiri ndi chinachake chosiyana. Achipentekoste ankaimira icho, nawonso. Ife tiri mu m'badwo wa Mkwatibwi. Si zoposa m—Mawu a Nowa kuti akanagwira ntchito mu masiku a Mose; si zoposa kuti lamulo la Mose likanagwira ntchito mu nthawi ya Paulo kuno. Iye ankayesera kuwauza iwo, “Ndinu okufa kwa awo, ndipo inu simungakhoze kukhala nawo awo.”

³²⁵ Mpingo, inu omwe ine ndikuyankhula nanu, usikuuno, ku fuko lonseli, n—ngati inu mwadzipatula nokha kuchokera ku chipembedzo ndi nyansi zonse ndi zinthu za mdziko lino, ndi zinthu zonse izo zomwe zimakusungani inu mu tizikhulupiriro topangidwa ndi anthu ndi madongosolo ndi zinthu zonga izo, inu mwadzilekanitsa nokha. Ziyang'anani mmwamba. Khalani okonzeka. Moto ugwa, limodzi la masiku awa. Mulungu amulola Iye kuti abwere, ndi mawonekedwe oti nkuwapenya. Kodi inu mudzakhala muli okonzeka pamene Iye akudza? Kodi inu mudzakhala muli okonzeka kudzapita naye Iye mmwamba pamene Iye akudza? Mkwatulo wachinsinsi wa Mkwatibwi wauzimu, “Iye adzapangidwa wac-...kuchoka ku chivundi kupita kuchisavundi; kukhala atasinthidwa, mu kamphindi, mu kuthwanima kwa diso. Ife omwe tiri amoyo ndipo titatsalira sitidzawalepheretsa iwo omwe ali chigonere.”

³²⁶ Tsiku lina, pa Tsiku la Kutha kwa nkondo, ine ndinali nditaima uko mu Tucson. Mnyamata wanga wamng'ono ankafuna kuti awone pelete. Ine ndinali ndikuwerenga, ndipo ine ndinalibe nthawi yoti ndikachite izo. Ine ndinali ndi kuitana kuchuluka kwa odwala ndi zinthu. Koteri iye anati, “Adadi, iwo sakufuna kunditenga ine.” Iye anati, “Nditengeni ine.”

³²⁷ Ine ndinati, “Chabwino.” M'bale Simpson, ine ndikuganiza iye ali pano; ndi mnyamata wake wamng'ono ankafuna

kupita. Kotero ine ndinawakokera iwo mu galimoto ndi kuthamangira uko.

³²⁸ Ine ndinaima pa ngodya apo ndipo ndinkayang'ana. Ndipo patapita kanthawi, ine ndinamva, komwe kumbuyo patali, mdidi ukubwera, “buu, buu,” ng'oma, zikulira. Ine ndinaima apo. Ine ndinaganiza, “Chabwino, anyamata aang'ono awa awerengadi kwenikweni mabuku onse awa okhudza ankhondo. Iwo azikonda kwenikweni izo.” Ine ndinazindikira, zobwera apo koyamba zinali zimathanki za Nkhondo Yoyamba ya Dziko lonse. Apo anabwerapo, anthu aang'ono kwambiri monga choncho. Apo panali otsatira kubwerapo, atatha awo; omwe anali wotsatira kubwera atatha awo inali thanki yaikulu yatsopano ya Nkhondo Yachiwiri ya Dziko lonse, thanki yaikulu ya Sherman ili ndi chowombera chothyoka pa iyo. Ndiye panadza otsatira, ndi otsatira, ndipo patapita kanthawi panabwera Amayi a Nyenyezi ya Golide.

³²⁹ Ndiyeno, patapita kanthawi, panabwera ankhondo akale khumi ndi awiri omwe atsalapo, mu dziko lonse la Arizona, a ku Nkhondo ya Dziko lonse Yoyamba; ankhondo akale khumi ndi awiri. Pambuyo pa awo, panabwera choyandama, msilikari wosadziwika, mtanda wawung'ono woyera. Apo panaima wa panyanja, apanyanja, ndi msilikari, ataima molondela; kagawo kakang'ono pa choyandamacho. Kumbali inayo kunali mayi wokalamba wa mutu waimvi, atakhala ali ndi nyenyezi ya golide itaikidwa pa iye, mkazi wamng'ono wokondeka akulira, mwamuna wake anafa; mnyamata wamng'ono wasanza, mutu wake atautembenezira chakumbali. Adadi ake anaphedwa. Ndiyeno kumbuyo kwa izo kunabwera zochuluka ndi zochuluka chuluka, ndiye mpaka kwa ankhondo atsopano. Ine ndinaima pamenepo. Mawonekedwe ake oti uwapenyewo, koma kuchititsa chisoni kwakeko!

³³⁰ Ine ndinaganiza, “O Mulungu, limodzi la masiku awa ine ndidzakapnya mawonekedwe ena.”

³³¹ Iwo adzabwerapo pa tsiku la chiukitsiro, pomwe, “Oyamba adzakhala otsiriza; iwo omwe ali otsiriza adzakhala oyamba. Aneneri akale adzabwera akuwonekerapo, choyamba, ndipo iwo adzaliwona gulu ilo likupita, akuguba kupita mlengalenga umo. “Ndipo ife omwe tiri moyo ndipo titatsalira sitidzawalepheretsa iwo omwe ali chigonere. Pakuti lipenga la Mulungu lidzawomba, okufa mwa Khristu adzauka choyamba.” Ife tidzagwera kumene mu mzerewo ndi iwo kupita mmenemo, aleluya, konse kudutsa mu m'badwo wa Lutera, Wesile, Chimethodisti, Presbateria, mpaka mmusi mpaka ku m'badwo wotsiriza, omwe analandira Mawu a mu m'badwo wao.

Mulungu akudalitseni inu. Fikitsani zinthu zonse pokonzeka, ndipo Moto ugwa.

³³² Tiyeni tiweramitse mitu yathu mphindi yokha. Ine ndikudabwa, mu gulu losawoneka ili usikuuno, pamene ine ndakusungani inu pano kwa . . . mpaka hafu pasiti naini. Kodi alipo mmodzi pano, kodi alipo dazeni pano, ndi angati pano, ndi kuti, “M’bale Branham, ine ndikudzichitira manyazi ndekha, momwe ine ndakhalira moyo. Ine ndasamalira kambiri ku zachipembedzo ndi anthu. Ine ndikudziwa kuti ine sindiri pamwamba ndi Mawu a Mulungu. Ine ndati ndingokupemphani inu kuti mundipempherere ine, M’bale Branham”? Kwezani mmwamba dzanja lanu. Mulungu akudalitseni. Mulungu akudalitseni inu. Tangowonani, mmwamba momwe umu mkhondelo, mozungulira. Mulungu akudalitseni inu. “Ine ndikudziwa . . .” Tsopano musachite manyazi. Tsopano, musati muchite.

³³³ Ndipo uko kutali, ku fuko lonseli, kuchokera ku New York mpaka ku California, kuchokera ku Canada mpaka ku Mexico, anthu inu omwe mwasonkhana mu matchalitchi amenewo komwe magulu aang’ono achikhulupiriro awo omwe akuukhulupirira Uthenga uwu ndi mitima yawo yonse. Iwo atuluka, atuluka kuchoka ku chisautso chachikulu, atuluka kupyola mu zipembedzo izo. Iwo ndi nyongolosi za Moyo. Kodi inu mukumverera kufulumizitsako, usikuuno, monga mphungu yaing’ono, kuti inu mukumva Chinachake chomwe chiri chosiyana pang’ono kwa chomwe inu munamva, koma, apobe, mu mtima mwanu inu mukudziwa kuti icho ndi Choonadi? Inu, mkati umu, pali m’busa waima apo penapake. Inu mwaimika dzanja lanu mmwamba. Ine ndati ndikukupemphereni inu.

³³⁴ Zinthu izi sizinachitidwe ku ngodya, mzanga, Kumbukirani, “Khwalala ndilo chipata ndipo njirayo ndi yopapatiza, ndipo koma ndi apang’ono ati adzakhalepo omwe ati adzaizepe iyo.” Musati muzipita ndi unyinji uwo womwe ukusunthira kutali, mzanga, M’badwo wa Mpingo wa Laodikaya uwo. Iwo ukhoza kumalumpha mmwamba-ndi-pansi, kumavina nayo nyimbo, ofunda. Ilo silinati iwo unali wozizira mwachisanu tsopano. Ilo linati, “Iwo unali wofunda,” ndicho Chipentekoste, “ndipo sakudziwa kuti ndi omvetsachisoni, opandapake, akhungu.” Khungu kwa chiani? Mawu, ku mawonetseredwe a Mulungu, chifukwa Iwo sanabwera konse kupyolera mu mabungwe awo. Iwo sangakhoze kuwalandira Iwo.

³³⁵ Ndipo inu atumiki kumusi uko mu Tucson, usikuuno, ine sindiri kukuimbani inu mulandu chifukwa cha izo. Mulungu ali. Ine ndinali kumeneko kwa zaka zitatu. Ine ndinakuuzani inu kuti ine sindikanati ndiyambitse mpingo. Ine sindinatero. M’bale Peary Green anauyambitsa iwo. Ine ndinali kumeneko kwa zaka zitatu, ndipo palibe nthawi imodzi yomwe inu munandiitanira ine ku guwa lanu. Ine ndinali mu Tucson kwa pafupi kwa zaka zitatu. Mulungu adzandichotsako ine ku chipululuko limodzi la masiku awa. Uthenga uwu uyenera ukhale moyo. Ine ndayesera

mwakukhoza kwanga kuti ndibwere kwa inu. I—ine ndikudziwa chifukwa chomwe inu munachitira izo. Inu mukumva? Chifukwa chokha chomwe inu munachitira izo, chipembedzo chanu chikanakukankhirani inu kunja. Ndipo inu mukudziwa, ambiri a inu omwe ndayankhula nanu, uko ku Restauranti ya a Furr, ndipo inu mukudziwa kuti ndi zoon. Manyazi pa inu.

³³⁶ Tulukani kwa izo. Chokako uko, m'bale. Ngati muli Moyo uliwonse mwa inu, inu mukhala ngati mphungu yaing'ono ija yomwe ine ndinaikamba posachedwapa, inu mwamva Mawu a Mulungu. Kumbukirani, inu mudzazimva Izi kwa nthawi yotsiriza, limodzi la masiku awa. Ife tayandikira kwenikweni tsopano. Kodi inu simubwera, usikuuno?

³³⁷ Wokonedwa Mulungu, ife takhala mwakachetechete tsopano, tsiku lopereka mathokozo ili liridi, Ambuye. Ndine woyamikira, Ambuye, kuti ndiri moyo mu tsiku ili. Ili ndi tsiku lalikulu. Paulo mtumwi ankakhumba kuti aliwone tsiku ili. Amuna aakulu akale ankafuna kuti aliwone tsiku lino. Aneneri ankakhumba kuti aliwone ili. Iwo ankayembekezera tsiku lino. Abrahamu ankayembekezera tsiku lino, pakuti iye ankafunafuna mzinda Womwe Woumanga ndi Woupanga Wake anali Mulungu; iwo uli pamwamba pathu pomwepa, usikuuno. Yohane anauwona Mzimu wa Mulungu ukutsika kuchokera Kumwamba, anachitira umboni, anadziwa kuti ameneyo anali Mwana wa Mulungu. Ndipo, taganizani tsopano, Iye akusankha Mkwatibwi Wake.

³³⁸ Wokonedwa Mulungu, kunjako mu dziko lonseli kulikonse, yankhulani kwa mtima wao. Ndinu Mmodzi yekha yemwe angasinthe mtima wao. Ngati iyo ikanati isakhale Mbewu itaikidwa mmenemo pachiyambi, iwo sakanadzakhoza konse kuuwona konse Iwo, Ambuye. Iwo akanangokhala... "Wakhungu akutsogolera akhungu. Iwo akagwera mu dzenje," motsimikiza basi monga chirichonse, chifukwa Mawu Anu ati iwo adzatero.

³³⁹ Tsopano, Atate, pokhala kuti ife tikuwona mu dziko lonseli, kuzungulira dziko, mu Afrika, madazeni, madazeni kupyola mu South Afrika, Mozambique, konse kudutsa dzikoli, timagulu tating'ono tikumawatenga matepi awa. Ndipo chotero tepi iyi idzapita ku mafuko ena makumi awiri osamvetsetseka, osiyana. Iwo akuyamba kuwuona Iwo ndipo akudzikokera kumbali, mazana ndi mazana a iwo. Sizitengera ambiri, Ambuye. Ndiye pamene membala wotsiriza walandiridwa kulowa mu Thupilo, Khristu adzabwera.

³⁴⁰ Ambuye Mulungu, ine ndikumufunsa Mkwatibwi, usikuuno, iwo omwe ine ndikumverera kuti adzikokera ndipo akudikirira. Mulole iwo adzipatule okha kuchoka ku chirichonse cha mu dziko. Iwo ayenera kuti akhale mu Kukhalapo kwa kufunda kwa

Kuwala kwa Mwana wa Mulungu, akusamba mu Mawu Ake, mu chikondi Chake. Perekani izi, wokondedwa Mulungu.

³⁴¹ Aloleni anthu awa pano, owoneka, omwe akwezera dzanja lawo mmwamba, usikuuno, madazeni a iwo mu kachisi wamkulu yense uyu. Ine ndikupemphera, Mulungu, kuti Moyo watsopano ubwere mwa iwo. Ine ndikupempherera izi, ku fuko lonseli ndipo ngakhale kuzungulira dziko, komwe tepi iti idzaseweredwe, kuti iwo nawonso adzalandire Uthenga uwu wa kupereka mathokozi ndi kudziwa, mwa mfundo ndi zinthu zomwe zaponyedwamo, zomwe iwo ayenera kuti achite. Ine ndikupemphera izi, Atate. Perekani izi. Adalitseni iwo. Iwo ndi Anu.

³⁴² Ine ndikudziwa ndi mwamwambo wake tsopano, Atate, kuti tiwafunse anthu abwere ku guwa. Ine ndikupemphera, wokondedwa Mulungu, kuti mu mishoni iliyonse, kulikonse kozungulira, ndi ku dziko lonseli, kuti iwo abwere ku guwa: akuda, oyera, achikasu, abulauni, kulikonse komwe iwo ali; olemera, osauka, osiyana, opemphetsa, chirichonse chomwe iwo ali.

³⁴³ Zipembedzo, iwo omwe akhala ali ochita zaokha ndi omva zawozokha, O Mulungu, “Amaliseche, omvetsa chisoni, opanda pake, akhungu, ndipo sali kuzidziwa nkomwe izo.” Inu munati izo zikanadzakhala mwanjira imeneyo, ndipo izo ziri mwanjira imeneyo.

³⁴⁴ Chotero ine ndikupemphera, Atate, kuti Inu muyiitana Mbewu iliyonse, usikuuno. Ndi kulikonse kuzungulira dzikoli komwe Iyi iti ikagwereko, mulole Iyo ikaigwire mphungu yaing’ono iyo yomwe ikulidziwa Liwu la Ambuye wake. Perekani izi, Ambuye. Ine ndikuwapereka iwo kwa Inu, mu Dzina la Yesu. Amen.

³⁴⁵ Tsopano ndi mitu yanu yoweramitsidwa, pano mwa omvetsera owoneka. Pangakhale ena pano, omwe sanakhale ali opulumutsidwa, simunapereke ngakhale mtima wanu kwa Mulungu, kodi inu simukuganiza kuti mukuyenera kukhala othokoza kwambiri chifukwa cha zomwe Yesu anakuchitirani inu? Kuganiza, kuti ndinu wochimwa, kuti ndinu mlendo kwa Mulungu, ndipo komabe Chinachake chiri pa mtima wanu, chikugogoda. [M’bale Branham akugogoda pa guwa—Mkonzi.] Inu mukudziwa bwanji kuti mwina chomwe inu ndinu imodzi ya mphungu zazing’ono izo! Ndinu omvetsa chisoni, ndipo muzikhala muli omvetsa chisoni, mpaka inu mutadzipereka kwa Iwo. Bwanji osakupanga uku kumodzi kwa kupereka mathokozi komwe inu munayamba mwakhala nako, pamene inu munamulandira Yesu Khristu ngati Mpulumutsi wanu.

³⁴⁶ Kodi inu mubwera pamwamba pano ndi kudzaima pa guwa? Ine ndipemphera ndi inu ngati inu muti mubwere, wochimwa aliyense, mwamuna kapena mkazi, mnyamata kapena mtsikana, membala wa mpingo kapena wosakhala

membala wa mpingo. Umembala wa mpingo sumakupangani inu kukhala Mkhristu tsopano. Guwali ndi lotseguka. Kodi inu mungabwere, wochimwa aliyense yemwe angafune kuti abwere, landirani Ambuye Yesu Khristu. Mungafune kuti musiyе kwenikweni. . .

³⁴⁷ Ena a achipembedzo inu omwe mukanafuna kuti musiyе kumadya pa chakudya cha nkukhu icho, chomati, “Ndinu a *ichi* ndipo izo nzabwino.” Kodi inu mukufuna kuti mudziwe kwenikweni chomwe ubatizo weniweni wa Mzimu Woyera uli? Bwerani, mudzaone.

³⁴⁸ Guwa ndi lotseguka. Ife takonzeka. Zingobwerani, pano— kuchoka pomwe mwakhalapo. Bwerani ndi kudzagwada pansi pa guwa apa, m’bale uyu wangobwera kumene.

³⁴⁹ “Kupereka mathokoza, O Mulungu, ndine wothokoza kwambiri kwa Inu. Kuti, moyo wanga wonse, ine ndimadziwa kuti panakhala pali chinachake, Ambuye. Ine sindinayambe ndakhutitsidwapo. Ine ndayesera. I—ine ndinkaganiza, ‘Chaka chamawa, ine ndidzachita izo. Sabata yamawa, ine ndidzachita izo, nthawi yotsatira yomwe ine nditi ndidzamve kuitanira paguwa. Ine ndidzatero, tsiku lina.” Ine ndachiika icho kumbali, ndi kuchiika icho kumbali. Koma, Ambuye, ine ndikudziwa kuti pali chinachake cholakwika ndi ine. Ine nthawizonse ndimakhulupirira panali chinachake chosiyana. Ndipo tsopano, Ambuye, usikuuno, ndine wothokoza kwambiri chifukwa cha kukonzeketsera komwe kunapangidwa ndi Mwana wa Mulungu, kuti machimo anga, makamaka kusakhulupirira kwanga, kungati kutsukidwe kuchoke kwa ine. Ine ndikudza, usikuuno, ndipo ndikugwada pansi kuti ndivomereze mdalitso wa kupereka mathokoza waukulu womwe Yesu Khristu anandichitira ine pamene Iye anandifera ine pa Kalvare.”

³⁵⁰ Kodi inu mungabwere? Tsopano pali anthu omwe agwada kuzungulira paguwali pano. Bwanji inu simukunyamuka ndi kubwera? Inu mwakhala mukufuna kuti muchite izi. Inu mwayesera izo.

³⁵¹ Tangoganizani za M’bale Lyle Palmer, m’bale wathu wabwino, wofunika. Iye anali atakhala pabwalo, ine ndamva choncho, akuyang’ana pa msungwana wake wamng’ono akusewera mpira ndi ndodo kunjа uko, kapena chinachake, ndipo iye anagwapo pa mpando ndipo anali atafa iye asanati apange kusuntha nkomwe. Iwe sumadziwa nthawi yomwe iwe uti udzachokeyo kuno. Iwe sumadziwa basi nthawi yake yomwe iwe uli kupita. Iyo ikhoza kukhala panobe, usikuuno, kotero bwanji osabwera ndi kudzazikonza izo tsopano?

³⁵² Bwerani, anthu. Kodi inu simukukhoza kumverera Chinachake chikukoka pa inu? I—ine ndikudziwa alipo ambiri a inu pano omwe mukuyenera kukhala muli pa guwa, ndi basi anthu sikisi kapena seveni ali pano si omwe ali muno. Tsopano,

ngati inu mukundikhulupirira ine ndikupenya pano pa guwa, zinthu zikuchitika, inu mundikhulupirire ine tsopano. Tsiku lina liwu langa lidzatontholetsedwa. Inu simudzalimvanso ilo kenanso. Inu mukanakhumba mukanati mubwere.

³⁵³ Inu mukuti, “Koma, M’bale Branham, ine ndakhala ndiri membala wa mpingo.” Izo sizimapangitsa kusiyana kulikonse chomwe iwe wakhala uli. Mmomwenso anali—mmomwenso analiri Nikodimo ali membala wa mpingo. Mmomwenso analiri Yohane, Petro, Yakobo, Paulo, onse enawo anakhala ali mamembala a mpingo.

³⁵⁴ Paulo anali membala wa mpingo mpaka chinachake chitachitika usiku wina, kapena tsiku lina nchomwe linali, ndipo iye anadza. Iye anali membala wa mpingo wosinthika ndiye, kukhala mwana wa Mulungu. Kodi inu simubwera? O, iye anali ataphunzitsidwa. Iye anali waluntha. Iye ankadziwa kuti iye anali wophunzitsidwa, imodzi ya sukulu zophunzitsa-mwapamwamba kwambiri zomwe zinalipo, Gamalielo, mmodzi wa aphunzitsi abwino zedi yemwe analipo mu dzikolo. Koma iye ankadziwa kuti ankasowa chinachake.

³⁵⁵ Kodi inu simubwera? Kamodzi kenanso ine ndikukupemphani inu. Komwe...Kuno kapena kuzungulira fukoli, ine ndikukufunsani inu, kulikonse komwe inu muli, gulu lomwe inu muli wa ilo, pa ora la kupereka mathokozi ili. Kumbukirani, ine ndiri kutepedwa pano; osati pano pokha, komanso Kumwamba.

³⁵⁶ Inu mukudziwa, izi zatsimikiziridwa mwasayansi kuti kusuntha kulikonse komwe iwe umakupanga kumajambulidwa. Iwo atsimikizira izo. Kumbukirani, televizioni inatsimikizira izo. Televizioni si—siimapanga chithunzicho. Inu ndinu chithunzicho. Iyo imangodusitsa icho chomwe inu mukuchita, kupita mu mpita. Inu muli apo, basibe. Mwaona? Pamene inu musuntha chala chanu, kusuntha kumeneko kumapita kuzungulira dziko. Nthawi iliyonse yomwe inu muvala diresi, mawonekedwe anu amapita kuzungulira dziko. Izo ziri pa rekodi. Lingaliro lirilonse lomwe limapita kupyola mu malingaliro anu liri pa rekodi. Ndipo tsiku lina rekodiyo idzasiya kusewera, izo zidzaikidwa pa chimbale.

³⁵⁷ Ndiyeno pa Chiweruzo izo zidzabwereranso. Apo inu mudzaima ndi tsitsi lodula, mukudzinenera kuti ndinu Mkhristu. Apo inu mutaima ndi mu maganizo mmalingaliro mwanu otsutsa Mawu, ndi izo ziri mmalingaliro mwanu momwe. Inu simungakhoze kuzibisa izo. Kumbukirani, televizioni, sayansi imadziwa ngakhalenso kuti izo nzoona. Inu mwaima pakali pano, mukudziwa kuti inu mukuyenera kukhala muli apa, kumbukirani, momwe izi ziri kujambulidwa. Pa Tsiku la Chiweruzo, ganizo lomwelo limene inu muli nalo lidzakhala likubwerera kudutsa mmalingaliro mwanu kachiwiri. Izo

zidzakakhala pa rekodi pomwepo. Dziko lonse lidzaziwona izo zikuseweredwa. Bwanji osati dziko. . . Akuyang'ana pa inu, pa Tsiku la Chiweruzo, Angelo onse ali pamene.

³⁵⁸ “Ngati inu mukuchita manyazi ndi Ine kuno, pamene chithunzi chanu chiri kupangidwa tsopano, pa Tsiku la Chiweruzo ine ndidzachita manyazi ndi inu. Pakuti, Ine ndinawadzoza Mawu Anga, ndinawatumiza Iwo kwa inu. Inu simunati muwakhulupirire Iwo. Inu munadzibisa nokha kumbuyo kwa chinachake.”

³⁵⁹ “O,” inu mukuti, “Ndine wabwino mokwanira. Ine ndachita *izi*. Ine ndavina mu Mzimu. Ine ndayankhula mu malirime.” Mmomwenso amachitira achikunja. “Ine ndinafuula.” Mmomwenso amachitira achikunja. Inu mungakhoze bwanji kulozetsa nsana pa Mawu ndiye?

Bwanji?

Bwanji osadza kwa Iye pano?

Bwanji? Bwanji?

Bwanji osadza kwa Iye pano?

Bwanji mukudikira, m'bale?

O, bwanji mudikira motalika?

Yesu ayembekeza akupulumutseni

Kwawo koyeretsedwa.

Dziikeni ngati mmodzi wa mamembala a Thupi Lake!

Bwanji?

O, mphungu yaing'onowe, bwera tsopano.

O, bwanji osabwera?

³⁶⁰ Ambuye, ndiri kuthokoza kwambiri. Ndine wothokoza kwambiri. Kupereka kwa mathokoza kwa Inu, Ambuye; osati chifukwa cha chakudya chachirengedwe, komabe icho. Koma, Ambuye, nthawi yotsiriza ili pano. Ndine wothokoza chifukwa cha Chakudya chauzimu ichi, Ambuye, Chakudya chauzimu cha Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri chomwe chinalonjezedwa kuti chidzatsegulidwe.

Inu mukuti, “Izo zidzakhala zinazake zosiyana.” Ayi, ayi.

³⁶¹ Inu simungakhoze kuwonjezera mawu amodzi. Ndi kutenga. . . Izo ziri kale Mmenemo, zinangobisika. Izo nzosindikizidwa. Ndi angati akumvetsa izo? Nenani, “Ameni.” [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Mwaona?

Inu mukuti, “Chabwino, icho ndi chinsinsi chomwe chiti chibwepo.” O, ayi.

³⁶² Izo Zinalembedwa kale. Inu simungakhoze kuwonjezera mawu amodzi kwa Iwo, kapena kuchotsa amodzi kwa Iwo. Mwaona? Izo ziri kale mMenemo. Izo zikungoyenera kuti ziululidwe mu tsiku lotsirizali.

363 Kodi inu simubwera? Bwerani tsopano, mzanga. Ngati inu simungakhoze kumvetsa, bwerani. Dzagwadeni pansu, dzayankhuleni kwa Iye pa Izo. Ngati ine sindikukhoza kuzipangitsa Izo kumveka kwa inu, Iye atero, pakuti Iye ali—Wosungunula zokaikitsa zonse.

. . . m khamu Lake loyera.

O, bwanji kodi inu simubwera? Bwanji?

Bwanji osadza kwa Iye pano?

364 Kumbukirani, pali kujambula kukupangidwa kwa izi, osati kokha pa tepi iyi, koma rekodi yaikulu ya Mulungu. Aliyense wa inu, kusuntha kulikonse, pamene inu mukuweramitsa mutu wanu, kuweramitsa mtima wanu, ganizo lomwe likudutsa mu malingaliro anu, kumbukirani, izo ziri kujambulidwa pakali pano mu Ulemerero, ndipo rekodiyo idzaseweredwa pa Tsiku la Chiweruzo. Kulingalira kwanu kuli kuti? O, momwe inu muti mudzafunire izo zitasinthidwa, pa Tsiku limenelo.

365 Ine ndikuti ndingodikira, chifukwa alipo ambiri, mbiri, kuzungulira pa guwa tsopano. Mwaona? Mwina mmodzi wa iwo, ngati ine nditangozigwira motalikitsa pang’ono, kwina kwake akhoza kukhalapo mmodzi wina kunja uko, akhoza kukhala kwina kwake mu New York, uyo akhoza kukhala kwina kwake mu Philadelphia, uko mu California, Arizona. Kwina kwake, uko akhoza kukhalapo mmodzi wina akubwera. M’busa, kulikonse komwe inu muli, musati musiyitse kuitanira pa guwaku tsopano.

366 Ife mwina sitikhoza kudzawona kupereka Mathokozo kwina. Uku kukhoza kukhala kotsiriza kwake, ndipo zolembidwa ziiqidwa pamwamba, usikuuno, kwa nthawi yotsiriza. Tepi itha, limodzi la masiku awa. Rekodiyo idzadulidwa ndipo idzakakhala mu chimbale cha Mulungu. Ndiye iyo idzakaseweredwa mobwereza, chomwe maganizo anu ali tsopano. Musati muti inu simunkadziwa kusiyana kwina. Inu muli. “Koma palibe munthu yemwe angakhoze kudza kwa Ine, kupatula Atate Anga atamukoka iye. Ndipo onse omwe Atate andipatsa Ine, iwo adzadza.”

. . . kudza kwa Iye?

367 Ine ndikukhulupirira, ngati ine ndikanati ndikhale ndiri kunja uko kwina kwake, ndipo ine nkukhala nalo ganizo laling’ono ng’ono, ine ndithudi ndikanauyamba wa pano molimba momwe ine ndikanathera.

Ulekeranji? Bwanji?

368 Kodi inu mwatha? Mukutsimikiza kuti inu simukuukwiyitsa Mzimu Wake tsopano? Tiyeni tisunge mitu yathu chiweramitsire ndiye. Inu mukutsimikiza kuti inu simunaukwiyitse Mzimu Wake? Inu mukutsimikiza kuti mwachita ndendende basi zomwe Iye anakuuzani inu kuti muchite? Inu movomereza tsopano? Kumbukirani, i—inu mwina simudzakhala nawo mwayi wina. Rekodiyo ikhoza kutha, usikuuno. Izi zikhoza

kukhala zonse zake. Iyi ikhoza kukhala tepi yotsiriza yanu. Kodi inu mukutsimikiza kuti inu mwakonzeka tsopano? Ngati ziri choncho, ine ndikuzisiyira izo mmanja mwanu, mu Dzina la Ambuye Yesu.

³⁶⁹ Tsopano pamene kwayala ikuimba mosafuula, ine ndikuti ndiwapempherere awa omwe ali pansi apa. Ine ndangokhala ngati Mkristu wa mtundu wosamvetsetseka kwambiri. Ine ndikukhulupirira kuti Mulungu ayenera kuchita zopulumutsazo. Ine ndikukhulupirira Mulungu ayenera kubzala Mawuwo. “Ine Ambuye,” limatero Baibulo, Yesaya, “Ine Ambuye ndawabzala iwo. Ine ndidzawatsirira iwo, usana ndi usiku, kuwopa kuti ena angawakhwathule iwo kuchokera mdzanja Langa.” Ine ndisanamupempha aliyense kuti abwere mozungulira guwa ndi anthu awa, ine ndikufuna kuti ndiwapempherere iwo, mwiniwanga.

Tiyeni tiweramitse mitu yathu tsopano.

³⁷⁰ Wokonededwa Yesu, ine ndimangobwereza Mawu Anu, omwe mneneri Wanu anawanena, ndipo ine ndikudziwa mawu a aneneri ndi owona. Ndipo inu munati, “Ine Ambuye ndawabzala iwo.” Bwanji, ndithudi, Inu munawaika iwo pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa, asanaikidwe maziko a dziko. “Ine Ambuye ndawabzala iwo, ndipo Ine ndidzawatsirira iwo, usana ndi usiku, kuwopa kuti ena angawakhwathule iwo kuchokera mdzanja Langa.” Awa, mwinamwake, Ambuye, amva kuitanira pa guwa kochuluka. Koma Inu mukadali kuwatsirirabe Iwo, Ambuye.

³⁷¹ Pano iwo ali, usikuuno. Aloleni iwo angomasuka, usikuuno, Atate, kuchoka ku zinthu zonse za mdziko, machimo onse ndi mavuto omwe ali mu mtima mwawo, ndipo basi mwaubwino, molemekeza, mu mtima mwawo, amasukire ku Mawu Anu, pakali pano, nkuti, “Ambuye Yesu, pansi pa mtima wanga, ine nthawizonse ndimakhulupirira kuti panali chinachake cha kwa ine, chimene ine ndinali ndisanachilandire apabe. Ngakhale ine ndayesera, monga kalongosoledwe kapangidwira usikuuno, kutsatira nkuku, koma umo kunali chinachake chimawoneka chachilendo kwa ine. Icho sichinali kumveka bwino basi. Ndiye, usikuuno, ine ndikumverera kuti ine ndikubwera tsopano moyandikira mu mikono ya Mawu amoyo. Ine ndikubwera kuno molemekeza basi, mu malingaliro anga olondola. Ine ndakhazikika pansi apa pafupi ndi guwa ili. Ine ndikufuna chipulumutso, Ambuye, moyipa kwambiri. Ndine wanjala kwambiri! Ine ndikukufunani Inu, Ambuye, kuti mundigwire ine mmikono Mwanu, usikuuno. Osati kupyolera mu zotengeka zanga, koma kupyolera mu Mzimu wa chikondi, nditengereni ine mmikono Yanu, wokonededwa Mulungu.

³⁷² “Ndine mwana Wanu. Ine ndikumverera kuti ndine mphungu imeneyo yomwe iwo amaikambayo. Ndigwireni ine,

Ambuye. Ine ndikudumpha. Ine ndanyamuka kuchokera pa mpando wanga, ndi kudzagwada pansi pano. Ndigwireni ine, Ambuye. Ine ndikudumpha. Ndibweretseni ine pa mapiko Anu, Ambuye, kutali ndi zinthu izi za mdziko. Ndiloleni ine ndiwulukire kutali kuchoka ku nyansi za dziko lino, kuchoka ku chizolowezi changa choipa, kuchoka ku mwambo wanga wachipembedzo wonse. Ndiloleni ine ndibwere kwa Inu nokha, wokondedwa Mulungu, kuti Mzimu Wanu Woyera ukhoze kutsanulira mwa ine kukhululukira kwa zokaikira zanga zonse. Ndiloleni ine, usikuuno, ndikhale mwana Wanu, mwatsopano, wobadwa, ndi cholengedwa chatsopano, usikuuno. Ndigwireni ine. Nditengereni ine kutali, kupitirira kuluku wa nkuku. Ndinyamulireni ine kutali, ku chisa cha Mphungu, kumene uko ine ndingakhoze kumakadyetsedwa ndi Mawu a Mulungu, mpaka ine nditamakhoza kuuluka.”

³⁷³ Perekani izi, wokondedwa Mulungu. Atengeni iwo. Iwo ndi Anu. Ili ndi pemphero langa ndi kudzipereka, kuwapempherera pa anthu okufa. Perekani izi, Atate. Ine ndikupereka pemphero ili mmalo mwawo. Kwa ulemerero wa Mulungu, ine ndikupempha izi.

Tsopano ndi mitu yathu itaweramitsidwa.

³⁷⁴ Ine ndikudabwa, kuzungulira pa guwali tsopano, ndi inu omwe mwagwada pano. Ambiri a inu mumadzinenera kuti ndinu Akhristu, koma inu mwamverera kuti nthawizonse pali chinachake, kwinakwake, chomwe inu munalibe. Inu mukhoza kukhala kuti munachitapo machitidwe onse achipembedzo. Inu mukhoza kukhala kuti munafuula. Inu mukhoza kukhala kuti munachita zinthu zonse. Mukhoza kukhala kuti munavina mu Mzimu. Inu mukhoza kukhala kuti munayankhula mu malirime. Ndipo palibe munthu angakhoze kunena chirichonse cholakwika motsutsa izo. Izo nzoona. Izo zonse ndi zabwino. Koma, inu mukuona, izo ndi *mphatso* za Mzimu, zopanda Mzimu. Ngati Mzimu ukanakhala pamenepo, kumverera uko sikukanamati kuzitsutsidwa monga chomwecho.

³⁷⁵ Kodi inu muli kwenikweni, modzipereka, pano paguwa, mukukhulupirira izo pakali pano, pamene inu muli pano, kuti kuchita kokha kodzitembenuza nokha nkumasuka, osati motengeka tsopano, koma mwa chenicheni, chikhulupiriro chosapitsidwa, kuti Mulungu akulandirani inu ndipo akudyetsani inu ndi Mawu Ake mpaka inu mutakhala mphungu, inueni, ndipo mukhoza kumauluka? Ngati inu mukutero, ndipo inu mukufuna kuti Mulungu achite izo, kwezani dzanja lanu mmwamba, inu omwe muli kuzungulira guwali pano. Mulungu akudalitseni inu. Aliyense ali ndi dzanja lake mmwamba.

³⁷⁶ Tsopano, mwakachetechete kwenikweni, ine ndikuti ndiwapemphe amuna ndi akazi odzipereka omwe akumudziwa kwenikweni Mulungu.

377 Ambiri a iwo, ndi zachilendo kwambiri, zikuwoneka ngati ziri mwanjira imeneyo, kuitanira paguwa komwe ine ndimakupanga kawirikawiri onse amakhala amuna. Inu mukudziwa, mwa kuchita kwachizolowezi, ndi akazi. Koma onse ndi amuna pano. Ine ndikuganiza pali mkazi mmodzi pa guwali, usikuuno, mwinamwake awiri. Izo kawirikawiri amakhala akazi. Koma, mwanjira ina kapena imzake, ine ndikulingalira izo zikuwoneka ngati akazi amaganiza kuti ine ndimanena mowasutsa iwo. Ine sinditero, mlongo. Atatu, ine ndikukhulupirira, winawake anati iwo akuwaona. Ine sindikukhoza kuwona pamwamba pa guwa pano. Chabwino.

378 Ena a inu Akhristu odzipereka bwerani kuno ndi kudzaima ndi ine mu pemphero miniti yokha. Pa guwa, paliponse pomwe inu muli, pa nsanja, winawake yemwe amamudziwa kwenikweni Mulungu, kungodziwa kuima pano maminiti pang'ono okha a pemphero ndi iwo, ndiye ife tiwabalalitsa omvetsera. Aliyense akhale molemekeza kwenikweni tsopano. Musati muchoke. Ingobwerani pano ndi kudzaima pozungulira.

379 Ena a inu anthu omwe mukukhulupirira kwenikweni Ichi kuti ndi Choonadi, kuti ife tikulowa mu m'badwo wina. Ife tikulowa mu M'badwo wa Mkwatulo. Inu mukudziwa mpingo sungakhoze kupita mu chikhalidwe chakechi, ndipo iwo sungakhoze kukhala bwino mulimonse. Iwo uyenera kumka moipira. Ndi angati akudziwa izo? Itini, "Ameni." [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.] Izo ziyenera kumka ziipira. Ndipo izo sizingakhoze kumapita monga chonchi. Mwaona? Chiyenera kukhala chiri Chinachake, ndipo Icho chikusuntha pakali pano, mzanga. I—i—izo zayambika, kusunthako kwayambika kwa Mkwatibwi. Ndi Choonadi. Izi ndi PAKUTI ATERO AMBUYE.

380 Sunthirani mmwamba tsopano, Akhristu odzipereka omwe mukufuna yanu—rekodi yanu idzakapeze ili, awa omwe akubwera modzipereka, omwe inu mukufuna kuti mubwere ndi kudzapereka pemphero ndi iwo, ngati abale anu ndi alongo, bwerani kuno mozungulira guwali. Imani mozungulira pano mphindi yokha, kwa pemphero. Winawakenso akufuna kuti abwere, adzaimo mozungulira pano? Ingogwadani pansi pafupi ndi iwo. Ingoyendani, kumene amuna inu mowazungulira amuna awo; akazi inu. Mokoma, modzichepetsa pempherani pemphero pa iwo.

Wokonedwa Mulungu, athandizeni . . . ? . . .

381 "Ine ndikupereka zonse. Ine ndikupereka chipembedzo changa. Ine ndikupereka chikwati changa choyamba. Ine ndikupereka mwamuna wanga woyamba. Ine ndikupereka chirichonse, Ambuye."

. . . -zonse

Zonse kwa Inu, Mpulumutsi,

Ndipereka zonse.
Ndipereka zonse,
Ndiper- . . .

382 Inu mukuperekeka lingaliro lanu lanulo? Kodi inu mungapereke malingaliro anu anuwo, ku Mawu a Mulungu?

Zonse kwa Inu, Mpulumutsi,
Ndipereka zonse.

Ndipereka zonse,
Ndipereka zonse.
Zonse kwa Inu, Mpulumutsi,
Ndipereka.

383 Onse omwe akukhulupirira tsopano, mwa omvetsera, imirirani. Tiyeni tiyiimbe iyi, palimodzi, tsopano.

Ndiper- . . .

Inu nonse mukupereka, konzekani kuti muimbe iyi tsopano?

Ine . . .
Kwa Inu, Mpulumutsi,
Ndipere- . . .

384 Tsopano, inu kuzungulira guwali, ngati inu mukudzipereka kwenikweni, kwezani mmwamba dzanja lanu kwa Iye, nkumaimba, “Ine ndikupereka zonse. Ine ndikupereka chipembedzo. Ine ndikupereka chipembedzo. Ine ndikuupereka mpingo. Ine ndikudzipereka ndekha. Ine ndikupereka lingaliro langa. Zonse kwa Inu, Mpulumutsi wanga wodala, ine ndikupereka zonse. Kwa Inu, wanga . . .”

Ndipereka zonse,
Ndipereka zonse.
Zonse kwa Inu, Mpulumutsi,
Ndipereka zonse.

Kodi inu mukutanthauzadi izo?

Ndipereka zonse,
[Maló osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]

385 Inu pano tsopano pa guwa. Inu pano omwe muli mozungulira guwali, omwe mumapemphera. Mpingo wakupemphererani inu. Inu munadzipempherera, nokha. Tsopano pali njira imodzi yokha yomwe inu mungakhoze kupulumutsidwa nayo, ndiyo, “Mwa chikhulupiriro inu mumapulumsidwa, ndipo izo mwa chisomo.” Chisomo cha Mulungu chayankhula kwa inu, chakubweretsani inu ku guwa. Inu mukufunafuna madalitso a Mulungu. Inu mukufunafuna Mawu Ake. Inu mukufunafuna Mzimu Woyera. Inu mukufunafuna zifundo za Mulungu. Ndipo ngati inu muli, ndipo inu mukhoza, kwenikweni, ndi mtima wanu wonse, perekani izo. Tsopano, musati mufunefune zotengeka zirizonse. Funafunani Choonadi, Choonadi chomwe chiri chochokera mu mtima wanu, mwa

chikhulupiriro. “Ambuye, ine ndikulolera kuti ndichite chirichonse chomwe Mawu Anu akundilamulira ine kuti ndichite. Ine ndikudzipereka ndekha, ndi zonse zomwe ziri mwa ine.”

³⁸⁶ Ngati inu mukukhulupirira izo ndi mtima wanu wonse, ine ndikufuna inu kuti muimirire pa mapazi anu, mutembenukire kwa mpingo uwu, omvetsera, ndi kukwezera mmwamba manja anu, ndipo ife tiziyimba iyo limodzi ndi iwo, “Ine ndikupereka chirichonse chomwe chiri mwa ine, Mulungu. Mwa kupambana kwa kudziwa kwanga, chirichonse chomwe ine ndiri, ine ndikuchipereka.”

³⁸⁷ Dzaponjeni pamwamba pa nsanja iyi pano, inu omwe muli pa guwa. Dzaponjeni pamwamba pomwe apa pa nsanjayi, abale, apa pomwe, nonse inu, ndi abale ndi alongo.

Tayang’anani kuno, mpingo.

³⁸⁸ [Mlongo ati, “M’bale Branham, ndine wa mpingo, koma posachedwapa ine sindiri—sindiri nkomwe mwa iwo panonso.”—Mkonzi.] Ndikupereka? [“Ambuye akudziwa momwe ine ndikufuna kuti nditsogozedwere ndi Iye. Ine ndikufuna...?...kwa mpingo. Ndipo ine ndikufuna Mzimu Woyera, ndidzazidwe ndi Mzimu. Ndipo ine posachedwapa ndifa, ngati izo ndi zomwe zikutengera.”] Inde. Ndiko kulondola. Kodi inu mukupereka gawo lililonse kwa Iye ndi Mawu Ake?

³⁸⁹ Mlongoyu pano, kuchokera ku chipembedzo. Iye anati, “Ndine wa mchipembedzo.” Ife sitikusowa kuti tichite kuwutchula iwo. Iye ndi wogwira ntchito kumeneko. Koma iye anati, “M’bale Branham, ine ndikufuna kuti ndifike ku Choonadi. Ine ndikufuna chinachake choti ndizidya kuposa zimenezo.” Mwaona?

³⁹⁰ Mundilole ine ndibwereze Mawu Ake. “Odala ali iwo omwe achita njala ndi ludzu lofuna chilungamo, pakuti iwo adzakhutitsidwa.”

³⁹¹ Tsopano, inu muli pano pa nsanja, omwe mwangobwera, ngati inu mwakonzeka kuti mupereke chirichonse chomwe inu muli, chirichonse, kuti muzimvera Mawu a Mulungu. Palibe yemwe wakuuzani inu, sabata ino, choti muchite. Tsopano, ngati inu mwakonzeka kuti mudzipereke pakali pano kwa Iye, ingokwezani mmwamba manja anu, monga *chonchi*, kwa omvetsera. Tsopano, inu muli aponu pa nsanja, tiyeni tiyimbe iyo limodzi tsopano, *Ndipereka Zonse*. Aliyense, palimodzi. Chabwino.

Ndipereka zonse,

Tsopano muzitanthauza kwenikweni izo!...?...

³⁹² Kodi inu mukutanthauza kwenikweni izo? Nenani, “Ameni.” [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Munene, “Ameni,” kamodzinsu. [“Ameni.”] Itini, “Ambuye,” [“Ambuye,”]

“ndifufuzeni ine.” [“ndifufuzeni ine.”] “Ndiyeseni ine.” [“Ndiyeseni ine.”] “Ndipo ndipatseni ine mwayi.” [“Ndipo ndipatseni ine mwayi.”] “Izi ndi zonse zomwe ine ndingakhoze kuzichita, usikuuno,” [“Izi ndi zonse zomwe ine ndingakhoze kuzichita, usikuuno,”] “ndi kudzipereka ndekha kwa Inu.” [“ndi kudzipereka ndekha kwa Inu.”] “Inu mukudziwa njala ya mu mtima wanga.” [“Inu mukudziwa njala ya mu mtima wanga.”] “Inu mukudziwa chokhumba changa.” [Inu mukudziwa chokhumba changa.”] “Lonjezo Lanu linali kuti mudzakhutitse chikhumbo chimenecho.” [“Lonjezo Lanu linali kuti mudzakhutitse chikhumbo chimenecho.”] “Tsopano ine ndikuzilandira izo.” [“Tsopano ine ndikuzilandira izo.”] “Ndipo ine ndikudzipereka kwa Inu.” [“Ndipo ine ndikudzipereka kwa Inu.”] Tonse palimodzi.

Ndipereka zonse,
 Ndipereka zonse.
 Zonse kwa Inu, Mpulumutsi,
 Ndipereka zonse.



CHILUMIKIZO CHOSAWONEKA CHA MKWATIBWI WA KHRISTU CHA65-1125
(The Invisible Union Of The Bride Of Christ)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham woperekedwa mu Chingerezi Lachitatu usiku, Novembala 25, 1965, ku Life Tabernacle mu Shreveport, Louisiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira uku kwa Chichewa kunadindidwa m'chaka cha 2004 ndi Voice of God Recordings:

CHICHEWA

©2003 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org